

CHISINDIKIZO CHACHISANU



Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano kwa pemphero.

² Atate Mulungu Wachisomo, Mulungu Wamphamvuzonse, Yemwe anabweretsa kachiwiri Yesu Khristu kuchokera kwa akufa, ndipo mwamupereka Iye kwa ife mu masiku ano otsiriza, mu Mphamvu ya Mzimu Woyera, ife tiri oyamikira chifukwa cha kutichezera kwakukulu uku kwa Mulungu wa chisavundi. Ndipo tsopano, Atate, ife tikuyang'ana ora lina, ora limene likhoza kusintha kopita Kwamuyaya kwa anthu ambiri.

³ Ndipo kuti tiyandikire ichi, Ambuye, ife tiri osakwanira. Chifukwa, izo ziri mu Malemba, kuti, “Mwanawankhosa anatenga Bukhu ndi kutsegula Zisindikizo.”

⁴ O Mwanawankhosa wa Mulungu, bwerani patsogolo, ife tikupemphera. Ife tikuyitanira pa Inu, Ambuye, Wowombola wamkulu. Bwerani patsogolo ndi kutiwonetsa ife dongosolo Lanu la chiwombolo limene lakhala lobisika kupyola mu zaka, kumatula Chisindikizo Chachisanu ichi kwa ife usiku uno, Atate, ndi kuwulula zomwe ziri pansi pa Chisindikizo chimenecho kwa ife; kuti ife tikakhoze kuchoka Akhristu abwino kuposa momwe ife tiliri tsopano; tikakhale okwanira ku ntchito imene yagona patsogolo. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

Khalani pansi.

⁵ Usiku wabwino, abwenzi. Ine ndikuwutenga uwu mwayi wopambana kukhala pano usiku uno, pa chochitika ichi chachikulu. Ine sindikudziwa kwina kumene ine ndikanakhoza kumverera bwino, kuposa kukhala pa ntchito ya Mfumu. Ndipo tsopano kubwera makamaka pa maphunziro awa pamene ife tikungoyembekezera; ngati Iye sakanawulula Izo kwa ine, ine sindikanakhoza kupereka Izo kwa inu. Ine sindikuyesa kugwiritsa ntchito lililonse la maganizo anga omwe kapena chirichonse; chabe monga Iye ati andipatsire Izo. Uko nkulondola. Ndipo ine—ine ndiri kutsimikiza, ngati ine sindigwiritsa ntchito maganizo angaanga, ndipo Icho nkumabwera mwa njira yomwe Izo zachitira. Ndipo monse kupyola mu moyo Izo sizinalakwikepo. Izo sizilakwika nthawi yino.

⁶ Tsopano, ife tiri chabe mwaulemerero ndiponso kwambiri, othokoza kwambiri pa zomwe Iye watichitira ife, dzanja lalikulu lachinsinsi la Mulungu wamoyo! Chingakhale chinthu chopambana bwanji, ife tingakhale anthu amwayi wochuluka chotani, kuposa kukhala naye mu kukhalapo kwathu Mfumu ya mafumu, Mbuye wa ambuye?

7 Ife mwina tikanaliza malikhweru ndi—ndi kukweza mbendera, ndi kuyala makarapeti ndi chirichose, kwa Purezidenti wa fuko kuti abwere ku mzinda. Koma, tangoganizani, izo zikanakhala zabwino, ndipo icho chikanakhala chaulemu kwa mzinda.

8 Koma ganizani. Mu kachisi wathu wamng'ono, wonyozeka, usiku uno, ife tikumuyitana Mfumu ya mafumu, Mulungu. Ndipo ife sitiri. . . Iye sakukhumba makarapeti kuti ayalidwepo, ndi zina zotero. Iye amafuna mitima yodzichepetsa kuti iyalidwepo, kotero kuti Iye akakhoze kutenga mitima yodzichepetsa iyi ndi kuwulula kwa iwo z—zinthu zabwino zomwe Iye wasungira iwo onse amene amukonda Iye.

9 Tsopano, ife tinafunsa. . . Ndipo ine ndiri nawo umboni umene ine ndikufuna ku—kuwupereka. Tsopano, ngati ine ndikulakwitsa pa izi; ine ndinangomva izo, ndipo ine ndikhoza kukhala kuti ndikulakwitsa. Koma ine ndikuganiza kuti anthu ali pano, ndi amene umboniwo ukuwakhudza.

10 Ndiyeno, masiku angapo apitawo, pamene ine ndinali kupita kwathu tsopano, mu—mu Arizona, ife tinalandira ku—kuyitana kumene anati panali mnyamata wamng'ono amene anali ndi nyamakazi. Ndipo iyo imapita ku mtima. Ndipo iye anali chotero. . . Abambo ake ndi amayi ali okonedwa chotero, amzanga okoma a ine. Anali mmodzi wa madikoni athu pano, wa mpingo, M'bale Collins. Mnyamata wawo wamng'ono, Mikey wamng'ono, wosewera naye wa Joe, anali kuvutika ndi nyamakazi ya mtima. Ndipo madokotala anali atamutumiza iye kwawo, kumuyika iye pa bedi, ndi kuwawuza makolo kuti asamulore iye ngakhale kudzuka, kapena kudzutsa mutu wake, kumwa madzi. Kutizimwera iwo mu kapaipi; iye anali moyipa kwambiri. Ndipo makolo, okhulupirika, amabwera ku kachisi kuno, ndipo amakhulupirira.

11 Ndipo usiku ungapo wapitawo, posafuna kuyesa kuyembekezera, ife tinalengeza msonkhano wamachiritso pa Lamlungu. Koma, powona kuti ife timayenera kuyankha mafunso, kotero ndiye ife tinayenera kuchotsapo msonkhano wa machiritso.

12 Ndiyeno ine ndinali nako kenakake kakang'ono kamene ine ndakhala ndikukasunga mkati mwanga, mu mtima mwanga.

13 Ndipo mayi ndi bambo ankafuna kudziwa ngati iwo angakhoze kumubweretsa mwanayo m—mchipinda. Ndipo iwo anamubweretsa mwana wamng'onoyo kumeneko, ndipo Mzimu Woyera unamuwuzi iye kuti wachiritsidwa.

14 Ndipo kotero, makolo, pokhala olemekiza izo, anamutengera mwanayo kwawo ndi kumutumiza iye ku sukulu, kumutumiza basi iye ku sukulu.

15 Adokotala anamugwira iye, kotero dokotala sanali wokondweretsedwa bwino bwino nacho chinthu choterocho.

Kotero, iye anawawuza amayiwo kuti mwanayo ayenera kukhala mu bedi, zedi. Ndipo mayiyo anawawuza iwo nkhaniyo. Ndipo ine ndikuganiza munthuyo ali, ine ndikumva, ali Mkhristu wokhulupirira, mwa chipembedzo. Wa—Seventh-day Adventist, dokotalayo ali. Ndipo kotero iye anati, “Chabwino, inu muyenera . . . ili nthawi yoti mwanayo, kuti ine ndimuyeze iye.” Anati, “Inu muyenera kutero, bolani, akhale atayesedwa.”

Iye anati, “Zabwino kwambiri.”

¹⁶ Anamutengera mwanayo uko, ndipo dokotala anamuyesa iye, mu magari, kumene nyamakazi inagona. Ndipo kotero ine ndikumva kuti dokotala anali wodabwitsidwa kwambiri iye sanadziwe choti achite. Mwana wamng’ono ali bwino mwangwiro, momveka ndi mwabwino, osati . . . ? . . . anapezeka.

¹⁷ Tsopano, kodi alipo a Collins pano? Ine mwina ndalankhula izo molakwitsa. Ine ndikufuna . . . Kodi nkulondola uko, Mlongo Collins? Eya. Chabwino. Eya. Ameneyo ndi Mikey Collins wamng’ono, chabe pafupi zisanu ndi chimodzi, zaka zisanu ndi ziwiri zakubadwa.

¹⁸ Ndipo zimenezo zinachitika mu chipinda momwe, pafupi mausiku atatu apitawo. O, iwo . . . Muyenera kuti munali Winawake mu chipinda chimenecho pambali pa munthu chabe! Anali y—Yehova wamkulu ndi wamphamvu, uko nkulondola, yemwe amabwera kudzalemekeza Mawu Ake. Ndipo ine—ine ndiri woyamikira kumva zimenezo. Mukuwona? Ine ndikudziwa ife tonse tiri. Osati ine ndekha, koma onse ali, chifukwa bwanji ngati ameneyo anali—anali mnyamata wanu wamng’ono kapena mnyamata wanga wamng’ono?

¹⁹ Ndipo, kumbukirani, ine ndikupereka umboni, monga ngati umodzi chabe, ndi kutenga umodzi apa ndi apo. Izo zikuchitika kulikonse, koma kukudziwisani chabe inu kuti—kuti utumiki wanga weniweni uli pa machiritso Auzimu. Koma inu . . . ine ndiri pano chifukwa cha Zisindikizo izi. Chifukwa, kanthawi kena, inu mudzamvetsa chifukwa chimene ine ndimayenera kuchita izi. Ndipo, kotero, ine sindine mphunzitsi, ine sindine wazaumulungu. Ine—ine ndimangopempherera odwala, ndipo ine ndimawakonda Ambuye. Ndipo tsopano, tsopano mu izi, ngakhale, kuti . . .

²⁰ Usiku watha ife tinapereka umboni wa msungwana wamng’ono . . . Ine ndiri nalo dzina lake. Ndipo Billy ali nalo ilo apa tsopano, penapake, la makholo ndi amene iwo ali. Ndipo msungwana wamng’ono uyu anali mu siteji yotsiriza ya leukemia, pafupi basi . . . Moyipa kwambiri basi mwakuti iwo samakhoza kumudyetsa iye ndi kamwa iyi nkomwe; iye amayenera kukhala . . . magari ake kulowesedwera kupyolera mmitsempha. Ndipo iye anali kanthu kokongola kakang’ono. Iye anali wamng’ono kwa usinkhu wake, pafupi monga dona wamng’ono uyu apa, ine ndikuganiza. Koma iye anali pafupi

kutalika *chonchi*, kwambiri . . . Iwo anali monga ambiri a ife. Inu mukanakhoza kuzindikira ndi kavalidwe ka mwana, kuti . . . ndi makolo, kuti iwo anali osawuka kwambiri, basi osawuka kwambiri, ndipo, kotero, koma aulemu kwenikweni. Ndipo Mzimu Woyera unalengeza kuti mwanayo wachiritsidwa.

²¹ Tsopano, taganizani chabe za izo, ndi leukemia, mwana wamng'ono uja. Ndipo magazi anali oyipa kwambiri mwakuti iwo samakhoza ngakhale kumudyetsa iye kupyolera pa kamwa nkomwe. Izo zinachita kutengera, kupita ku chipatala ndi kukatenga magazi, kapena kulowetsa kupyolera mmitsempha, kumudyetsa iye; ine ndikuganiza, gulukosi, kapena chirichonse. Ine sindikudziwa dzina la zamankhwala lomwe liri kwa matenda amenewo, koma, ngakhalebe, iye ankayenera kumadyetsedwa mwanjira imeneyo. Ndipo mwanayo asanachoke pamalopo, analirira chitumbuwa.

²² Ndipo makolo, atatha iwo kumva Mzimu Woyera, wa PAKUTI ATERO AMBUYE, onani, iwo . . . Ndipo, iwo, achirendo, sanakhalepo pafupi kale. Koma iwo . . . A—okoma awiri achikulire amene apeza kumene mipando yawo apa kwa iwo, maminiti pang'ono apitawo, M'bale ndi Mlongo Kidd, anali atawalangiza iwo choti achite, ndi chakuti amvere. Ndipo mwanayo amadya chakudya chake panjira ya kwawo.

²³ Masiku awiri kapena atatu zitachitika izo, mu sukulu. Ndipo anakapita kwa dokotala, ndipo dokotala anali wodabwa kwambiri! Iye anati, “Palibe ngakhale chisonyezo chimodzi cha leukemia chapezeka mwa mwanayo.” Mukuwona? Tsopano, ndicho cha pomwepo, pa malo omwewo, Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse, kutenga mtsempha wamagazi ndi kuwutsuka iwo, kumene monga choncho, ndi—ndi kuyika kugunda kwa—kwa moyo watsopano kuwubwezera mmenemo. Chifukwa wanu—mtsempha wamagazi wanu uli moyo wanu, wachivundi. Ndi kulenga makhungu atsopano, ndi kutsuka onse akale! Ndipo—ndipo chimene icho chiri, icho chiri mwamtheradi . . . ine ndikanakhoza kunena ichi, iwo uli wa kulenga kwa Mulungu Wamphamvuzonse; kutenga m—mtsempha wamagazi umene wayipitsidwa ndi khansara, mpaka mwana wamng'onoyo, wachikasu ndi wotupa, ndipo, mkati chabe mwa mphindi za pang'ono, mtsempha wamagazi watsopano!

²⁴ Ine ndikukhulupirira . . . ine sindilankhula izo mu Dzina Lake; ine ndilankhula izo mu langa . . . mu vumbulutso la chikhulupiriro changa, chimene chinachitika mu Sabino Canyon tsiku lina. Ine ndikukhulupirira kuti ora likuyandikira, pamene miyendo yosowa idzabwezeretsedwe, ndipo Mphamvu ya ulemerero ya Mlengi. Ine—ine ndikukhulupirira, ngati Iye angapange gologolo kuwoneka, amene alibe . . . Apa pali mwamuna kapena mkazi, ali nalo kokha gawo losowa. Ndipo

ndiyo chinyama chathunthu, mwa icho chokha. Iye ali Mulungu. Ine—ine ndimamukonda Iye.

²⁵ Chabwino, tsopano, ine ndikayamba pa maphunziro amenewo, ndipo ife timangolankhula mopitirira. Ndipo anthu azungulira makoma, ndipo ayimirira mu maholo ndi zipinda, ndi zina zotero, kotero ine ndifika molunjika kumene ku Uthenga.

²⁶ Ndipo ine ndikufuna kunena ichi, ndipo ine ndikufuna kupereka kuthokoza kwa Iye Yemwe ali wopezekapaliponse. Ndipo, kuti, lero, wosadziwa kanthu kamodzi za Chisindikizo Chachisanu icho, Icho chinabwera mwa njira yomweyo yachinsinsi, mmawa uno, pafupi ora lokha kusanache, pamene ine ndinali kunja mu pemphero. Ndipo lero . . .

²⁷ Ine ndangokhala masiku asanu apita awa kapena asanu ndi limodzi, basi mu kanyumba kakang’ono, osawona mmodzi aliyense. Kumangotuluka ndi kukadya zakudya zanga ndi—ndi mzanga, ndi ena a amzanga apa. Ndipo, zedi, inu mukumudziwa yemwe mzanga ameneyo ali, ali M’bale ndi Mlongo Wood. Eya. Ndipo—ndipo inu mukudziwa, ndipo ine ndinapita kumeneko ndi—ndi kukakhala nawo iwo, ndipo aliyense wakhala ali wabwino. Ndipo sipanakhale chirichonse, mophweka chabe . . .

²⁸ Ine ndikuyesa kukhala nawo Uthenga umenewo wa Zisindikizo izi. Ndi wofunikira. Ine ndikukhulupirira ndilo—ndilo ora la nthawi Yake yowulula, ya vumbulutso la Izo.

²⁹ Ndipo tsopano ine ndikufuna inu mukhale otsimikiza tsopano, moyambirira, tisanati, mofulumira momwe inu mungathere, mulembe kumvetsa kwanu kosadziwika kwa—kwa Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri izi, ngati inu muli nazo izo, ndi kuziyika izo pa desiki. Ndipo mwina M’bale Neville kapena winawake akhoza kuyika bokosi pamwamba apa. [Wina akuti, “Apa pali bokosi.”—Mkonzi.] O, apa—apa, ine ndikuwawona iwo tsopano. Izo nzabwino. Kulibwino ine ndikhale nawo iwo usiku uno, kuti ine ndikhoza mwina kuwerenga pa iwo kanthawi, a Lamlungu mmawa. Tsopano, musati, nthawi yino, panthawi ino kumene, musati mpange mapempho a, kuti, “Kodi *uwu* uli umboni wa Mzimu Woyera?” Mukuwona? Ine—ine ndikanafuna kudziwa za, zimene ine ndaphunzitsa, inu mukuwona, kotero ife tikhoza kutenga phunziro limodzi ili (monga mibadwo ya mpingo) molunjika, mwawona, chifukwa ndilo limene ife tikuchita nalo tsopano.

³⁰ Tsopano, monga ife timati tipempherere odwala, ndiye izo zimatenga mwinamwake p—pemphero losiyana. Ndipo iwe utadzedwa, kulowa mkati kuti uchite chinthu chosiyana, inu mukudziwa. Ndipo iwe ukufunafuna Mulungu, kuti upeze, “Kodi kukakhala wina mmenemo usiku uno, Ambuye?”

³¹ “Inde, akakhala winawake atavala diresi ya chikasu, atakhala mu ngodya ya dzanja lamanja. Ndipo pamene iwe ukamuyitana iye, ukamutche iye *ichi*. Ndi kunena *chakuti* ndi

chakuti iye anachichita. Ndipo iye ali ndi *chakuti-ndi-chakuti*.” Ndiye iwe umapita kumeneko ndi kukayang’ana, ndipo apo iye ali. Mukuwona? Ndi zimenezotu, mwawona. Ndi zosiyana. Mukuwona?

³² Ndipo mwanjira iyi, ine ndikupemphera, “Ambuye Yesu, ndi chiyani kumasulira kwa Ichi? Wululani Icho kwa ine.” Amen.

³³ Tsopano tiyeni titenge athu—Malupanga athu titulutse kanonso tsopano, ndipo, Mawu.

³⁴ Ndipo ine ndikuyamikira thandizo lauzimu la M’bale Neville, limodzi ndi chikondi chaubale chake, kumbuko kuno kuseri kwanga, kundipempherera ine. Ndi anu onse kunjako, nawonso. Ndipo, tsopano, usiku uno pokhala usiku wa Lachisanu, ife tiyesa, kungolipanga ilo ngati. . . ife. . .

³⁵ Iwe sungakhoze motheka kugunda zinthu zonse. Iwe. . . Chifukwa, iwe ukhoza kutenga Icho, chimodzi chokha cha Zisindikizo zimenezo, ndi kukhalapo, basi—kungochibweretsa Icho kupyola kumene mu Lemba, mpaka mmusi. Mukuwona? Icho chikanakhoza kutenga miyezi ndi miyezi ndi miyezi, ndipo iwe sukanakhala nachobe Icho, chifukwa c—Chisindikizo Pachokha chikumangiriza Lemba lonse, kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso, Chisindikizo chimodzi cha Izo.

³⁶ Kotero chimene ine ndikuyesa kuchita, chiri, kulewa kuchoka kupita kutali kwa Icho, ine ndikulemba Lemba, kapena—kapena kamfundo kakang’ono apa penapake, ndi kulewa kwa. . . Kumangopitirirabe pa chinthu chimodzi icho, ine ndiyenera kumayang’ana mmbuyo, chifukwa, ine kokha. . . Kulankhula, ine ndimalankhula mwa—mwa njira. . . Ine—ine ndikuyembekeza ndiko kudzoza koyenera. Ndiyeno pamene ine—pamene ine ndiyang’ana mmusi kuti ndiwone. . . Ndipo ine—ine ndimayamba kulankhula, ndipo ine ndimadzimverera ndekha ndikuchoka pa phunziro, ine ndichewuka pozungulira, nkuyang’ana mmbuyo mbali yina, kuti ndiyese kupeza Lemba lina, kuti ndifike pa chimenecho, inu mukuwona, kukhala ngati kuchiwalitsira icho pang’ono ku mbali imeneyo, mmalo moyesa kumapitirira nazo zimenezo.

³⁷ Ndipo kotero tsopano ife tiwerenga usiku uno, mwa chisomo cha Mulungu, mwa kuthandiza Kwake, c—Chisindikizo Chachisanu. Ndipo Ndi chimodzi chachifupi. Ndi chotalikirapo pang’ono kuposa china. Okwera pa kavalo anai, tsopano, anali ndime ziwiri kwa chirichonse, ndipo izi ziri ndime zitatu mu chimodzi ichi. Tsopano, Chisindikizo Chachisanu chikuyambira, mutu wa 6 wa Chivumbulutso, ndime ya 9.

³⁸ Ndipo, tsopano, ngati inu mukakhala kuti ndinu m—mlendo amene sanamve akavalo anai awa, chabwino, inu. . . Onani, nthawizina iwe—iwe umangobwerera mmbuyo ndi—ndi kukhala ngati kusomeka chinachake, ndipo, pamene iwe utero, iwe ukuyembekezera anthu kuti amvetse Izo. Kotero ngati

pali chinachake chaching'ono chimene inu simukuchimvetsa, chabwino, mungokhala ngati kupirira pang'ono. Kapena, mutenge tepi ndipo kukamvetsera kwa Izo, ndipo—ndipo ine ndikutsimikiza inu mudza—mudzalandira dalitso kuchokera kwa Izo. Ine ndalandira. Ine—ine ndikuyembekeza kuti inu—kuti inu mutero.

³⁹ Tsopano, aliyense wakonzeka, kuchokera ndime ya 9 tsopano mpaka ku ya 11, kapena kuphatikiza ya 11.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona pansu pa guwa miyoyo ya iwo amene anaphedwa chifukwa cha mavu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene iwo anali nawo:

Ndipo iwo analira ndi liwu lokweza, kunena, Mpaka liti, O Ambuye, woyera ndi wowona, muchite inu... kuweruza ndi kubwezera magazi athu pa iwo amene akukhala pa dziko lapansi?

Ndipo miinjira yoyera inapatsidwa kwa mmodzi aliyense wa iwo; ndipo kunanenedwa kwa iwo, kuti iwo abapumula apobe kwa k—kanthawi pang'ono, mpaka antchito amzawo nawonso... abale awo, amene ayenera kuphewedwa monga iwo anali, kuti zikwaniritsidwe.

⁴⁰ Tsopano, ichi chiri kani chachinsinsi. Ndipo tsopano chifukwa cha matepi, ndi amuna awubusa ndi aphunzitsi amene akhala ali pano, tsopano, ngati inu muli nako kuyang'ana kosiyana kwa Ichi; ine ndinatero, nanenso. Koma ine ndikungotenga Izo kuchokera ku kudzoza, kumene mwathunthu kunasintha kuyang'ana kwanga kwa Icho. Mukuwona?

⁴¹ Ndiyeno ine ndikupeza kuti, pamene inu mukuwona izi zikuwululidwa, Izo zikubwerera mmbuyo ndi kubweretsa mibadwo ya mpingo iyo ndi Malemba palimodzi kumene, ndi kuzimangiriza Izo. Mukuwona? Ndipo ndicho chifukwa chake ine ndikukhulupirira kuti Izo zikuchokera kwa Mulungu. Tsopano, ife tikuzindikira zimenezo.

⁴² Ndipo ine ndikuganiza kuti nthawi zina ife timadalira pa zomwe mphunzitsi wina wamkulu akanalankhula za Icho. Mukuwona? Ndipo ndizo—ndizo zabwino zonse. Ine sindikutsutsa mphunzitsiyo, osati mwanjira iliyonse. Ndipo ine sindikutsutsa aliyense. Ine ndikungotsutsa tchimo, kusakhulupirira; osati winawake.

⁴³ Ndipo anthu ena anenapo, “Inu mumatsutsa bungwe.” Ayi, ine sinditero. Ine—ine ndimatsutsa kachitidwe ka bungwe; osati anthu mmenemo, gulu la anthu limene limapanga bungwe, inu mukudziwa. Koma kachitidwe komwe iwo akulamulidwa nako, ndiko kamene ine ndimatsutsa, Chikatolika ndi Chiprotestanti, zofanana. Mai! Ine ndiri... .

44 Ena mwa amzanga abwino amene—amene—amene ine ndikuwadziwa, ali a Chikatolika, basi...?..Kodi inu mukuzindikira... Ndipo munthuyo mwina ali pano usiku uno, mwinamwake ali. Njira yokhayo imene ife tinamangira kachisi uyu, chifukwa wa Chiroma Katolika anayima pa mapazi ake mu khoti kumeneko, ndipo anapita patsogolo kwa ine, ndipo, mnyamata, monga palibe aliyense akanachita. Uko nkulondola. Ndipo iwo sakadachikana icho. Uko nkulondola.

Ndipo anati, “Iwo anatulutsa chiwerengerochi, ‘Anthu ochulka kwambiri.’”

45 Iye anati, “O, zimenezo sizipanga makumi asanu ndi atatu ena mu mpingo umenewo, monga choncho.” Anati, “Mpingo umenewo ukuyima pamenepo.” Anati, “Ine—ine ndikumudziwa m’busa, ndi zonse monga choncho.” Ndipo anati, “Mpingo umenewo wakhala uli pamenepo.” Anati, “Ena nonse inu mukhoza kuwonjezera kwa iwo, ndiye iwo sakhoza bwanji?” Wa Chiroma Katolika, mzanga wabwino wa ine. Mukuwona? Inde, bwana.

46 M—mnyamata amene ali m—Mkatolika, mzanga weniweni womvana ndi ine, anali kulankhula kwa ine. Anali nayo sitolo yinayake ya ziwiya; ine ndisanachoke. Iye anati, “Billy, ine—ine ndikudziwa iwe sumakhulupirira mu kachitidwe kathu ka chipembedzo.” Iye anati, “Koma ine ndikukuwuzwa iwe pakali pano,” anati, “Mulungu walemekeza mapemphero ako mochulukwa kwambiri kwa ife! Ine ndikukhulupirira, ngati iwe ukhala mu vuto kulikonse mu dziko,” anati, “Mkatolika aliyense mu dzikoli adzabwera kwa iwe.” Kotero, inu mukuwona, ndiko...

47 Iye anati, “Aliyense wa mtandapansana,” iye anachiticha icho. Ine ndinena izo basi momwe iye anachitira. Chifukwa, iwo amanena kuti ali icho chifukwa Akhristu oyambirira ankanyamula mitanda pa misana pawo. Ife timadziwa zimenezo mwa mbiriyakale. Ndipo iwo amanena kuti ali Akhristu oyambirira, chimene iwo anali, koma kachitidweko kawachotsa iwo pa njira imeneyo, inu mukuwona.

48 Ndipo anthu amenewo, Achikatolika, kapena Myuda, kapena chirichonse chimene chiri, iwo ali anthu ochokera pa mtengo womwewo umene ife tikuchokerako. Mukuwona? Uko nkulondola. Iwo ali—iwo ali anthu amene amakonda, ndi kudya, ndi kumwa, ndi kugona, ndi monga basi wina aliyense. Ndipo kotero ife tiyenera kusatsutsa anthu pawokha, ayi, osati mmodzi, mwawona. Koma, ife tisamawatsutse anthu pawokha.

49 Koma, monga mtumiki, ine ndiyenera kukantha serpenti imeneyo kunjako, imene ikuluma mwa anthu amenewo, inu mukuwona. Ndipo ine sinditi—ndipo ine sinditi ngakhale... Ine basi, ndipo ine ndekha, ine sindikanamachita icho ngati sikunali kutuma kochokera kwa Mulungu, komwe ine ndiri

wokakamidzwa kuchita icho, mwawona. Ndipo ine ndiyenera kuchisunga icho mowona ndi mokhulupirika.

⁵⁰ Koma ngati Mkatolika, Myuda, kapena chirichonse chimene iye anali, abwera kuno; ngati iye anali wa Chimuhamadi, Mgriki, kapena Orthodox, kapena chirichonse chimene iye angakhale. Ngati iye abwera apa kuti adzapemphereredwe, ine ndikanadzakhoza kumupempherera basi modzipereka kwa iye monga ine ndikanachitira kwa wanga yemwe. Uko nkulondola. Ndithudi, chifukwa ndi munthu wokhalapo. Ndipo ine ndapempherera Achibudha, ndi Achisikh, Achijain, Achimuhamadi, ndi—ndi mtundu uliwonse, inu mukuwona, monga choncho. Ndipo ine sindimawafunsa iwo mafunso; ine ndimangowapempherera iwo, chifukwa iwo ali winawake, munthu wokhalapo amene akufuna kupeza bwino, ndi kuyesa kuwupanga moyo kukhala wophweka pang'ono motsatira njira kwa iwo.

⁵¹ Tsopano ife tikuzindikira, kuti, mu ichi, ndipo ambiri a inu apa ine ndikudziwa, apo pali pafupi awiri kapena masikolala enieni atatu akhala apa. Ndipo—ndipo iwo ndi anzeru, ndipo awerengapo kuchokera—kuchokera mu ziphunzitso za anthu ena pa phunziro ili. Ndipo ine ndikufuna abale awa adziwe kuti ine—ine sindikuwatsutsa anthu awa. Ine ndiri kufotokoza kokha chimene Ambuye akundiwonetsera ine. Ndipo ndizo zonse ine ndiri nazo.

⁵² Tsopano, ife sitikufuna konse kumaganiza kuti, chifukwa mkazi wina wochapa kapena—kapena mnyamata wamng'ono wolima kumeneko, sakanakhoza kupeza vumbulutso kuchokera kwa Mulungu. Chifukwa, inu mukuwona, izo... Mulungu, Iye makamaka amadziwulula Yekha mu kuphweka. Ndiko, ife tinali nazo izo Lamlungu, kuti tiyambirepo izi, momwe Iye amadziwululira Yekha mu kuphweka Kwake. Ndicho chimene chimamupanga Iye kukhala wamkulu.

⁵³ Tsopano lolani—ndiroleni ine chabe... Ndiroleni ine ndingobwerezanso izo kwa miniti yokha. Chimene chamamupangitsa Mulungu kukhala wamkulu, chiri chifukwa Iye akhoza kudzipangitsa Yekha mophweka chotero. Ndicho chimene chimamupanga Iye kukhala wamkulu. Mulungu ndi wamkulu, ndipo akhoza kudzipanga Yekha mwa mawonekedwe ophweka chotero mwakuti anzeru a dziko lino sangakhoze kumupeza Iye. Iwo basi sangakhoze kumupeza Iye, chifukwa Iye amadzipangitsa Yekha kukhala wophweka kwambiri. Tsopano yang'anani. Ndipo ichi, pa icho chokha, chiri chinsinsi cha vumbulutso la Yesu Khristu. Mwawona? Ichi, mwa icho chokha, kuti pa... Pali... sipangakhale kanthu kopambana kuposa Mulungu. Ndipo inu simungapange chirichonse kukhala chophweka monga momwe Iye amadzipangira Yekha. Mukuwona, ndicho chimene chimamupanga Iye kukhala wamkulu. Mukuwona?

⁵⁴ Tsopano, munthu wamkulu, iye akhoza kungokhala wamkulu pang'ono, kapena mwinamwake iye akhoza kudzitsitsa pansi ndi kunena, “Muli bwanji inu?” kwa iwe, mwawona, kapena chinachake chonga chimenecho. Koma iye sangadzipange yekha kukhala wamng'ono. Pali basi chinachake cha iye. Iye ndi munthu. Iye sangakhoze chabe kudzipanga yekha wamng'ono. Chifukwa, pamene iye afika potsika kukakhala wamng'ono kwambiri, ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iye ayenera kufanizira ku chimene winawake anachita, ndipo monga choncho. Ndiyeno iye amayamba kudzikokera yekha mmwamba kachiwiri, inu mukuwona.

Koma, njira yopitira kumwamba ndi pansi, mwa Mulungu. Inde.

⁵⁵ Anzeru a mdziko ali kuyesetsa, mu nzeru yawo, kuti amupeze Iye. Iwo amangokwera kutali ndi Iye, mu kuchita choncho. Mwawona, anzeru a mdziko, ngati iwe ukuyesera kufotokoza chinachake mwa masamu ena kapena chinachake. Kumbukirani, Iye wayika ngakhale izo... Mu Baibulo, mu Chivumb-... Ayi, ine ndikupempha kukhululuka kwanu.

⁵⁶ Yesaya 35, ine ndikukhulupirira iye ali, kuti ngakhale ziri choncho—ziri zophweka kwambiri mwakuti ngakhale m—m—munthu wamakhalidwe oyipa akhoza kumvetsa Izo, mukuwona. Chabwino, “Ngakhale chitsiru sichidzaphophonyetsa mmenemo.

⁵⁷ Anzeru amachiphonya icho kutali, mwa nzeru zawo, kupita kutali kuchoka kwa Iye, pakuyesa kumupeza Iye mwa nzeru. Tsopano, musati muyiwale izo. Izo zidzajambulidwa, mwawona. Anzeru, mu nzeru zawo, amapita kutali kwambiri kuyesa kumupeza Iye mwa nzeru zawo, iwo amamuphonya Iye, mwawona. Ngati iwo akanakhoza kukhala akulu mokwanira kuti akhale ophweka mokwanira, iwo akhoza kumupeza Iye. Ngati iwe uli wamkulu mokwanira kuti ukhale wophweka mokwanira! Mwawona izo? Ndipo, inu mukudziwa, kuti—izo ziri kwenikweni Chowonadi.

⁵⁸ Ine ndapitapo kwa anthu, mu maofesi awo, ndi zina zotero, amene anali kwenikweni anali amuna, akulu, mafumu, mwawona, ndi amphamvu, atsogoleri, ndipo kawiri kawiri iwo ali anthu aakulu. Ndiye, ine ndapita mmalo mmene munthu ali nazo zovala zosintha, mwinamwake mtumiki wina amene amafuna kutsutsana nane ine kanthawi, ndipo iwe—iwe ukhoza kuganiza kuti dziko silingakhoze kuyenda popanda iye, mwawona. Ndipo uyo—ndiko kungodzitukumula mmutu, mwawona. Koma, m—munthu wamkulu, munthu wamkulu amakhala pansi ndi kuyesera kukupanga iwe kuganiza kuti iwe ndiwe munthu wamkulu. Mukuwona? Mwawona, iye akhoza kudzichepetsa yekha.

59 Ndipo, inu mukuwona, Mulungu ali wamkulu kwambiri mpaka Iye akhoza kudzichepetsa Yekha, ku malo, amene munthu sangakhoze kutsika patali choncho, inu mukuwona. Ndizo zonse. Ndipo mkati mwawo . . .

60 Ndipo iwo akuyesa kumupeza Iye. Tsopano penyani. Iwo akuyesa kumupeza Iye pa kutumiza anyamata ku sukulu, ndi kukatenga digrii ya Bachelor of Art. Ndipo—ndipo iwo akuyesera kuyipeza Iyo mwa kufotokoza kwa zaumulungu kwa—kwa—kwa—kwa Baibulo. Ndipo iwo akuyesa kumupeza Iye mwa madongosolo a maphunziro, ndi mwa madongosolo a zabungwe, ndi mwa kukongoletsa zinthu, ndi kuyesera kupeza. Iye sali kumeneko, nkomwe. Inu mukungomenyana nayo mphepo, ndizo zonse. Inu muli—inukupita kutali kwa Icho.

61 Iwo akanakhoza kukhala akulu mokwanira kuti akhale—kuti akhale ophweka mokwanira, iwo akanakhoza kumupeza Iye ku mbali imeneyo, pa kukhala ophweka. Koma malingana ngati iwe ukupita molunjika ku nzeru, iwe ukupita kutali ndi Iye.

62 Tsopano ndiroleni ine nditenge izo kotero inu musaziphonye izo. Malingana ngati inu mukuyesa kumupeza Mulungu mwa nzeru, monga zinali mu munda wa Edeni, monga izo zinali mu masiku a Mose, monga izo zinali mu masiku a—a Nowa, monga izo zakhala ziri mu masiku a Khristu, mu masiku a Yohane, mu masiku a atumwi, ndipo mpaka ku tsiku lino! Pamene iwe uyesa kuchilingalira Icho, ndi kuyesa kumupeza Mulungu mwa nzeru, iwe ukupita kutali kuchoka kwa Iye nthawi zonse. Iwe ukuyesera kuchimvetsa Icho. Apo palibe njira yochitira izo. Ingochirandira Icho. Mukuwona? Ingokhulupirira Icho. Usati uyesere kuchimvetsa Icho.

63 Ine sindingakhoze kumvetsa chifukwa, chimene, chabwino, zinthu zambiri. Si zinthu zambiri zimene ine ndimazimvetsa kapena ndingakhoze kuzimvetsa. Ine sindingakhoze kumvetsa momwe mnyamata wamng'ono uyu wakhala apa amadya chakudya chomwecho chimene ine ndingakhoze, ndipo—ndipo, apa iye ali, ali nawo mutu wodzaza tsitsi, ine ndiribe lirilonse. Ine sindimvetsa zimenezo. Iwo amandiwuza ine kashiyamu amapanga ilo; ndipo ine sindingasunge zikhadabo zanga kuti ndidzawenge mokwanira, ndipo ndiribe tsitsi nkomwe kuti ndizilimeta. Ine—ine sindimvetsa zimenezo. Monga mwambi wakale uli, ine . . .

64 Osati kungokhala ngati kusintha malo, kutsimikiza; koma, Izo ziri zotsimikiza, koma ine sindinafiikebe ku Chisindikizo.

65 Momwe ng'ombe yakuda iyo ingakhoze kudya msipu wobiriwira, ndi kupereka mkaka woyera, womwe umapanga batala wa chikasu! Ine—ine ndithudi sindingakhoze kufotokoza zimenezo, mwawona. Chifukwa, inu mukuwona, chirichonse chiri chotuluka mwa chimodzi china. Ndipo momwe izo zimachitira, ine sindingakhoze kufotokoza zimenezo.

⁶⁶ Sindingakhoze kufotokoza momwe akakombo awiri, kapena maluwa awiri, a mtundu womwewo, ndipo lina lofiira, ndipo limodzi lina la chikasu, ndipo limodzi la bulawuni, ndi limodzi la buluwu. Ine sindimvetsa zimenezo. Duwa lomwelo pa iwo. Kodi mtunduwo umachokera kuti? Mukuwona? Ine—ine sindingakhoze kufotokoza zimenezo, komabe iwe uyenera kuvomereza zimenezo.

⁶⁷ Ine ndimangokhumba kuti wina wazaumulungu wamkulu afotokoze kwa ine momwe dziko ili limayimira mu mlengalenga. Ine ndikukhumba inu mukanakhoza mwasayansi kundiponyera ine mpira mu mlengalenga, ukuzungulira, ndi kuwusiya iwo kuti upange kuzungulira kwachiwiri, mu malo omwewo. Inu simungakhoze kuchita izo. Ndipo komabe ili liri mwangwiroyoyikidwa mwa nthawi mpaka iwo akhoza kudziwa kadansana wa dzuwa pa miniti, zaka makumi awiri kuchokera pano. Iwo alibe wotchi kapena koloko, kapena chidutswa chirichonse cha makina, zomwe ziri mwangwiroyochoncho. Ndipo komabe ilo likuyima pamenepo. Ndipo, ndiye, litatsamira chammbuyo. Bwanji ngati ilo litadziwongola pang'ono chabe? Eya. Iwe umangodzzipusitsa wekha, kuyesa, mwawona.

⁶⁸ Kotero, inu mukuwona, musati muyesere kutenga nzeru, kuti mumvetse. Ingokhulupirira zimene Iye anena. Ndipo kuphweka koposa kumene inu mungakufike, ndiye pamenepo inu muli, inu mudzachipeza Icho. Tsopano, ine ndiri wothokoza kwambiri chifukwa cha izo, wothokoza kwambiri kuti Iye ali, wadzipanga Yekha wophweka. Tsopano, ife tikupeza, mutu wa 6 ndi ndime ya 9. Ndiroleni ine ndiyambe tsopano.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona panso pa guwa miyoyo ya iwo amene anaphedwa chifukwa cha mavu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni. . . iwo anawugwira:

⁶⁹ Zindikirani, apo palibe kutchula kwa Chirombo china, kapena chamoyo—Cholengedwa chamoyo, ku kulengeza uku kwa Chisindikizo Chachisanu. Tsopano kumbukirani, chinalipo, pa Chisindikizo Chachinai. Chinalipo, pa Chisindikizo Choyamba, Chachiwiri, Chachitatu, ndi Chachinai, koma palibe apa. Mukuwona?

⁷⁰ Tsopano, ngati inu mungazindikire, tiyeni tingowerenga mmbuyo, chimodzi cha Zisindikizo. Tiyeni tibwerere ku Chisindikizo Chachinai, mwawona. Ndipo ndiyo ndime ya 7.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachinai, ine ndinamva liwu la chamoyo chachinai likunena, Bwera. . . udzawone.

. . . pamene iye. . . anatsegula chisindikizo chachitatu, ine ndinamva liwu la—la chamoyo chachitatu likuti, Bwera ndipo udzawone.

. . . la chamoyo chachiwiri. . . Bwera. . . udzawone.

. . . ndipo chamoyo choyamba kunena, *Bwera ndipo udzawone.*

71 Koma ndiye pamene ife tikufika ku Chisindikizo Chachisanu, apo palibe Chamoyo. Tsopano ingozindikirani.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona pansi paguwa. . .

72 Mwamsanga kumene! Onani, apo palibe—palibe Chamoyo pamenepo. Ndipo Chamoyo chimayimira mphamvu. Ife tikudziwa zimenezo, mwawona. Apo palibe Cholengedwa chamoyo.

73 Tsopano, chimodzi cha Zamoyo zimenezo, ife tikuzipeza, mu kuwerenga kwa—kwa—kwa vumbulutso mu mipingo, kuti chimodzi cha izo chinali nawo. . . chinali mkango; ndipo chimodzi china—chimodzi china chinali ng’ombe; ndipo chimodzi china chinali munthu; ndipo chimodzi china chinali mphungu. Ife tikupeza, mu mibadwo ya mpingo, kuti Zamoyo zinai izo, kutanthawuza mphamvu zinai, zinasonkhana mozungulira Machitidwe a Atumwi, basi momwe uja—kachisi mu chipululu. Ndipo inu mukumvetsa zimenezo, chifukwa ine sinditenga nthawi kulowa mu zimenezo. Momwe ife tinajambulira izo apa, ndipo tinawonetsa chimodzimidzi basi! Iwo anali kuyang’anira pa Izi, Mwanawankhosa ndi Mawu, kukachita Mawu basi momwe iwo ankachitira—likasa la pangano mu Malo Woyera mu chipululu, ndi zina zotero.

74 Tsopano, ife tinawonetsa ngakhale malo awo, mwa mitundu yamafuko ya Israeli, ndi mwa. . . Ndi angati anamva isanu ndi iwiri—mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo? Ine ndikuganiza ambiri ali nayo, awiri pa atatu a inu. Zindikirani, kuti ngakhale chikhaliidwe cha Chamoyo chinali chimodzimidzi mbendera yafuko, mbali iliyonse zinai. . . mafuko khumi ndi awiri ankakhala, zinai mbali iliyonse, kapena—kapena mafuko atatu ku mbali iliyonse. Ndipo Zamoyo zinai zinkakhala ndi kuyang’anira, mafuko awa, kuchokera ku mbali zonse zinai.

75 Ndipo, pamene, ife tinapita ndi kukatenga Mawuthenga, ndi kuwonetsa chimodzimidzi. Pamene inu mulowa mu likasa, iwo anali kulondera likasa, pangano. Ndiyeno ife tikupeza kuti pangano la Mpingo watsopano, choyimira Chake pa dziko lapansi, chinali Mzimu Woyera. Magazi anali atabwezera, kwa ife, Mzimu Woyera. Ndipo Zamoyo zinai zinkayimiridwa, ndipo monga—mafuko khumi ndi awiri a Israeli, pamene izo zinkayang’ana. Ndipo tikupeza zikhaliidwe zawo, ndi kutenga chikhaliidwe chomwecho ndi kuchibweretsa icho kwa chimodzi chirichonse cha Mawuthenga anai awo, chimodzimidzi, zinai zofanana chimodzimidzi. Chimodzi chinkalankhula kwa mkango, chimodzi china kwa ng’ombe, ndipo china. . . Mawuthenga anai! Apo izo ziri. Mawuthenga anai ali chitetezero cha Mzimu Woyera. Amen.

76 Ine basi nthawizonse ndimadabwa...Icho chinakanirira kwa ine. Tsopano, izi ziri pafupi zaka zisanu ndi chimodzi, ine ndikuganiza, kuyambira pamene ine ndinamva munthu wamkulu akuti awo anali...“Machitidwe a Atumwi anali miyanga chabe.” Ine ndamvapo izo zikulankhulidwa nthawi zambiri. Koma kumumva mwamuna wa udindo wake, monga mlaliki ndipo monga mphunzitsi, amene walembe ena a mabuku otchuka amene anthu amawerenga kulikonse, ndipo kunena kuti Machitidwe a Atumwi sanali kwenikweni ofunikira kuti aziphunzitsa kwa Mpingo!

77 Pamene, Machitidwe a Atumwi ali maziko kumene a Icho; osati miyanga. Maziko! Chifukwa, Baibulo limanena kuti m—m—m—maziko a Mulungu “amangidwa pa Chiphunzitsa cha atumwi,” kulondola “Khristu, Mutu, Mwala wapangodya.”

78 Ndipo pamene munthu uyu anayimirira pamenepo napanga ndemanga imeneyo, ine—ine—ine—ine basi...Mtima wanga unangolephera. Ndipo ine ndinaganiza, “Palibe chodabwitsa.” Chabwino, ine ndikuwona tsopano, mu Zisindikizo. Izo zinali basi zisanawululidwe. Ndizo zonse. Mukuwona?

79 Koteri, kuti, apo iwo anali, atayimirira pamenepo, koma panali chinachake chinali kungonena zimenezo. Tsopano, zindikirani, iwo amalondera.

80 Tsopano, pamene ife tapeza Mateyu 28:19, ndi kuchiyendetsa chinthu chimenecho mmusi kupyola mu Mateyu, amene ankayimira mkango. Ndipo kubwera, mkati umo, ife tinapeza chimodzimodzi chifukwa chomwe iwo amatizira mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo apo Iye anali, atayima pamenepo ndi Lemba lomwelo, kuti alondere mphamvu yopatulika ya ubatizo, wa Dzina la Yesu Khristu. Chabwino. Chabwino, ine ndikuchoka kumka ku mibadwo ya mpingo tsopano.

81 Zindikirani. Koma, apa, pamene ife tikufika ku Chisindikizo Chachisanu ichi tsopano, apo pali—apo pali—apo palibe wokwera amene akutulukira, ndipo apo palibe Chamoyo choti chirengeze Icho. Yohane basi... Mwanawankhosa anatsegula Icho, ndipo Yohane anachiwona Icho. Apo panalibe mmodzi aliyense pamenepo kuti anene, “Tsopano bwera, yang’ana. Bwera, udzawone.” Zindikirani, panalibe mphamvu ya Cholengedwa chamoyo. Kapena apo pali. . .

82 Ndipo pa Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi, palibe Chamoyo choti chirengeze Icho. Ndipo pa Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, palibe Chamoyo choti chirengeze Icho. Palibe mphamvu yoti irengeze Icho. Mwawona, palibe mmodzi amene akuchita izo. Pa. . .Penyani. Pa. . .Chitachitika Chisindikizo Chachinai, palibe kulengeza mwa mphamvu iliyonse ya Chamoyo, kuchokera pa Chisindikizo Chachisanu, Chachisanu ndi chimodzi, kapena Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri, palibe konse.

⁸³ Tsopano zindikirani. Ine ndikuzikonda izi. Monga mu nthawi za wokwera wa akavalo anai, wokwera (mmodzi) wa akavalo anai osiyana, apo panali Chamoyo chimene chinkalengeza mphamvu. Nthawi iliyonse wokwera ankakwera kavalo wina ndi kubwera kudzakwera, Chamoyo chamtundu wina chinkatuluka ndi kulengeza icho, “Ndicho chinsinsi chachikulu.” Mwawona? “Icho chiri chinsinsi.” Chifukwa? Kulengeza chinsinsi.

⁸⁴ Chifukwa chiyani palibe chimodzi apa pa Chisindikizo Chachisanu, kuti chirengeze Icho? Apa icho chiri, molingana nalo vumbulutso limene Ambuye Yesu anandipatsa ine lero, onani, kapena mmawa uwu, mmamawa. Ndicho, kuti, chinsinsi cha mibadwo ya mpingo chatsirizika kale, pa nthawi iyi. Chinsinsi cha wotsutsakhristu chawululidwa, pa nthawi iyi. Wotsutsakhristu anatenga kukwera kwake kotsiriza, ndipo ife tinamupeza iye pa kavalo wotumbululuka wake, wosakanizidwa ndi mitundu yake yambiri, ndipo akukwera njira yonse mpaka ku chitayiko.

⁸⁵ Ife tizipeza izo pa Malipenga, ndi zina zotero, pamene ife tiphunzitse zimenezo. Ine ndikanapita kwa izo tsopano, koma ife tichoka ku phunziro kachiwiri. Ndipo ife—ife tipite. . . iye akukwera. . .

⁸⁶ Ndicho chifukwa chake palibe mmodzi aliyense pamenepo. Tsopano, ife tiribe chifukwa cholembedwa, zifukwa zina za chinachake. Tsopano, inu kumbukirani, poyamba, kuyamba, ine ndinati sipangakhale kanthu popanda chifukwa. Mumbukira dontho laling’ono la inki? Mukuwona? Tsopano inu muyenera kupeza chifukwa. Pali chifukwa chimene iwo sanasowe kukhala nacho Chamoyo, kapena mphamvu, kuti alengeze Chisindikizo ichi chikumatulidwa. Ndipo Mulungu yekha akhoza kuwulula chifukwa, ndizo zonse, chifukwa Ndicho zonse—zonse zagona mwa Iye.

⁸⁷ Koma chifukwa chimene Iye akuwululira Icho, monga momwe ine ndikumvetsera, kuti icho chiri chifukwa chinsinsi cha Bukhu la Chiwombolo, malingana monga wotsutsakhristu akuwululidwa; ndipo panthawi yomweyo, Mpingo wapita, ndipo zinthu izi sizikuchitika konse mu m’badwo wa mpingo, konse. Uko nkulondola. Izo ziri—izo ziri kutali ndi mibadwo ya mpingo. Mpingo mwamtheradi Wakwatulidwa, pa nthawi iyi. Mpingo ukupita mmwamba, mu mutu wa 4 wa Chivumbulutso, ndipo sukubwerera mpaka Iwo ukubwerera ndi Mfumu Yake, mu mutu wa 19. Koma Zisindikizo izi apa zikuwulula zimene zakhala ziripo, zomwe ziri, ndi zomwe ziti zidzakhale. Mukuwona? Ndipo, tsopano, zomwe zinali zoti zidzakhale za m’badwo wa mpingo, zinawululidwa ndi Zisindikizo izi. Ndipo tsopano yang’anani zomwe zikutenga Icho.

⁸⁸ M—masiteji anai a wokwera wake awululidwa kale. Masiteji anai a wotsutsakhristu, akukwera, awululidwa pa nthawi iyi, chotero iwo sasowa kukhala nawo enanso.

⁸⁹ Ndipo apo panali Zolengedwa zamoyo zinai za Mulungu, kuti zilengeze wokwera pamene iwo ankakwera. Zamoyo zinai ziri mphamvu zinai. Tsopano, ife tikudziwa kuti *Chamoyo*, mwa kutanthawuzira kwa manenedwe a zophiphiritsa za m’Baibulo, chimatanthawuza “mphamvu.” Tsopano, tiyeni titenge izo mwacheru. Zinai ndi Zamoyo, mu Baibulo, kuyimira mphamvu pakati pa anthu.

⁹⁰ Tsopano, ife tikupeza, monga mu Daniele, pamene iye anawona fuko linalake likuwuka, ilo likanakhala mwina chimbalangodo chitagwira nthiti mu mbali mwake, mwa chophiphiritsa. Ndiye iye anawona mphamvu yina ikuwuka, mbuzi. Iyo inkayimira chinachake. Ndiye iye anawona mphamvu yina ikuwuka, ndipo—ndipo iyo inali kambuku ali ndi mitu yambiri. Iye ankayimira ufumu winawake. Ndiye iye anawona mmodzi wina akuwuka, mkango waukulu uli nawo mano, ndipo—ndipo unapondereza zotsalira. Izo zinkayimira mphamvu yosiyana, palimodzi. Umodzi unali u—ufumu wa Nebukadinezara; ndi wina, mtundu wa—wa loto. Daniele anawona masomphenya; Nebukadinezara analota loto. Koma Daniele anamasulira loto lake, ndipo linali molondola ndi masomphenya.

⁹¹ Ameni! Psyii! O! [M’bale Branham awombetsa manja ake palimodzi kamodzi—Mkonzi.] Ngati inu mukanangodziwa zomwe zinachitika! Chinachitika nchiyani ife tisanachoke kuno? Inu mukumvetsa? Chifukwa, maloto asanu ndi amodzi olunjika anabwera chimodzimodzi ndi masomphenya. Ameni. Mukuwona? Loto, lomasuliridwa, liri masomphenya. Chifukwa munthu mwina posakhala wobadwa nacho chikumbumtima kuti akhale, ali maso pamene iye akuwona izo, ndiye Mulungu amabwera mu chikumbumtima ichi ndi kulankhula kwa iye. Chimene, Iye analonjeza kuti, mu maloto, mu masiku otsiriza, Iye adzawachezera anthu, ndiponso mu masomphenya. Mukuwona?

⁹² Tsopano, masomphenya ali pamene iwe uli chipenyere maso, utayimirira kumene monga chonchi, ndipo zinthu zina nkumawululidwa. Ndi kuyima, nkumawawuza iwo kumene za izo; kumawona zomwe zinachitika, ndi zimene ziti zikhalepo, ndi zina zotero.

⁹³ Koma, tsopano, loto liri pamene iwe ukugona, ndipo mphamvu zisanu zako zisakugwira ntchito, ndipo iwe uli—iwe uli mu chikumbumtima chako. Iwe uli kwina kwake, chifukwa, pamene iwe ubwererako, iwe umakumbukira kumene iwe unali, umakumbukira izo moyo wako wonse. Mukuwona? Koteru, ndicho chikumbumtima chako. Ndiye polinga kuti, onani. . .

⁹⁴ Monga Congressman Upshaw anakonda kunena kuti, “Iwe sungakhale chinachake chomwe iwe siwuli.” Ndipo ndicho chapafupi kulondola basi, mwawona.

⁹⁵ Ndipo, ndiye, ngati iwe ubadwa mpenyi. Tsopano, inu mukuwona, kuti uchite izo, zikumbumtima zonse izo ziyenera kukhala pamodzi kumene; osati chimodzi *apa* ndi mphamvu zisanu, zikugwira ntchito, ndipo china kutali *apa* pamene iwe uli chigonere, ndipo mphamvu zisanu zisakugwira ntchito. Koma, inu mukuwona, pamene zonse za izo, iwe umabadwa, limodzi nazo, iwe sumapita kukagona. Iwe umangopita kuchokera ku chimodzi kupita ku chimodzi china, monga—monga choncho. Iwe sumapita kukagona. Palibe malo okwanira kuti ukagone. Ndipo iwe sungakhoze kudzipanga wekha mwanjira iyo.

⁹⁶ Kotero, “Mphatso ndi kuyitana ziri zokonzedweratu za Mulungu.” Izo ziri—izo ziri mphatso za Mulungu ndi kuyitana, ngakhale “popanda kulapa,” Baibulo linatero. Mukuwona? Izo zinakonzedweratu kusanakhale maziko a dziko. Mukuwona?

⁹⁷ Tsopano, tsopano, ife tikupeza kuti... Chamoyo, cha Daniele, icho chinkatanthawuza kuti icho chinali mphamvu ikuwuka pakati pa anthu. Chabwino. Ndipo—ndipo masomphenya a Yohane apa, nawonso, anawonetsa kuti zinali mphamvu, mafuko akuwuka. Monga, United States akuwonekera mu Chivumbulutso 13, monga mwanawankhosa. Ndiyen ngati inu mukufuna kudziwa, kusiyana. . .

Inu mukuti, “Chabwino, izo, ndiko kulankhula za mphamvu ya fuko.”

⁹⁸ Izo zimayimiranso mphamvu yoyera, nayonso, chamoyo. Kodi inu mumadziwa zimenezo?

⁹⁹ Zindikirani Rabeka; pamene—pamene w—wantchito wa Abrahamu, Eliyeza. . . Pamene iye anabwera kudzamutenga - beka—Rabeka, iye. . . Iye anamukweza iye pa ngamira, ngamira yomweyo imene iye anayipatsa madzi. Ndipo iye anakwera ngamira iyi, kukakumana naye mkwati wake wosawoneka. Chinthu chomwecho chimene iye anachipatsa madzi, chinali chinthu chimene chinamutengera iye kwawo kwa mtsogolo ndi mwamuna wake.

¹⁰⁰ Ndipo ndicho chinthu chomwecho lero, mwawona. Chinthu chomwecho chimene Mpingo ukuthirira madzi, imeneyo ili Mbewu, Mbewu ya Mawu. Ali Mawu omwewo amene akukhala amoyo ndi kutinyamulira ife kupita kwa Mkwati wathu wosawoneka. Mukuwona? Mukuwona?

¹⁰¹ Ndipo penyani momwe mwangwiro. Isaki anali atachoka kwawo, ndipo anali kunja mminda, kutali ndi kwawo, pamene Rebeka anamuwona iye.

¹⁰² Ndipo Mpingo ukukumana naye Khristu mu mlengalenga, ndiyeno Iye akumutengera Iye kubwera Kwawo, Kwawo kwa

Atate, kumene nyumba zakonzedwa. Isaki anamutenga Rabeka mwanjira yomweyo.

¹⁰³ Ndipo, zindikirani, icho chinali chikondi pa kuwonana koyamba. O, mai! Iye anangothamanga kukakumana naye iye.

¹⁰⁴ Ndipo ndimo momwe Mpingo udzakumanirane naye Khristu, mu mlengalenga, ndipo kwanthawizonse kukakhala naye Iye.

¹⁰⁵ Tsopano, mwamanenedwe a Baibulo, Zamoyo izi ziri mphamvu. Zindikirani. Ine ndikufuna, tsopano, ine ndikufuna inu muzindikire.

¹⁰⁶ Mdierekezi anali nazo zake zinai, kusintha, zamoyo zamitundu, kuti apite nazo patsogolo. Iye anali nazo zamoyo zake zinai. Zimenezo zinali zonse zitatu za izo, kuyikidwa mu mtundu wa chimodzi, ndipo anapanga mmodzi ameneyo k—kavalu wotumbululuka; kavalo woyera, kavalo wofiira, kavalo wakuda. Ndipo ife tinawona, aliyense wa iwo inali siteji ya utumiki wake, siteji ya mpingo woyambirira umene unali utapangidwa kukhala chipembedzo, ku Nicaea. Mpingo woyambirira wa Chipentekoste, pa umene Mzimu Woyera unatsanuliridwapo, kubwera pansu, unatenga mzimu wotsutsakhristu, unapanga bungwe, unabala ana akazi ena achibungwe. Unasintha mphamvu yake, nthawi zitatu, ndi kuziyika izo mwa imodzi, ndipo anapanga kavalo wotumbululuka. Ndiyeno anapatsidwa dzina lotchedwa Imfa, ndipo anamukwera iye kumka mu Muyaya. Mophweka basi monga momwe zingakhalire! Tsopano, tsopano zindikirani, iye wapatsidwa uyu—kavalu uyu, ndipo iye akumukwera iye.

Mulungu, Mulungu ali naye, nayenso, pamene nthawi iliyonse. . .

¹⁰⁷ Tsopano yang'anani. Pamene wotsutsakhristu anawonekera, koyamba, kodi iye anawonekera mwa chiyani? Kavalo woyera. Mukuwona, bwanji, wosalakwa monga iye akanakhoza kukhalira, chiphunzitso chabe mu mpingo. Iwo ankafuna chijanano. Chijanano chanu chiri ndi Khristu. Koma iwo ankafuna chijanano. Iwo sanakhoze chabe kupirira icho, iwo ankafuna kupeza. . .

¹⁰⁸ Chabwino, inu mukudziwa, tonga timalingaliro tating'ono tidzawuka mu mpingo. Inu, inu mukudziwa zimenezo, inu azibusa. Mukuwona? Iwo, momwe iwo anati, "Mbalame za nthenga." Koma ngati ife tiri obadwa kachiwiri, abale, icho—sindiko kalingaliridwe koti utenge, mwawona. Ayi. Tsopano, ife—ife—ife. . .

¹⁰⁹ Ngati ife tiwona chinachake cholakwika mwa abale athu, tiyeni ife tingopemphera ndi kuchisunga icho pamaso pa Mulungu, ndi kumukonda munthu ameneyo mpaka ife timubweretse iye mu Kukhalapo komwe kwa Mulungu. Mukuwona? Ndiyo njira, kwenikweni njira yochitira izo.

110 Inu mukudziwa, Yesu anati. “Padzakhala mawuzu mmenemo,” chifukwa Yesu anati adzakhala mmenemo, “koma musati muwazule iwo; inu mudzatenga tirigu limodzi nawo.” Mwawona, “Ingozisiyani izo zokha.” Iye adzachita... Musiyeni Iye achite masankhidwe pamene nthawi ifika. Mukuwona? Zisiyeni izo zonse zikulire pamodzi.

111 Zindikirani, pamene chamoyo chinatuluka, wotsutsakhristu anatsika pa chamoyo, mphamvu yake.

112 O, ine ndimakonda izi! Ine ndikungoyamba kumverera mwachipembedzo pakali pano, onani, mwinamwake kukondoweza. Zindikirani, pamene wotsutsakhristu... O, awo—mavumbulutso awo, mu Kukhalapo kwa mpira uwo wa Moto utapachikika pamenepo mu chipindamo! Mpaka... O, m'bale! Ngakhale ine ndachiwona Icho, kuyambira ndiri mwana, nthawi iliyonse Icho chimafika pafupi ndi ine, Icho chimandiwopsyeya ine. Iye pafupifupi amandiyika ine mu chikhalidwe cha kukomoka. Iwe sumazolowerana nacho Icho; iwe sungakhoze. Ndi chopatulika kwambiri.

113 Zindikirani, pamene wotsutsakhristu anapita (zinai) pa zirombo zake za utumiki, pamenepo, Mulungu anatumiza Chamoyo kukamenyana nacho icho. Mukuwona? Tsopano yang'anani. Ndiye, nthawi iliyonse (chamoyo chinkakwera) pa kavalo wake, wotsutsakhristu ankakwera pa kavalo wake, pa chirobho chake, kukalengeza utumiki wake; Mulungu ankatumiza Chamoyo Chake, nayenso, ndipo Iye anali pa Icho, kukalengeza kumenyana Kwake ndi icho.

114 Tsopano, Lemba limati, “Pamene mdani abwera mkati monga kusefukira kwa madzi, Mzimu wa Mulungu umadzutsa muyeso womutsutsa iye.”

115 Ndipo kotero pamene mdani anapita kunja monga wotsutsakhristu; Mulungu anatumiza mphamvu ya mtundu wina kukakumana naye iye. Ndiyeno pamene iwo... .

116 Iye anapita kunja kachiwiri, monga wokwera pa kavalo wofiira, mtundu wina, mphamvu yina, utumiki wina; Mulungu anatumiza mmodzi wina pambuyo pa iye, kukamenyana naye iye, kuti ukagwire Mpingo Wake.

117 Anatumiza chimodzi chachitatu; apanso, Mulungu anatumiza Chake, Chamoyo chachitatu chinabwera ndipo chinalengeza icho.

118 Iye anatumiza chimodzi chachinai; Mulungu anatumiza chimodzi Chake chachinai. Ndiyeno wotsutsakhristu akutha, ndipo mibadwo ya mpingo inatha, nayonso, pa nthawi imeneyo. Yang'anani. Tsopano, o, izi ndi zabwino kwenikweni!

119 Tsopano, ife tikuwona kuti mdierekezi akusintha, zinai—zamoyo zinai, zinkatanthawuza mphamvu zimene izo zinawululidwirako... .kapena mphamvu imene iye anawulula

kwa dziko, ndipo momwe iwo anathera pa wotumbululuka uyu, kavalo wa “imfa.”

120 Tsopano tiyeni tiyang’ane pa mphamvu ya Mulungu, ya Zamoyo izi, kuti zimenyane nawo.

121 Chamoyo choyamba cha Mulungu, chimene Iye anapita nacho kukakomana naye wotsutsakhristu, mzimu wotsutsakhristu pamene uli mu kuphunzitsa kwake chabe. Tsopano kumbukirani, pamene wotsutsakhristu anakwera koyamba, iye anali mu utumiki wa kuphunzitsa. Wotsutsakhristu anakwera, poyamba, mu utumiki wa kuphunzitsa. Tsopano yang’anani mmodzi amene anapita kukakomana naye iye: mkango, Mkango wa fuko la Yuda, amene ali Mawu. Pamene kuphunzitsa kwabodza kwake kunapita, Mawu owona anapita kukakomana naye iye.

122 Ndicho chifukwa chake ife tiri naye Ireniyasi, ndi Polekapu, ndi—ndi—ndi—ndi anyamata amenewo, Marteni Woyera.

123 Pamene wotsutsakhristu ameneyo anali kukwera ndi kuphunzitsa kwake kwabodza; Mulungu anatumiza Kuphunzitsa Kwake, Mawu, Mkango wa fuko la Yuda, amene ali Mawu atawonetseredwa mwa Mzimu Woyera. Ndipo Mzimu Woyera, mmenemo, kuti ukawonetsere Iyemwini, amene ali Mawu!

124 Ndicho chifukwa chake Mpingo woyambirira unali nawo machiritso, ndi zozizwitsa, ndi masomphenya, ndi mphamvu, chiri chifukwa iwo anali Mawu amoyo, mwa mawonekedwe a Mkango wa fuko la Yuda, ukukwera chotuluka kukamenyana nacho chimenecho. Amen! Tsopano inu mwamvetsa izo? Iye akutumiza mphamvu yake, wotsutsakhristu; Mulungu akutumiza Yake, Mawu. Wotsutsakhristu, kuphunzitsa kwabodza; Kuphunzitsa kowona kunapita nawo iwo, kukamenyana nacho icho! Tsopano, uwo unali umodzi woyamba. Tsopano, uwu unali Mpingo woyamba, wautumwi, umene unapita kukakomana naye iye.

125 Tsopano, chamoyo chachiwiri chimene wotsutsakhristu anachitumiza, chinali chamoyo chofiira, chimene chinali kuka... chimene iye anakwerapo, chinali kuti chikatenge mtendere (ndi) kuchokera pa dziko lapansi, ndi—ndi nkondo.

126 Tsopano, chimodzi chachiwiri chimene chinapita kukamenyana naye iye, chinali Chamoyo cha ng’ombe. Ng’ombe imatanthawuza kuvutikira, Chamoyo cha kulemedwa.

127 Ndipo tsopano ngati ife tikanakhoza kuyima miniti chabe. Ndiroleni ine, eya, ndiroleni ine, chabe kotero inu mukhale otsimikiza kuchiwona ichi tsopano. Tsopano, ndicho cha mtundu umene ungakhale wosokoneza pang’ono kwa inu. Koma tiyeni titenge Tiyatira cha apa. Yang’anani ndipo tiwone ngati sululi m—Mpingo wovutikira, inu mukuwona.

Ndipo kwa mngelo wa mpingo wa Tiyatira lemba; Zinthu izi anena Mwana wa Mulungu, yemwe maso ake ali monga malawi a moto, ndi mapazi ake ali monga mkuwa wonyezimira;

Ine ndikudziwa ntchito zako, . . .

128 Mwawona, zonse zikukhala ntchito tsopano, onani, chifukwa ndicho chimodzi chinali kukwera naye iye.

. . . ndi chikondi chako, ndi utumiki, (onani, zonse ziri basi. . .) ndi chikhulupiro, ndi . . . chipiro, ndi ntchito zako (apanso, kachiwiri, “ntchito zako”), ndipo zotsiriza kukhala zochuluka kuposa zoyamba.

129 Onani, izo zikusonyeza kuti, M’badwo wa Tiyatira, wotsutsakhristu atakhazikika panso ndi kubwera mu M’badwo wa Tiyatira, Mpingo wawung’ono sukanachita kanthu koma basi—mophweka chabe kuvutikira.

130 Ndipo chinthu china, ng’ombe ili, nayonso, ili Chamoyo cha nsembe. Mukuwona? Iwo anapereka miyoyo yawo basi mwawulere monga iwo akanakhozera kuyipereka iyo, mu mibadwo ya mdima, zaka chikwi kumeneko zomwe Chikatolika chinkalamulira dziko. Ndipo iwo anangolowa mkati, inde kapena ayi. Iwo sanasamale za kufa. Ngati iyo inali imfa, ndizo zonse zabwino. Iwo anapita ndi kukafa, mulimonse. Chifukwa? Mzimu umene wa m’badwo!

131 Ndicho chifukwa chake iwo, ndicho chifukwa chake Ireniyasi, ndicho chifukwa chake Polekapu, Yohane, Paulo, amuna amphamvu ndi opambana awo kumeneko, akumenyana nacho chinthu chimenecho!

132 Paulo anachiwona icho. Iye anati, “Ine ndikudziwa, kuti pambuyo pa kuchoka kwanga, kuti mimbulu idzalowa pakati pa inu, abale, kuphunzitsa zinthu zosokoneza, ndipo iyo idzakukokerani inu kutali.” Yang’anani pa kulimba uko, kamtumwi kokalamba katayima pamenepo, nsana wake utamenyedwa utadzaza mikwingwirima, maso ake amisonzi. Koma iye amakhoza kuyang’ana patali kuposa chawo. . . choyang’anira icho akuchiseweretsa icho kutsidya, chimene iwo angakhoze kupenyera zaka zowala mamilioni zana ndi makumi awiri za danga la kuwala. Iye akanakhoza kupenyu mpaka mu Muyaya. Apo iye anali. Ndipo iye ananeneratu zimenezo ndipo anati kuti izo ziri zomwe zikanadzachitika. Ndipo anati, nayenso, anapita mpaka mmusi ku m’badwo wina wakudza. Tsopano zindikirani, apo iye anali.

133 Motsatira, iye atapita, Yohane Woyera anakhala motalika kwambiri. Ndipo pamene Yohane Woyera anali kuyesera kutenga akalata onse opatulika, atadzozedwa nawo Mzimu Woyera, ndi kuwayika iwo palimodzi kuti apange Baibulo, ufumu wa Roma unamugwira iye ndi kumuyika iye pa Chisumbu cha Patmo. Iye anali kunjira kumeneko pa Chisumbu cha Patmo

chifukwa cha Mawu a Mulungu. Polekapu anali kumuthandizira iye kumasulira iwo.

¹³⁴ Ine ndinawerenga, tsiku lina, kalata imene Maria iyemwini analemba kwa Polekapu. Ndi kumamudzudzula... osati kumudzudzula iye. Koma kumuyamikira iye chifukwa chokhala mwamuna wochirimika yemwe amakhoza kuphunzitsa ndi kulandira zophunzitsa za Yesu Khristu, Yemwe anali wobadwa kwa iye, kuchokera kwa Mulungu. Zolemba zake zomwe za Maria zimene iye analemba kwa Polekapu.

¹³⁵ Polekapu anadyetsedwa kwa mikango, inu mukudziwa. Ayi, iye anawotchedwa. I—inali nthawi itatha kuti iwo amasule mkango mosungiramo zinyama, ndipo kotero iwo anangophwasula bafa, nyumba yosambiramo yakale kumeneko, ndi kumuyika iye mu—mu—pabwalo ndi—ndi kumuwocha iye.

¹³⁶ Ndipo pa panjira yake, akubwera mmusi, iye anali akuyenda mutu wake atazyolika. Kenturiyo wa Chiroma anati, “Ndiwe munthu wachikulire, ndi wolemekezedwa bwino. Bwanji iwe osachinyoza chinthu chimenecho?”

¹³⁷ Iye anangopitirira kuyang’ana Kumwamba. Ndipo Liwu linalankhula kuchokera kwina kwake. Iwo sanakhoze kumvetsa ndi kuti. Anati, “Polekapu, usawope. Ine ndiri ndi iwe.” A-ha. Chifukwa? Iye anali kuyima ndi Mawu amenewo.

¹³⁸ Ndipo pamene iwo anayamba kuwunjika zipapati pa iye, kuti amuwotche iye, panali nyimbo Yakumwamba ikubwera pansu. Ndipo—ndipo nyimbo zikuchokera kwa Angelo ena kwina kwake akuyimba nyimbo. Iye sanakhoze ngakhale nthawi imodzi kuphethira diso kwa onyoza.

¹³⁹ Ndiwo amuna ochirimika. Ndiwo amuna amene angakhoze kuyima. Ofera mmusi kupyola mu mibadwo, kumeneko, anavutika moyipa. Koma iwo anali chiyani? Iwo anali pansu pa kudzoza, Mzimu wa Mulungu, mphamvu. Ine. . .

¹⁴⁰ Musati muyiwale ichi, mpingo. Ndipo inu abale, pa tepi, ine ndikufuna inu muchiyese ichi. Anthu akanakhoza bwanji kuchita china chirichonse pambali pa mphamvu ya Mulungu imene inali itaperekedwa kwa iwo? Ine ndiyika bokosi ili apa, kuti liyimire zimenezo. Ngati Mulungu atumiza Mzimu winawake pakati pa iwo, ndicho chinthu chokha chimene iwo angagwire nacho ntchito, chiri Mzimu umene umagwira ntchito pakati pawo. Tsopano titsimikizira kwa inu, mwa mbiriyakale ya Mpingo, ndi mwa—kutsegula kwa Zisindikizo, ndi mphamvu zimene zamasulidwa; ndi kupenya, chimodzimidzi, Mpingo unavomereza ku—kukudzoza, ndipo iwo sakanakhoza kuchita kanthu kalikonse.

¹⁴¹ Tsopano, choyamba chinali mkango umenewo umene unabangula, Mawu angwiro, osakhudzidwa aja.

142 Chachiwiri, mu Tiyatira, chinali ng'ombe. Ndipo Icho chinali—cholemedwa... Chamoyo cholemedwa. Mundikhululukire ine. Ndipo Icho chinalinso Chamoyo chansembe. Ndipo kodi sunali umenewo chimodzimidzi Mpingo wosawuka, wawung'ono? Roma anali atakhazika pansi kumeneko, kwa zaka chikwi za mibadwo ya mdima, ndi chirichonse chimene sichinavomereze kuti chiri cha mpingo wa Roma chinkaphedwa mwamsanga. Ndipo iwo ankachita kuvutikira, kuchokera pa malo kumka ku malo.

143 Inu a Masons, ine ndiyitana tcheru chanu. Inu mukukumbukira chizindikiro cha mtanda? Tsopano inu—inu mukudziwa chimene ine ndikulankhula.

144 Tsopano zindikirani. Tsopano, ngati inu—ngati inu mungazindikire, uko kunali kupachila ndi kusamalira Baibulo limenelo. Mukuwona? Ndipo iwo ankachita kuvutikirana pakati pa wina ndi mzake. Ndi zimenezotu, ng'ombe. Ndipo pamene inafika nthawi... Iye tinawerenga izo usiku watha. Mwawona, pamene chinthucho chinatuluka, ndipo nsembe nkubwera, ndipo iwo ankayenera kupita.

Iye anati, “Musati inu muwononge vinyo ndi Mafuta.”

145 Anachita chiyani iwo? Iwo mololera anapita kumeneko ndipo anafa. Iwo sanachite koma kusamala, chifukwa Mzimu wa Mpingo mu tsiku limenelo unali nsembe, kuvutikira. Ndipo iwo ankayendera kubwera basi momasuka momwe iwo akanayendera, atadzedwa nawo Mzimu woona wa Mulungu wa m'badwo umenewo, ndipo anafa ngati agonjetsi, nsembe; zikwi kuchulukitsa zikwi, mamilioni makumi asanu ndi imodzi mphambu zisanu ndi zitatu za iwo pa kawundula.

146 Ng'ombe, nsembe! O, mai! Kodi inu mukumvetsa izi? [Osonkhana ati, “Ameni”—Mkonzi.] Chabwino. Zabwino. Tsopano, nsembe, iyo ikanangokhoza kugwira ntchito mu m'badwo umenewo, kuti imenyane nako kutsutsa kwakukulu kwa zaka chikwi chimodzi uko.

147 Tsopano, chamoyo chachitatu chimene chinatuluka kuchokera kwa Mdierekezi, chinali kavalo wakuda uyu. Mukuwona?

148 Tsopano, Chamoyo chachitatu chimene chinatuluka, mphamvu yochokera kwa Mulungu, kukamenyana naye iye, kukamenyana nayo mphamvu za kavalo wakuda; anali munthu, wokanika, wochenjera, ali nazo nzeru za Mulungu. Inu mukudziwa, munthu ndi wochenjera, kuposa chamoyo chirichonse. Mukuwona? Iye ali wochenjererapo, chifukwa iye akhoza kumugonjetsa iye, kwambiri. Iye ali wokanika, thyaka. Mukuwona? Ndipo iye... .

149 M—m'badwo, kuchokera ku m'badwo wa mdima, tsopano kubwera kuchokera mu m'badwo wa mdima; tsopano, mbali ina iyi, pamene kavalo wakuda uyu anali kuyenda, pamene iwo

ankalipiritsa zawo—zawo—zawo—nsembe zawo ndi chirichonse chimene iwo ankachita. Ndipo ndalama zinali chabe. . . O, inu mukudziwa momwe izo zinaliri.

¹⁵⁰ Tsopano, chinthu chotsatira chimene chinatuluka, kukamenyana nacho icho, chinali Chamoyo chokhala nayo nkhope ya munthu; wochenjera, wophunzira, wothyathyalika, wabwino, wodzozedwa nawo Mzimu umenewo wa tsiku limenelo. Inu mukuzindikira zimenezo? Tsopano, iye anapita kukamenyana naye, ndi kukanika kwa nzeru za Mulungu limodzi naye. Uwo unali m'badwo wa kukonzanso, Marteni Lutera, Joni Wesile, ndi ena otero. Mukuwona, uko kunali kukonzanso. Zwingli, ndi, o, onse amene, Knox, Calvin, ndi onse amene, mwawona, anatuluka. Iko kunali kukanika. Tsopano, inu mupenye, chimodzimodzi kuchokera ku m'badwo wa mdima, kuchokera ku kukonzanso, mwanjira iyi, yang'anani, iko kunali kuthyathyalika kwa munthu.

¹⁵¹ Ngati inu mungatsitse mazenera anu pang'ono chabe! Ine ndikukhulupirira anthu akukhala ngati atenthedwa pang'ono, eya, mwinamwake, mkati umo. Ngati inu mukanati mungotsitsira mazenerawo mmusi pang'ono pokha. Chifukwa, ine ndikudziwa, ngati ine ndikuyimirira apa kumalalikira, ndikumva kutentha, ine ndikudziwa inu muyenera kutero, kumenekonso.

¹⁵² Chabwino, zindikirani, iko kunali kuthyathyalika kwa munthu. Tsopano, kodi inu mukumvetsa?

¹⁵³ Chamoyo chachitatu icho chimene Satana anachitumiza, iye akukhala wothyathyalika, nayenso. Yang'anani, "Muyeso wa tirigu wogula rupiya. Miyeso itatu ya barele kugula rupiya." Mukuwona? O, mai! Mukuwona? Njira yopangirandalama, kuthyathyalika, kuti atenge golide wa dziko, ndi chuma, kubweretsedwa mwa icho. Ndicho chimodzimodzi kuti akwaniritse. Ndicho chimene chinayambitsa kulipiritsa mapemphero. Ndipo kwa. . . Anapanga malo otchedwa purigatorio, ndipo ankapempherera makolo awo kuti achokeko. Ndipo, o, iwe umayenera kupereka chikalata chaumwini ndi chirichonse, malo ako. Mpingo, ndi boma zinali zofanana, ndipo mpingo umalanda malo akowo.

¹⁵⁴ Ndipo kodi inu simukuwawona, ena a alaliki awa, tsiku lino, akadali nako kudzoza komweko pa iwo? Kuwapangitsa anthu okalamba kupereka mapenshoni awo a ntchito, ndi kupinyolitsa nyumba zawo pa zinthu zina zake. Chifukwa, m'bale, ine—ine sindikufuna kufika pa izo, mwawona. Koma tsopano ine ndikhala ndi chomwechi; ine ndikuyang'ana mmbuyo kuti ndiwone kumene ndikupita. Tsopano zindikirani, anthu amenewo, ziri kwa iwo. Ziri kwa iwo. Izo—izo—izo ziribe chinthu chimodzi chochita ndi ine. Ine ndiri wokhuzidwa kokha ndi Izi pano.

155 Tsopano zindikirani, c—Chamoyo chinabwera kudzamenyana ndi icho, tsopano, chinali munthu. Ndipo ife tonse tikudziwa kuti Chamoyo ichi, cha munthu, mphamvu iyi ya munthu, mu luntha lake, anazindikira kuti mkate uja umene Marteni Lutera anali nawo mdzanja lake, pamene iye anali kukwera masitepe amenewo. . .

156 Iwo anati, “*Awa* ndi Magazi a Yesu Khristu. *Ili* ndi thupi la Yesu Khristu.”

157 Ndipo Lutera anawuponya iwo pansi, ndipo anati, “Ndi mkate ndi vinyo. Osati thupi la Khristu; chifukwa, ilo linakwezedwa, ndipo akukhala pa dzanja lamanja la Mulungu, kupanga chitetezero.” Mukuwona, nzeru; mukuwona, munthu.

158 Ndipo pamene Joni Wesile anabwera motsatira, atatha Zwingli kubweramo, ndi Calvin.

159 Ndipo iwo anawufikitsa mpingo ku malo, pa chitetezero, mpaka iwo sanafune zitsitsimutso zinanso. “Chirichonse chimene chiti chikhalepo chikhalapo.” Izo zinali zonse. Ndipo iwo ankangokhala miyoyo ya mtundu uliwonse. Mpingo wa Lutera uli wopotozedwa kwambiri, ndi mpingo wa Angilikani! O, mai! Dziko lonse lakhala lovunda, basi monga ziliri tsopano. Mipingo inali itapotozedwa. Pamene Mfumu Henry ya—ya VIII, ndi kubwera mu England, ndipo atatha Maria wamagazi, ndipo zinthu zonse izi zitachitika. Ndipo, ndiye, mpingo unali utadzaza ndi chiwawa ndi chivundi. Ambiri kumati ali nacho Chikhristu, ndi kumakhala nawo akazi anai kapena akazi asanu, kapena kumachita chirichonse iwo ankafuna kuchita, ndi kumapitirirabe, ndi zonyansa.

160 Joni Wesile, powerenga Lemba, kuliyang’ana Ilo, izo zinawululidwa kwa iye kuti Magazi a Yesu Khristu amayeretsa wokhulupirira. Ndipo ndipo. . .sukuyenera. . .Ndiye iye anachita chiyani? Iye anatuluka mu kukonzanso kwina. Iye anapulumutsa dziko mu tsiku lake, monga Lutera anachitira. Mukuwona? Chinali chiyani icho? Munthu ameneyo, mphamvu ya Chamoyo, chikupita uko.

161 Kumupatsa munthu nzeru, za kumvetsa, kuti chinthucho ndi cholakwika. “Amenewo si Magazi a Yesu Khristu. Iwo suli—thupi la Yesu Khristu. Iwo ukuyimira thupi.” Mukuwona?

162 Iwo ukadali mkangano wawukulu pakati pa Akatolika ndi Aprotostanti tsopano. Ndicho chinthu chokhacho chimene iwe sungakhalire pamodzi nawo pano. China chirichonse, iwo akhoza kukhalira pamodzi, koma icho; awa mu mu mabungwe akukhala nawo. Zindikirani tsopano. Koma, ichi, koma iwo—iwo sakanakhoza kukhalira pamodzi pa chimenecho. [M’bale Branham agogoda pa guwa nthawi zitatu—Mkonzi.] Mukuwona?

163 Mmodzi, “Ndi Magazi, ndipo,” akuti, “ndi Magazi weniweni; wansembe uyo ali nayo mphamvu yosintha mkate uwu kukhala thupi lenileni la Khristu.” Ndicho chimene kachisi wamng’ono

ali, mu—mu tchalitchi, inu mukudziwa. Ndicho chifukwa iwo amapanga zizindikiro ndi ndi nsembe yamtundu uliwonse ya chikunja yomwe iwo amachita nayo, inu mukudziwa, ndi kudzigwaditsa okha, ndi kuvula zipewa zawo, ndi zina zotero. Izo siziri kwa nyumbayo; ndi kwa mkate uwo umene uli mu—kachisi. Ndipo zindikirani momwe Satana mothyathyalika anakokera izo!

¹⁶⁴ Koma, onani, pa nthawi imeneyo, pa thunthu la munthu, mwawona, Mulungu anayika Mzimu wa nzeru pa munthu, kuti akamvetse kuti icho ndi cholakwika. Tsopano, kumeneko kunali kuti amenyane nacho chamoyo chachitatu, chimene chinafikitsa mpingo povunda kwambiri, umene iye anali kukwera, kuti zinali zowopsya. Okonzanso, anachita chiyani iwo ndiye, iwo a mu m’badwo wa okonzanso? Iwo anawubweretsa Mpingo, kuchokera ku miyambo yake ya chikunja ya mafano, kubwerera kwa Mulungu kachiwiri. Mukuwona? Ndicho chimene Chamoyo chinatulukira, kuthyathyalika uko kwa munthu, wokwera, kukachita zimenezo.

¹⁶⁵ Tsopano, koma, werengani tsopano ndime 3 ndi . . . kapena Chivumbulutso 3:2, miniti yokha. Tsopano, ine ndazilemba apa pa chifukwa china. Tsopano izi ziri, zikulowa mkati tsopano, m’badwo wa Chilutera, mu m’badwo wa okonzanso, wa Chivumbulutso 3:2.

¹⁶⁶ Chimene iwo anachita, iwo anapanga bungwe. Mwamsanga pamene Lutera anayambitsa mpingo wake, iwo anawupanga iwo bungwe. Chabwino, chinthu chomwecho chimene Wesile anachita. Chinthu chomwecho a Pentekosti anachita, chimodzimodzi, anawupanga bungwe iwo. Ndipo iwo akuchita chiyani? Iwo akutenga kachitidwe komweko kamene iwo atulukamo. Mukuwona?

¹⁶⁷ Tsopano yang’anani ichi, Chivumbulutso, kulankhula za mpingo wa Sarde uwu. “Kwa mngelo wa mpingo,” ndiyo ndime ya 1, zedi. Mukuwona? Chabwino.

Khala woyang’anira, ndipo limbikitsa zinthu zimene zatsalira, . . .

¹⁶⁸ Amenewo ali, “Mawu amene inu mwaphunzitsidwa,” mwawona, “zinthu zimene zatsalira.”

. . . zomwe ziri zokonzeka kufa: . . .

¹⁶⁹ Iye ali pomwepo wokonzeka kuyamba kubwerera mu bungwe basi monga mpingo wa Katolika kumene iye anatulukako. Mukuwona?

. . . pakuti Ine sindinapeze ntchito zako zangwiro pamaso pa Mulungu.

¹⁷⁰ Ndi zimenezotu. Apo pali . . . Apo iye akupita, mmbuyo momwe kachiwiri. Kodi inu simukuwona chifukwa chimene kachitidwe ka bungwe kali kolakwika? Anayambitsa iko ndi

ndani? Kodi anali Mulungu? Kodi anali atumwi? Mpingo wa Roma Katolika unachita izo. Tsopano mungomulola wazambiriyakale aliyense anene mosiyana. Si pamenepo. Iwo ali, iwo amati iwo ndiwo manthu mpingo, ndipo iwo ali. Koma iwo apanga bungwe chinthucho, ndi kuyika kachitidwe, ndi mutu wa munthu kwa icho. Ndipo ife sitinatenge munthu mmodzi, monga iwo anachitira; ife tikutenga gulu lonse la anthu, kuwayika iwo pamodzi, ndiyeno inu munakhala nako kusongonekera kwenikweni. Uko nkulondola. Gulu lingakhoze bwanji, mulimonse?

171 Ziri chabe monga, ife timaganiza kuti demokarase ndi yolondola. Ine ndikukhulupirira iyo ili, nanenso, koma iyo siyidzagwira bwino ntchito. Iyo siyingakhoze. Ndi gulu la ma Ricky pafupi apa kuti ayiyendetse iyo, mungakhoze chotani mdziko kuyipangitsa kukhala bwino? Inu simungakhoze. Zindikirani, chinthu chenicheni chinali mfumu yaumulungu.

172 Zindikirani Chamoyo, Chamoyo chachitatu, tsopano, chinali kukanika kwa munthu. Ndipo iye ankayimira okonzanso amene anatulukira.

173 Kuchokera ku fano, la kutenga, kunena, “*Uwu* ndi mkate.” [M’bale Branham awombetsa manja ake pamodzi kanai—Mkonzi.] “*Uyu* ndi vinyo.” [M’bale Branham awombetsa manja ake pamodzi kawiri.] Mukuwona, wotsutsakhristu akadali nacho chinachake chophiphiritsa Chikhristu. Iye ayenera kutero, chifukwa iye ali “wotsutsa,” inu mukuwona. Ndiyeno, ngati iye ayenera kukhala wotsutsa chinachake . . .

174 Tsopano, ngati iye abwera ponsepo, kunena, “O, ine ndine wa Buddha.” Chabwino, icho chiribe chochita chirichonse. Iwo onse amachita. Icho chiri chikunja chabe, kuyamba nkuyamba.

175 Koma wotsutsakhristu ali wokanika. Iye ali nayo mitundu ya zinthu zonse zimene zimayimira Chikhristu kumeneko. Kokha, wazitengera izo kumbali yina, chinachake chotsutsa Chiphunzitso chapachiyambi cha Izo. Mwawona, ndicho chimene chikumupangitsa iye kukhala wotsutsakhristu. Mukuwona?

176 Kotero, okonzanso, pamene Chamoyo chinatuluka mu mawonekedwe a—a munthu, kukamenyana nacho icho!

177 Tsopano, musati muyiwale ichi, kalasi! Musati muyiwale ichi! [M’bale Branham akugogoda pa guwa kanai—Mkonzi.] Mukuwona? Kumbukirani Izo, masiku onse a moyo wanu! Mukuwona? Zamoyo izi ziri zolondola. Izo ziri PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuwona?

Zindikirani, kupembedza mafano kunabweretsa . . .

178 Munthu Wachamoyo anatulukira ndi mphamvu ya Mulungu, mwa nzeru zimene Mulungu anamupatsa iye, ndipo

anawubweretsa Mpingo kuchoka ku kupembedza mafano, kubwerera kwa Mulungu. Koma mu. . .

179 Ife tikupeza, mu m'badwo womwewo wa mpingo, pamene iwo anayamba kupanga chipembedzo, kuchita chinthu chomwecho chimene iwo anachita pachiyambi, chimene Roma anachita, tsopano iye apanga ana aakazi kwa mpingo umenewo. Ndipo iye akuti chiyani?

180 Anati, "Tsopano pakuti uli. . .Ine sindinakupeze iwe wangwiwo. Ndipo iwe uyenera kulimbikitsa mphamvu pang'ono iyo yomwe iwe watsala nayo." Tsopano mverani kwa Iye akuwachenjeza iwo, mu Chivumbulutso kachiwiri, 3:3. Tiyeni titenge. . .Chabwino, ine ndikukhulupirira ndinatenga izo, maminiti pang'ono apitawo.

Kumbukira kuchokera momwe iwe unalandirira ndi kumva, ndipo gwira zolimba, ndi kulapa.

181 Basi, mwanjira yina, "Kumbukira kuti iwe unachokera mu chivundi chonga icho." Mukuwona? Ndipo yang'anani apa.

. . .Ngati chotero iwe sudzayang'ana, Ine ndidzabwera kwa iwe ngati mbala, (a-ha), ndipo iwe udzazindikira. . .ndipo iwe sudzadziwa ora lomwe Ine ndidzabwera pa iwe.

182 Mpaka mmusi, Iye adzasuntha choyikapo nyali, mwawona. Koteró, ndi zimenezo. Ndi chiyani icho? Kuwala kwa Mpingo.

183 Ndipo iye anapita mpaka mu kachitidwe komweko kabungwe la mdima wa chikunja kumene iye anatulukako, ndipo kumeneko iye watsalirabe lero, ndipo anthu-owona-mtima kumaganiza kuti ndicho Chowonadi, basi momwe aliri Akatolika. Ndipo Aprotestanti amawaseka Akatolika; pamene, iwo ali asanu ndi mmodzi kumodzi, ndi theka la dazeni kwinako, chimodzimodzi, molingana nawo Mawu. Nzeru za munthu!

184 Tsopano zindikirani. O, momwe ine ndikukokondera Izi! Mverani kwa Iye tsopano akuwachenjeza iwo. Tsopano, tsopano ife. . .Inu mwangwiwo mukuvomereza, mmodzi aliyense wa inu? Tsopano, ngati inu simukutero, mundilembere ine funso. Kutu, Zamoyo zimenezo ziri chimodzimodzi kuzindikiridwa mu m'badwo uliwonse, monga momwe Baibulo lawazindikira iwo apa. Ndizo chimodzimodzi zomwe izo zachita uko. Mbiriyakale imasonyeza zomwe iwo anachita. Ife tikuyang'ana pomwe apa ndi kuwona zomwe iwo achita.

185 Ndipo apa, Zamoyo izo, ine—ine—ine sindinkadziwa zimenezo poyamba. Ine ndinali kungokhala pamenepo. Ine ndimakhoza kungoziwona izo zikuyenda pamenepo, basi momwe inu mukuyang'anira pa ine. Mukuwona? Ndipo izo ziyenera kukhala zolondola, chifukwa ziri pomwe apa ndi Baibulo. Koteró inu muchita bwanji china chirichonse kupatula kunena kuti izo nzolondola? Zindikirani.

186 Tsopano, Chamoyo chachinai, chimene chinatumizidwa kukamenyana naye wotsutsakhristu, mu Chamoyo chotsiriza ichi. Kodi inu mwakonzeka? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chamoyo chotsiriza chimene chinatumizidwa, kapena mphamvu yotsiriza kuti ikamenyane naye wotsutsakhristu amene anali kutsutsa Kuphunzitsa kwa Mulungu, wotsutsakhristu, inali mphungu. Mukuwona? Cholengedwa chamoyo chachinai chinali mphungu. Tsopano, inu mwaphunzira kumene mibadwo, kuwerenga Malemba. Ndi mphungu! Ndipo mu Baibulo, m’badwo wotsiriza unali m’badwo wa mphungu. Ndipo Mulungu amafanizira mphungu kwa aneneri Ake. Mukuwona? Izo. . . Tsopano yang’anani. M’badwo wotsiriza, m’badwo wa mphungu, m—muuluri wa Mawu owona. Mwawona?

187 Mulungu asanasunthe kuti achite, monga Iye anachitira mmasiku a Nowa, Iye anatumiza mphungu. Pamene Iye anabweretsa Israeli, ndipo ankhondo a Farao anali okonzeka kupita, Iye anatumiza mphungu. Nthawi zonse, Iye amatumiza mphungu potsirizira, mapeto a icho.

188 Ndipo apa Iye akutumiza mphungu, apanso. Ndicho chimodzimodzi ndi Mawu. Kotero inu mungachipange bwanji icho kukhala chinachake? Amatumiza mphungu, (chifukwa?) muuluri wa Chowonadi chomwe chakhala chikugwa konse kupyola mu m’badwo.

189 Kotero ingakhoze motani mu dziko n—ng’ombe, kapena—kapena munthu, kapena Chamoyo chirichonse chimene anali kukwera, chingawululidwe bwanji icho mpaka mphungu itabwera? Iwo anali nawo malo awo; iwo anali aumulungu, Zamoyo zotumidwa, basi ngati momwe wina aliyense anali.

190 Mkango, umenewo unali chiyambi. Apo pali pamene wotsutsakhristu akutulukira mu—mu kumenyana.

191 Ndiye iye anadzutsa mphamvu yina; Iye anatumiza mphamvu kukakumana nacho icho.

192 Ndiye iye anadzutsa mphamvu yina; Iye anatumiza mphamvu yina kukakumana nacho icho.

193 Ndiyeno pa mphamvu yotsiriza, Iye akubwereta pansu mphungu, “Kuti ibwezeretse ana kubwerera ku Chikhulupiriro chapachiyambi kachiwiri, cha atate awo.” M’badwo wa mphungu! Ndiye, inu mwazindikira, kulibenso Zamoyo. Ndizo zonse za izo. Amenewo ali mapeto. Tsopano, ngati inu mungatenge tsopano Chivumbulutso 10:1, 7. Ine ndakhala ndikulozera kwa iwo. Kumbukirani, mu m’badwo wa mtumiki wotsiriza, mwawona, chimene chimayenera kudzachitika? “Zinsinsi zonse za Mulungu zikanadzawululidwa.” Mphungu! Ameni!

194 Tsopano inu mukuwona zamoyo zinai zimene zinakwera. Izo zinali zolondola mwangwiro. Kodi inu mukukhulupirira

izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo tsopano apa pali m’badwo uliwonse, kapena mphamvu iliyonse imene imakwera pambuyo pa iwo. Ndipo pamenepo pali Lemba limene likusonyeza chimene mdani wokwerayo anachita. Zimenezo zawululidwa mu Zisindikizo izi. Ndiponso zawululidwa tsopano kuti Chamoyo chirichonse, mphamvu imene Mulungu anayitumiza, kukamenyana naye iye, zinagunda chimodzimidzi pa dontho, mpaka ku nthawi ya mphungu. Tsopano, ngati iyi ili nthawi yotsiriza, kudzabwera mphungu, kulondola, ndipo kwa iyo. Tsopano, kumbukirani.

¹⁹⁵ Tsopano, mu masiku amene mkango uwo unabwera, Mawu apachiyambi, pafupi mmodzi mu zana-limodzi la iwo anamvetsera kwa mkango.

¹⁹⁶ Mu masiku amene n—ng’ombe inabwera, kadontho kakang’ono chabe ka iwo anamvetsera ku uthenga wa ng’ombe.

¹⁹⁷ Mu masiku amene m—munthu anabwera, iye anagwira ntchito pakati pa anthu, inu mukuwona, kotero Iye anali wothyathyalika. Iye anatulutsa kagulu kakag’ono.

¹⁹⁸ Ndipo anachita chiyani iwo? Satana anawona izo, kotero iye anangowatumiza iwo mmbuyo kumene ndi kuwakwatitsa iwo mu icho.

¹⁹⁹ Ndipo kumbukirani, pamene mphungu ikubwera potsiriza, iwo adzakhala mmodzi pa gawo limodzi la zana amene adzamvetsera. Iwo ndi m’badwo wa mphungu. Kumbukirani, ndi okwera ena onsewa. . . Ndiyeno ngakhale Yesu ananeneratu, “Ngati Iye akanapanda kufulumizitsa Kudza Kwake, sipakanakhala mnofu uliwonse, nkomwe, ukanapulumsidwira Mkwatulo.” . . .? . . . Kodi ndi Lemba limenelo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mukuwona pamene ife tiri ndiye, sichoncho inu, m’bale ndi mlongo? [“Ameni.”] Mukuwona pamene ife tiri?

²⁰⁰ Mulungu, ine ndiri wokondwa kwambiri, ine—ine—ine sindikudziwa choti nkuchita! Uyu si ine chabe kuyimirira pano ku—kuti ndilankhule. Ine ndiri pano, nanenso. Ine, ine ndiri pakati pa inu. Mukuwona, ine, Ndi ine. Ine ndiri nalo banja. Ndipo ine ndiri nawo abale ndi alongo amene ine ndimawakonda. Ndipo Mulungu wa Kumwamba, wachifundo mokwanira kubwera pansu ndi—ndi kuwulula chinthu icho, mwa Iye mwini, mwa masomphenya amene atsimikizidwa kwa zaka makumi atatu, ndi Chowonadi. Ife tiri pano. Ife tiri. . . Ife tafika. Ndizo zonse. Kufufuza kwa sayansi kwatsimikizira Izo. Kuvomerezera kwa Mawu kwatsimikizira Izo. Ndipo ife tiri pano! Ndipo Vumbulutso ili likuchokera kwa Mulungu, ndipo Ilo liri Chowonadi!

²⁰¹ Kodi inu mwagwirapo china chake? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ine ndimangodabwa ngati inu munatero. Mukuwona? Inde, bwana. Ine mwina sindisowa kukuwuzani

inu ndiye, Lamlungu. Zindikirani. Zindikirani. Zodabwitsa! Tsopano, tsopano, zindikirani tsopano.

202 Ndiyeno molingana nayo—nthawi imene Mulungu anali kukawombola dziko la chikugumula, Iye anatumiza mphungu.

Ndipo nthawi yomwe Iye anali kukawombola Israeli, Iye anatumiza mphungu.

203 Kodi inu mukukhulupirira kuti nthawi, ngakhale kwa Yohane, pa Chisumbu cha Patmo, Uthenga uwu unali wangwiro kwambiri kotu Iye sakanakhoza kuwudalira Iwo kwa Mngelo? Inu mukudziwa, mngelo ndi mtumiki. Koma kodi inu mukudziwa kuti mtumiki anali mneneri? Inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Tiyeni titsimikizire izo. Chivumbulutso 22, tiyeni tiwone ngati iyo inali mphungu. Eya. Mwawona, iye anali... Ndithudi, iye anali mngelo, iye ndi mtumiki, koma uyo anali mneneri amene anawulula Bukhu lonse ili la Chivumbulutso kwa iye.

204 Chivumbulutso, mutu wa 22 ndipo ndime ya 19, ine ndikukhulupirira izo nzolondola ngati ine ndazilemba apa... 22:19, ine ndikhoza kulakwitsa. Ayi. [Winawake akuti, “Ndi 22:9, mwinawake.”—Mkonzi.] 22:9, ndicho chimene icho chiri. Ine ndinali kuyang’ana pa 22:9. Uko nkulondola. O, inde, apa.

Ndiye ananena iye kwa ine, Ona iwe usachite icho ayi: pakuti ine ndine wa antchito amzako, ndi wa abale ako aneneri, . . .

205 Yang’anani chimene Yohane anawona apa.

. . . Ine Yohane ndinawona zinthu izi, ndi kuzimva izo.

206 Tsopano iye akutsekera. Uwu ndi mutu wotsiriza.

. . . Ndipo pamene ine . . . ndinamva ndi kuwona, ine ndinagwa pansu kuti ndipembedze pa mapazi a mngelo yemwe anandiwonetsa zinthu izi, yemwe anandiwonetsa ine zinthu izi.

207 Ndipo, “iye,” ndiye, “mngelo,” mukuwona.

Ndiye ananena iye kwa ine, Ona kuti iwe usachite icho ayi: . . .

208 Palibe mneneri woona amene akanapembedzedwa, kapena mtumiki wamtundu uliwonse, mwawona. Izo ziri za kwa Mulungu yekha.

Ndiye ananena iye kwa ine, Ona kuti iwe usachite icho ayi: pakuti ine ndine wantchito mzako, ndi wa abale ako aneneri, ndi wa iwo amene asunga zonena za buku ili: pembedza Mulungu.

209 Mukuwona? Tsopano, Bukhulo linali lofunikira kwambiri, mwakuti, Ilo liri Mawu a Mulungu. Tsopano yang’anani. Ndipo pamene Mawu a Mulungu abweretsedwa, Iwo ayenera

kubweretsedwa ndi mneneri, chifukwa ali yemwe Mawu a Mulungu amafikirako.

210 Ine ndimayembekezera kupeza funso pa izo, mu—mu bokosi ili apa. Ine ndimaganiza ine ndidzangowatsimikizira iwo kwa ilo, pang’ono pokha, inu mukudziwa. Ine ndikungomverera lirimo limodzi mmenemo monga limenelo, ndizo zonse. Ine—ine ndimangoganiza ine ndikanadzafika kwa ilo, inu mukuwona. Mwawona?

211 Mawu aliwonse a Mulungu amabweretsedwa. Baibulo silimasintha kachitidwe, ayi konse, mukuwona. Ndi chinthu chomwecho. Iwo ayenera kubwera kwa mpenyi uyu yemwe ife tikumuyembekezera kuti afike, tsopano zindikirani, Chivumbulutso 10:1, 7.

212 Tsopano tiyeni tiwerenge—ndime ya 9 kachiwiri. Tsopano ife titenge . . . ife . . . Tsopano, tisanafike ife ku ndime imeneyo, ine ndikufuna kukufunsani inu chinachake.

213 Kodi inu mukuwona, mwangwiwo, ife tisanasiye Zisindikizo izi? Tsopano kumbukirani, palibenso mphamvu zomwe zikutulukira itachoka mphungu iyo, mukuwona, palibe inanso. Nthawi iliyonse wotsutsakhristu ankatumiza chinachake, Mulungu amatumiza mphamvu. Wotsutsakhristu amatumiza mphamvu yina; Mulungu amatumiza chinachake kukamenyana nacho icho. Ndiye iye amatumizanso mphamvu yina; Mulungu amatumiza chinachake kukamenyana nacho icho. Mukuwona? Ndiyeno pamene Iye anakafika mpaka kwa mphungu, amenewo anali Mawu Ake, kubwerera monga Iwo analiri mu malo oyamba.

214 Tsopano yang’anani. Kodi sali mneneri yemwe ife tikumuyembekezera kuti abwere, munthu wina wodzozedwa nawo—nawo Mzimu wonga wa Eliya? Iye sadzakhala Eliya, zedi. Koma iye adzakhala munthu, monga choncho, adzabwera pansi. Ndipo utumiki wake womwe uli wodzatumiza, kuti abwezeretse, kwa anthu akugwa awa kupyolera mu zopotoka zachipembedzo izi, kubwerera ku Chikhulupiriro chapachiyambi cha atate. Tsopano, ngati icho sichikumangiriza Baibulo ilo palimodzi, ine—ine sindikudziwa chimene chikutero. Ine—ine sindinganenense zochuluka za icho, chifukwa ndi chimenecho. Inu mwafika basi. Ndicho Chowonadi. Inu mukachotsapo chirichonse pamenepo, inu muchipotoza icho. Mwawona? Koteri, izo, ziri kungoyenera kukhala mwanjira iyo.

215 Tsopano zindikirani, tsopano, mu ndime ya 9, “Miyoyo pansi pa guwa.” Tsopano, apa pali pamene ine nditi ndipeze kusagwirizana kwenikweni kwina. Koma mung’oyang’ana miniti yokha. Ndipo basi . . . Mukuwona? Ine ndinkaganiza izo, nanenso, koma izo sizinabwere mwanjira iyo. Ife takhala . . . ine ndakhala nthawizonse ndikuganiza kuti miyoyo iyi pansi pa guwa anali o—o—ofera a Mpingo woyambirira. Ndipo ine

ndikutsimikiza kuti Dr. Uriah Smith, ndi aliyense wa iwo, amati iwo ali. Mukuwona? Koma, ine ndinkaganiza choncho, inemwini. Koma pamene Mzimu Woyera unawonetsa masomphenya a icho, icho sichinali; iyo sindiyo miyoyo.

Tsopano, tsopano inu mukuti, “Chabwino, tsopano, ine sindikudziwa za izo.”

²¹⁶ Chabwino, tsopano, miniti yokha, ife tizipeza. Yang’anani. Iyi siyiri miyoyo ya—ya Mpingo wa Mkwatibwi, ayi konse. Ife tinkaganiza kuti umenewo unali Mpingo wa Mkwatibwi ukuyembekezera uko, miyoyo pansi pa guwa, inu mukuwona, ikulira, “Mpaka liti, Ambuye, mpaka liti?” Ndiroleni ine ndiwerenge izo kachiwiri tsopano, kotero ife tizitenge izo molondola.

Ndipo pamene iye anali atatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona pansi pa guwa miyoyo ya iwo amene anaphedwa chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene iwo anagwirizira:

²¹⁷ Mwaona, “Mawu a Mulungu, ndi umboni umene iwo anagwirizira.” Tsopano, musati—musati musunthe kuchoka pamenepo. Miniti yokha, mukuwona.

Ndipo iwo analira...Mpakana liti,...Ambuye, mpakana liti?... (Mukuwona?)...woyera ndi wowona, muchite inu...kuweruza ndi kubwezera magazi athu pa iwo amene akukhala pa dziko lapansi?

Ndipo miinjiro yoyera inapatsidwa kwa aliyense wa iwo; ndipo kunanenedwa kwa iwo, kuti apumulebe kwa kanthawi pang’ono, mpaka antchito amzawo nawonso ndi—ndi... abale, amene ayenera kuphedwa monga iwo anali, ayenera kukwaniritsidwa.

²¹⁸ Tsopano, pakuti iwo, pa nthawi iyi, ngati inu mungazindikire, Chisindikizo Chachisanu ichi kukhala chikutsegulidwa, onani, Mpingo wapita. Iyo siyingakhale chabe, miyoyo yapansi m—Mpingo woyambirira.

²¹⁹ Tsopano, tsopano, chonde, ngati inu munachitapo perekani tcheru kwa ichi tsopano, chifukwa ichi chiri chitsutsano chachikulu...chitsutsano, kotero ine ndikufuna inu mumvetsera mwatcheru kwenikweni tsopano. Ndipo inu muli nawo mapepala anu, ndi zinthu zoti mulembe nazo. Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire.

²²⁰ Tsopano, iyi siyingakhale miyoyo iyo. Chifukwa, m—miyoyo ya o—olungama, ophedwa, ndipo anthu olungama, Mpingo, Mkwatibwi, watengedwera kale mmwamba, kotero iwo sakanakhala pansi pa guwa. Iwo akanakhala mu Ulemerero, ndi Mkwatibwi. Tsopano yang’anani. Pakuti, iwo apita mu Mkwatulo, mu mutu wa 4 wa Chivumbulutso. Iwo anatengedwera mmwamba.

221 Tsopano, ndi ndani miyoyo imeneyi, ndiye? Ndicho chinthu chotsatira. Iwo ndi ndani, ndiye, ngati iwo sali Mpingo woyambirira? Uyu ndi Israeli amene ati adzapulumutsidwe monga fuko, onse awo amene anakonzedweratu. Ndiye Israeli. Ndiye Israeli, iyeyekha.

222 Inu mukuti, “O, dikirani miniti.” Inu mukuti, “Iwo sangakhale.” O, inde, iwo ali woti adzapulumutsidwe.

223 Apa, tiyeni tichikhazikitse icho, miniti chabe. Ine ndiri nawo Malemba anai kapena asanu. Ine nditenga limodzi. Tiyeni titenge Aroma, miniti yokha, ndipo tipeze ngati iwo ali. Tiyeni titenge Bukhu la Aroma, ndipo tipite ku—ku mutu wa 11 wa Aroma, ndipo ife tizipeza. Basi...Tiyeni tingowerenga pamenepo, ndiyeno ife tidzipezera tokha izo. Aroma, mutu wa 11, ndime ya 25 ndi ya 26. Tsopano mverani kwa Paulo apa.

224 Ndipo Paulo anati, “Ngati wina aliyense, ngakhale Mngelo, akalalikira uthenga wina uliwonse,” (chiyani?) “iye anali woti akhale wotembereredwa.” Yang’anani.

Pakuti ine sindikanafuna, abale, kuti inu mukhale osadziwa za chinsinsi (aha!), kuti mungadziyese anzeru mwa kudzinzyenga kwanu (ndi zimenezotu); kuchita khungu mwa gawo kwachitika kwa Israeli, mpaka kukwaniritsika, chidzalo cha Amitundu chitabweramo.

225 Mkwatibwi wotsiriza wa Amitundu akhale atabweretsedwa mkati, pakuti Mkwatibwi, kuchita khungu wabwera kwa Israeli kwa chifukwa pa chimenecho.

Ndipo kotero Israeli yense adzapulumutsidwa: monga kunalembedwa, Kudzabwera kuchokera mu Zioni Wowombola, ndipo adzachotsa zosakhala zaumulungu kwa Yakobo:

226 Kulondola! Tsopano, iwo ali Aisraeli, amene ali pansi pa guwa ili. Yang’anani. Israeli anachititsidwa khungu kwa cholinga chomwecho kuti ife tipulumutsidwe. Inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano, ndani anawachititsa khungu iwo? Mulungu. Mulungu anachititsa khungu ana Ake Omwe.

227 Nzosadabwitsa Yesu, akuyimirira pamenepo pa mtanda, ndipo iwo Ayuda kulirira Magazi Ake! Awo anali ana Ake Omwe. Ndipo Iye anali Lemba. Iye anali, Iyemwini, Mawu. Ndipo apa, Iye podziwa kuti anthu amenewo akanadzamulandira Iye mosekera! Ndipo ndicho chifukwa Iye anawachititsa khungu iwo, kotero kuti iwo asamuzindikire Iye. Iye anabwera mwa njira yophweka choncho, ndi kuwachititsa khungu iwo kwa icho, kuti iwo asachilandire icho. Mukuwona? Lemba linati iwo akanadzachita izo. Ndipo Iye anawachititsa khungu. Anachititsidwa khungu! Yesu anawamvera chisoni iwo, ngakhale mochulukwa kwambiri, pamene Iye anati, “Atate, akhululukireni iwo. Iwo sakudziwa chimene iwo akuchichita.”

Mukuwona? Iwo anachita khungu. Paulo anati iwo anachita khungu kwa cholinga, chifukwa cha ife.

228 Zindikirani. Tsopano ine ndikufuna inu muyang'ane izi mwatcheru kwenikweni. “Iwo anapatsidwa miinjiro.” Iwo anali alibe iyo. Iwo anapatsidwa miinjiro, miinjiro yoyera, aliyense wa iwo. Tsopano, oyera tsopano ali nayo, alinawo kale; iwo akuwupeza iwo kuno. Koma, uko, “Iwo anapatsidwa miinjiro.” Ndipo oyera anali nayo kale yawo, ndipo atapita kale. Mukuwona? Mukuwona? Iwo anali—anali osati. . .

229 Iwo, onani, iwo analibe mwayi, chifukwa iwo anachititsidwa khungu ndi Mulungu, Atate wawo yemwe; kotero kuti chisomo cha Mulungu chikanakhoza kukwaniritsidwa, kotero Mkwatibwi akanakhoza kutengedwa kuchokera mwa Amitundu. Nkulondola uko? [Osonkhana ati “Ameni.”—Mkonzi.]

230 Ndiroleni—ndiroleni ine ndikuwonetseni inu choyimira chokongola apa mwa Yosefe; Yosefe, munthu wa Mzimu, mphungu. Iye anabadwa pakati pa abale ake, basi monga Mpingo uli pakati pa yina. Ndipo iye amakhoza kumasulira maloto ndi kuwona masomphenya. Ndipo ena onse a iwo ankamuda iye. Abambo ake ankamukonda iye.

231 Zindikirani, ndiye, iye anali kunja, anatulutsidwa ndi abale ake, osati ndi abambo ake. Kutulutsidwa, ndi abale ake, ndipo anagulitsidwa kwa pafupi zidutswa zitatu za siliva. Kuponyedwa mu dzenje, ndipo ganiziridwa kuti anali wakufa.

232 Kutulutsidwako, ndi kuyikidwa ku dzanja lamanja la Farao. Ndipo chifukwa iye anatulutsidwa ndi abale ake, onani, iye anapatsidwa mkwatibwi Wamitundu, osati wa anthu ake omwe. Kupyolera pamenepo, iye anabala Efraimu ndi Manase, omwe anawonjezedwa kwa Israeli.

233 Pamene Israeli ankawadalitsa iwo, pa kupingatsitsa manja ake, kuchokera kwa wamng'ono kupita kwa wamkulu, kupingasitsa madalitso kuchokera kwa Ayuda, kubwerera. . . kapena kuchokera kwa Ayuda kupita kwa Amitundu. Mukuwona? Anapingatsitsa manja ake, kwa mwana wamng'ono, umene uli Mpingo wawung'ono woti udzabweremo. “M—mayi mpingo anayima mu dzuwa; iye anabala mwana uyu.” Ndipo zindikirani, kuti amutenge iye, Israeli anapingatsitsa manja ake, moyimira. Ndipo Yosefe. . .

Iwo ana omwewo, anali a mayi Wamitundu.

234 Mkwatibwi wa Israeli, mmbuyo umo, anapingasitsidwa, kuchokera ku Orthodox yakale, kupita ku njira ya Chikhristu, mwa Mzimu Woyera umene unapingasitsa manja a Israeli. Iye anati, “Mulungu wapingasitsa manja anga.” Iye analibe kanthu koti achite nacho icho.

²³⁵ Zindikirani. Ndiye, Yosefe, atakanidwa ndi abale ake omwe, anthu ake omwe, anatenga mkwatibwi Wamitundu. Chimodzimodzi basi chimene Yesu anachita; atakanidwa ndi Ayuda, anatenga Mkwatibwi Wamitundu.

²³⁶ Tsopano tiyeni tiwerenge chinachake apa. Ine ndiri nalo Lemba ndalilembaapa, Machitidwe 15. Ndipo, o, izi ziri chabe mtundu wa basi zomwe ife tiyenera kuphunzitsa, mulimonse. Tsopano, ine ndikukhulupirira ndiri napo apa molondola, tiwerenge Machitidwe 15:14. Chabwino. Ine ndikuyembekeza izi ziri zolondola tsopano. Chabwino. “Simioni wafotokoza momwe Mulungu . . .” Ayi, tiyeni tiyambire pa ndime ya 13.

Ndipo atatha iwo kukhala chete, Yakobo anayankha, . . .

²³⁷ Tsopano, inu mukuwona, chimene chinali chitachitika, iwo anali atapita kwa Amitundu. Mukuwona? Ndipo mkangano unalipo, chifukwa iwo anali Ayuda. Mukuwona?

Ndipo atatha iwo kukhala chete, Yakobo anayankha, nati, Amuna ndi abale, mverani kwa ine:

Simioni (ameneyo ndi Simoni Petro) wafotokoza momwe Mulungu poyamba anachezera Amitundu, kuti atenge kuchokera mwa iwo anthu kwa dzina lake.

²³⁸ Aha! Mukuwona, dzina la mkazi wanga linali Broy. Pamene ine ndinamutenga iye, iye anali Branham. Mukuwona?

²³⁹ Yesu akuwutulutsa Mpingo Wake, kapena Mkwatibwi Wake, kuchokera mwa Amitundu. Ndilo Lemba, atayimiridwa, monga momwe Yosefe analiri.

²⁴⁰ Tsopano zindikirani izi, tsopano, miyoyo iyi pansi pa guwa. Chabwino, a . . . iyi, “Miyoyo iyi,” kumvetsa tsopano, “ndiwo amene ali pansi pa guwa,” chifukwa chomwe iwo anaphedwera ndi anthu ochimwa monga Eichmann. Mwawona? Iwo akuyembekezerabe, mamilioni a iwo, mukuwona, koma iwo adakali Ayuda.

²⁴¹ Tsopano, kumbukirani. Chinali chiyani icho? “Iwo anaphedwa chifukwa cha Mawu a Mulungu,” osati chifukwa cha umboni wa Khristu. Kodi inu munamvetsa izo?

²⁴² Koma, kumbukirani, Mpingo ukubweramo, nawonso, ofera a Mpingo, anali chifukwa cha Mawu a Mulungu ndi umboni wa Yesu Khristu. Ndi angati akudziwa izo, apa pa . . . [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Eya. Chabwino.

²⁴³ Tsopano, koma awa analibe umboni wa Yesu Khristu.

. . . chifukwa cha Mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene iwo anagwira:

²⁴⁴ Ayuda! Ndipo Hitler ankawada iwo, choteronso Eichmann, choteronso Stalin, ena onse a mdziko. Mukuwona? Koma

iwo anakhala owona kwa chimene iwo anakhulupirira. Ndipo anawapha iwo chifukwa iwowo anali Ayuda.

²⁴⁵ Kodi inu mukudziwa kuti Marteni Lutera akukhala ngati anali nalo lingaliro lomwelo, nayenso? Izo nzowona. Iye anati, “Ayuda onse anayenera kutulutsidwa. Iwo ali otsutsakhristu.” Mukuwona? Koma iye anali chabe pansi pa nyengo yina, ndipo sanachiwone icho, sanawawone Mawu.

²⁴⁶ Tsopano Mawu, Chowonadi, chikubwerapo. Inu mumuchititsa khungu chotani Israeli nkomwe? Inu simungakhoze kuchita izo. Ayi.

²⁴⁷ O, mneneri ameneyo akanakhoza kuyima bwanji pamenepo, tsiku lija, ndi kunena, “Iwe ukuwoneka ngati chipembere, Israeli?” Pamene iwo anali kuyesetsa kumusonyeza iye mbali zoyipisitsa za iye! Iye anati, “Bwanji,” iye anati, “aliyense amene ati adzadalitse iwe adzadalitsidwa, ndipo aliyense ati adzatemberere iwe adzatembereredwa.” Uko nkulondola. O, munthu! Inu mudzachita motani icho?

²⁴⁸ Nthawi imodzi iwo ankakaganiza kuti Mulungu akanayiwala, pamene mneneri anawona chinthu chakuda icho chikubwerera Ayuda. Munthu ameneyo atayimirira pamenepo, ndipo Mawu a Mulungu akutsanuliridwa kwa iye. Iye anati, “O Ambuye, kodi Inu muwataya anthu Anu?”

Iye anati, “Nchiyani icho chagona pambali pako?”

Iye akuti, “Ndodo yoyezera.”

²⁴⁹ Anati “Kumwamba nkotalika chotani? Tayeza iko.” A-nha. “Nyanja ndi yakuya chotani?”

Iye anati, “Ine sindingakhoze kuchita izo.”

²⁵⁰ Iye anati, “Ngakhale ine sindingakhoze, ngakhalenso Ine sindingakhoze kuyiwala Israeli.” Ayi, bwana. Iye sikuti amuyiwala iye.

²⁵¹ Iye anachita kuchititsa khungu mwana Wake Yemwe. Tsopano, ganizani za izo. Kuchititsa khungu mwana Wake Yemwe, kuti atipatse ife mwayi, ndipo ife tikuwukankhira Iwo pansi. Tsopano, kodi izo sizikukupangani inu kumverera pafupi wamng’ono kwambiri mwakuti inu mukhoza kukwawira pansi pa chimwala cha konkire mutavala chipewa cholemera magaloni khumi, ndipo nkusachikhudza icho? Ndiko kuchepa kwambiri, inu mukudziwa. O, mai! Inde.

²⁵² “Iwo anagwiritsa chifukwa cha Mawu a Mulungu.” Iwo anali Ayuda. Iwo anali nalo Lamulo lawo; iwo anakhala nalo ilo. Mukukumbukira usiku watha, tsopano? Mukuwona? Iwo anakhala nalo ilo. Ndipo iwo anali Ayuda, ndipo iwo anali nalo lamulo. Ndipo lamulo linali Mawu a Mulungu, ndipo iwo anakhala molondola nalo ilo. Uko nkulondola. “Ndipo chifukwa cha umboni umene iwo anagwira, iwo anaphedwa.” Ndipo apa panali miyoyo pansi pa guwa, utatha Mpingo kupita kale.

253 Tsopano yang'anani. Iwo anali, mu khungu lawo, anapha Mesiya wawo, ndipo tsopano iwo anali kukolola chifukwa cha zimenezo. Iwo anazindikira icho. Iwo anazindikira icho, izo zitapita kale. Iwo anamuwona Iye ndiye, pamene iwo anabwera patsogolo pa guwa la Mulungu. Koma tsopano chisomo cha Mulungu chiri kwa iwo.

254 Yang'anani. Tsopano, iwo sakanakhoza, mwanjira iliyonse, kukhala oyera, chifukwa iwo anavekedwa kale mwinjiro. Koma apa iwo ali tsopano, basi “miyoyo pansu pa guwa, chifukwa cha Mawu a Mulungu, ndi umboni umene iwo anagwira,” kuti akhale anthu a Mulungu, Ayuda.

255 Koma tsopano, yang'anani, chisomo cha Mulungu chikubwera kwa iwo. Ndipo Yesu akuwapatsa iwo, mmodzi aliyense, mwinjiro woyera, (o, mai, yang'anani; kutsidya uko, utatha Mpingo kupita), chifukwa iwo anali omvera kwa cholinga chawo. Ndipo iwo anachititsidwa khungu, ndipo iwo sanadziwe icho. Iwo sanadziwe icho. Iwo anali kusewera chimodzimodzi gawo limene Mulungu anali atalikonzza kuti iwo akasewere. Ndipo apa, apa, Yohane akuyang'ana uko ndipo akuwona miyoyo pansu pa guwa. Tsopano yang'anani, iye akuwona miyoyo imeneyo. Yang'anani chimene iye akuwatacha iwo.

Iwo akulira, “Ambuye, mpakana liti?”

Yang'anani, “Kanthawi kotalika pang'ono chabe.” Mukuwona?

256 Tiyeni titenge icho, pamene ife tikupita mmusi, mpaka kupyola mu Lemba tsopano. Iwo akuzindikira kuti iwo anali atamupha Mesiya wawo. Mukuwona? Ndipo iwo sanali kudziwa icho, koma ndiye iwo anazindikira. Iwo anapeza—iwo anaphedwa, kubwezera, kuti alipirire izo, pamenepo kuchita cholakwika. Ndipo tsopano yang'anani chinthu chimene iwo amayenera kuchita! Mukuwona, iwo anali olakwa pakupha, kotero iwo anaphedwa. Mukuwona? Iwo Anafuwula, “Magazi Ake akhale pa ife!” Mukuwona? Uko nkulondola. Ndipo iwo anachititsidwa khungu.

257 Tsopano, ngati iwo akadapanda kuchititsidwa khungu; Mulungu anati, “Asiyeni iwo okha. Iwo sali oyenera.” Koma pokhala kuti iwo anachititsidwa khungu ndi Mulungu, chisomo Chake chinafikira pansu kwa iwo. Amen! Kulankhula za chisomo chodabwitsa! Ndi kumupatsa mmodzi aliyense wa iwo mwinjiro, chifukwa Israeli yense adzapulumutsidwa, mmodzi aliyense ali nalo dzina lake lolembedwa. Uko nkulondola. Yesu akuwapatsa iwo miinjiro.

258 Monga Yosefe anachitira kwa abale ake; choyimira. Penyani, pamene Yosefe anayimirira pamenepo, ndipo pamene iye potsiriza...Iye anadzizindikiritsa yekha pamenepo pa guwa, guwa lake lomwe, mu nyumbayachifumu yake, mpandowachifumu wake. Iye anati, “Aliyense andichokere ine.”

Mkazi wake anali mu nyumbayamfumu; kumene Mkwatibwi adzakakhale.

259 Ndipo iye anati kwa iwo, iye anati, “Kodi inu simukundidziwa ine?” Heyi, iye akulankhula Chihebri tsopano. “Ine ndine m’bale wanu, Yosefe.” O, mai!

Iwo anati, “Tsopano, o, iwe utipezeketsa ife.”

260 Anati, “Dikirani miniti. Dikirani miniti. Mulungu anachita izo kwa cholinga. Chinatengera inu kundiponya ine kunja, polinga kuti ndipulumutse moyo.” Ulemerero! Ndi zimenezotu, chimodzimidzi. Anati, “Musati, musati mudzikwiyire nokha.” Mukukumbukira Yosefe ananena izo? Anati, “Musati mudzikwiyire nokha. Zonse ziri bwino tsopano. Zonse izo zatha. Mulungu ananditumiza ine kuno, patsogolo pa inu.”

261 Inu mukudziwa, Baibulo linati iwo adzanena kwa Iye, pamene iwo amuwona Iye akubwera, anati, “Nnena, Ndinu Mesiya, ife tikudziwa. Koma, koma, nanga bwanji mabala awo?” Mukuwona?

262 Iye anati, “O, Ine ndinawatenga iwo m’nyumba ya abwenzi Anga.” Amzanga?

263 Ndiyeno pamene iwo ati adzazindikire izo, iwo amene atsalira, Zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, Baibulo linanena kuti iwo adzadzapatula, nyumba imodzi kwa yina. Ndi kutenga masiku, kuti alire basi, ndi kubuma, ndi kumayendayenda pansu; kumati, “Tinachita bwanji ife izo? Tinachita bwanji ife izo? Bwanji, ife tinamupachika Mesiya wathu yemwe.” Anati, kulira monga mmene nyumba ikanachitira chifukwa cha mwana wawo yekhayo, “Tinachita bwanji ife izo?”

264 Ayuda amenewo, ndiwo—ndiwo anthu achipembedzo kwambiri mu dziko; osankhidwa a Mulungu. Koma Iye anawachititsa iwo khungu, kuti atitenge ife, ndipo ife tinachikana Ichu. Chiweruzo cha mpingo wa Amitundu nchiyani! Ndi zimenezotu. Mukuwona? Kuchititsidwa khungu mwacholinga, ndi Mulungu, kotero kuti Iye akanakhoza kutitenga ife, Mkwatibwi wa Yesu. Kuwatenga iwo kuchokera... Mukuwona? Ndipo kuchifanizitsiratu icho, ndi chirichonse.

265 Tsopano inu mukuwona amene miyoyo ali? Iwo sindiwo oyera ophedwa. Awo apita kale. Uko nkulondola. Zindikirani, iwo anali, iwo anali atapita kale. Mukuwona?

266 Kotero, awa akupatsidwa miinjiro, mmodzi aliyense wa iwo. Ndipo tsopano ine ndikufuna inu kuti muzindikire. Koma tsopano chisomo cha Mulungu chikutsikira kwa iwo. Yesu akuwapatsa iwo aliyense mwinjiro woyera, monga Yosefe anachita, chisomo chake kwa abale ake.

²⁶⁷ Tsopano yang'anani. Ngakhale iwo anayesera kumuchotsa Yosefe, nayenso, koma chisomo chake chinafikira kumene kwa iwo. Mukuwona? "O, ziri bwino zonse. Izo ziri bwino. Inu simunatanthawuze kuchita izo. Koma, onani, ameneyo anali Mulungu akuchita izo. Mukuwona? Mulungu anakulolani inu nonse kuchita izo kotero kuti Iye akhoze kundithamangitsira ine kunja, ndi kundibweretsa ine kumusi kuno kotero kuti ine ndikakhoze kupulumutsa miyoyo ya anthu, Amitundu awa apa, kumene ine ndinapeza mkazi wanga. Ine sindikanakhala naye mkazi ayi ngati—ngati ine ndikanatsalira ndiri komweko. Tsopano, ine ndikumukonda mkazi wanga. Iye wandibalira ine ana awa apa." Ndipo anati, "Ine—ine... Ndipo tsopano—tsopano ine ndikubwera kudzakutengani inu nonse. Tsopano inu nonse mukhala nacho icho bwino, inunso. Ine ndikubweretsani inu komwe kuno. Ife tonse tizidzakhala limodzi, monga banja limodzi lalikulu." Mukuwona? Mukuwona? Mukuwona? Anati, "Chinthu chimodzi ine ndikufuna kukufunsani inu. Kodi abambo anga okalamba akanali moyo?" O!

²⁶⁸ Ndipo muyang'aneni iye, chimene iye anachita kwa Benjamini wamng'ono, amene ali choyimira cha zikwi zana limodzi, makumi anayi ndi zinayi, monga ife titi tipeze mtsogolo. Mukuwona chimene iye anachita? Iye anangothamangira mofulumira kumene kwa Benjamini, anagwera pa khosi pake ndi kuyamba kumukumbatira iye. M'bale wake wamng'ono amene anali atabadwa mu banja iye ali atapita, mwawona; ndi amayi ake, mpingo woyamba, mpingo wa Orthodox. zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi anabadwa Iye atachokako, pamene Iye anali kutali kukatenga Mkwatibwi Wake Wamitundu. O, mai! Kodi izo sizikuchita chinachake kwa inu! Apo izo ziri. Kotero inu mukuwona chimene iwo ali? Apo iwo ali.

²⁶⁹ Zindikirani tsopano, ngakhale iwo anayesera kumuchotsa Yosefe, chisomo chake chinafikira kwa iwo.

²⁷⁰ Ngakhale iwo anali atayesera kumuchotsa Yesu, Iye akubwererabe kumeneko (chifukwa iwo anali akhungu) ndi kuwapatsa iwo, mmodzi aliyense, mwinjiro woyera. Iye awatengera kumene iwo mkati, kwawo, mulimonse. Sichikupanga kusiyana kulikonse, chifukwa Iye ananena kale, "Ine ndidzawapulumsa iwo onse, mulimonse." Mukuwona?

Tsopano ndime 10. Zindikirani, iwo anafunsa "kubwezera." Mukuwona?

²⁷¹ Tsopano, ngati uyo akanakhala Mkwatibwi, zikanakhala monga Sitefano. "Atate, akhululukireni iwo," inu mukudziwa. Mwawona?

²⁷² Koma awa ali Ayuda amene angobweramo kumene, mwawona. Iwo anapempha "kubwezera." Zindikirani kachiwiri, mwawona, kachiwiri Iye anatero...Zindikirani, sikuti...Iye

anati, “Ndi abale anu,” Ayuda. Zana . . . Tsopano iwo ankafuna kubwezera. Iwo anati, “O, tikupita kuti . . . Ife, ife tikufuna Inu mutibwezerere ife pansu pamenepo.”

²⁷³ Iye anati, “Kanthawi pang’ono chabe, tsopano, kanthawi pang’ono chabe.” Pakuti, zindikirani, ndiroleni ine ndiwerenge izo apa. Ziri mu—ndime ya 10. Chabwino.

Ndipo iwo anafuwula ndi liwu lomveka, kunena, mpakana Liti, O Ambuye, woyera ndi woona, muleka inu kuweruza ndi kubwezera magazi athu pa iwo amene akukhala pa dziko lapansi?

Ndipo miinjiro yoyera inapatsidwa kwa mmodzi aliyense wa iwo; ndipo kunanenedwa kwa iwo, kuti iwo ayenera kupumulabe . . . kanthawi pang’ono, mukuwona, (chiyani?) kanthawi pang’ono, mpaka antchito amzawo . . .

²⁷⁴ Mukuwona? Tsopano icho ndi chiyani? Aneneri tsopano akulalikira kwa Israeli. Mukuwona?

. . . mpaka antchito amzanu nawonso . . . antchito amzanu ndiponso abale anu, amene ayenera kuphedwa . . .

²⁷⁵ Mukuwona, iwo okonzedweratu kuti akachitidwe choncho. Inu mukuwona?

. . . ayenera kuphedwa monga iwo anatero, ziyenera kukwaniritsidwa.

²⁷⁶ Mukuwona, mwa kulankhula kwina, ziri zokonzedweratu kwa iwo. Ndi Malemba, kuti iwo anayenera kuchita izo. “Ndipo ingopumulani kanthawi pang’ono. Tsopano inu muli nayo miinjiro yanu; inu mukupita kwanu; ndipo ingokhalani pamenepo kanthawi pang’ono, mwawona, yembekezani kanthawi pang’ono chabe.”

²⁷⁷ Tsopano zindikirani. Tsopano zindikirani, “Abale anu.” “Abale anu akuyenerabe kuphedwa,” chimene chikutanthawuza zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi amene ati ayitanidwebe mu Chisawutso. Zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi amene ayitanidwa.

²⁷⁸ Ndikukhumba ife tikadakhala nayo nthawi. Ife mwina tidzatenga izo mawa usiku, ngati Ambuye alola, ife . . . basi tisanalowe kumene mkati pa Chisindikizo china. Mukuwona?

²⁷⁹ Komanso, tsopano penyani, iwo anayenera kuphedwa ndi wotsutsakhristu. Ife tingobwera chodutsa; ndipo zindikirani, mu kukwera kotsiriza kwake, pamene iye akuswa—akuswa pangano limenelo ndi Ayuda awo kumusi uko. Ndipo apo iye akupita. Mukuwona?

²⁸⁰ Ayuda awa, zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, ali oti atulutsidwe ndi mboni ziwiri za Chivumbulutso 11. Tsopano, inu mukukumbukira, iwo anali oti anenere.

281 Inu mwawerengapo izo. Ndi angati awerengapo izo? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndithudi, ife tonse tikulidziwa, kuwerenga Lemba.

282 Ndipo iwo akunenera, mboni ziwiri izi zikunenera, mu nthawi ya theka lachiwiri la Daniele la masabata makumi asanu ndi awiri. Zimenezo ndi zaka zitatu ndi theka limodzi lotsiriza.

283 Mukukumbukira momwe ife tinatengera masabata makumi asanu ndi awiri a Daniele? Ine ndinati ife tidzazifuna izo pamene tidzafika mkati umu. Ine sindinkadziwa chifukwa chake, koma ine basi. . . Chinachake chinandiwuza ine kuti ife tidzazifuna izo, ndipo apa ife tiri. Eya. Mukuwona?

284 Zindikirani, mu nthawi ya Daniele. Tsopano kumbukirani, Daniele anawuzidwa kuti, “Mesiya akanadzabwera,” kalonga, “Mesiya,” kani, “ndipo Iye akanadzanenera. Israeli anali nawobe masabata makumi asanu ndi awiri otsalira. Ndipo mkati mwa masabata makumi asanu ndi awiri, Mesiya akanadzadulidwa, ndipo nsembe za tsiku ndi tsiku kuchotsedwapo.” Nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] “Koma analipobe atatu ndi theka, masabata oyikidwiratu.”

Mu kampata aka, Iye akutenga Mkwatibwi Wamitundu.

285 Tsopano, Mkwatibwi akupita mmwamba. Ndipo pamene Iye akupita mmwamba, aneneri awiri akuwuka kwa Israeli. Mukuwona?

286 Ndipo miyoyo iyo yomwe yakhala itaphedwa, tsopano, kutsika kupyola apa, Ayuda enieni, owona mmusi kupyola pamenepo; amene anali nalo dzina lawo pa Bukhu, amene ankakhala moyo woyenera ndi kuchita chinthu choyenera, amakhala moyo wa Chiyuda ku dontho. Iwo, iwo anaphedwa ndi Eichmann ndi ena ambiri. Anthu owona mtima, mamilioni a iwo kumusi uko! Ndipo Ajeremani aja anawawombera iwo ku imfa, ndi kuwazinga iwo, ndi kuwapha iwo, ndi kuwapachika iwo pa mipanda, ndi kuwatentha iwo, ndi kuwawotcha iwo, ndi china chirichonse. Wopandamagazi uyo, kapena wa mtima-wamagazi, Hitler wanjala, ndi Stalini, ndi Mussolini, ndi anthu onse awo amene ankawada Ayuda awo!

287 Ine ndikuganiza ndicho chimodzi cha—chimodzi cha zinthu chomwe chikugwirizira fuko ili pamodzi, chifukwa nthawizonse iwo ankalemekeza Myuda, uko nkulondola, ankamupatsa iye malo. Iwe ukalemekeza Myuda, ndipo Mulungu adzakulemekeza iwe.

288 Tsopano, liripo gulu la Ayuda amene ali zigawenga, basi monga pali Amitundu mwanjira yomweyo.

289 Koma Myuda weniweni, Mulungu anayika dzina lake pa Bukhu maziko a dziko asanakhazikitsidwe. Ndipo apa iye anali, wophedwa mu nthawi iyi. Ndipo kumbukirani, ganizani za izo tsopano, chiri changwiwo bwanji ichi. Zitachitika kumene

kuti mamiloni awo a Ayuda ophedwa, anthu osalakwa, ndi mafuko a mdziko; apa Lemba likuti, mu nthawi iyi kumene, yomwe mmodzi aliyense ali pansu pa guwa, kuzindikira chimene chinachitika, ndipo iwo akupatsidwa miinjira zoyera.

²⁹⁰ Ndipo iwo anati, “Chabwino, chifukwa? Kodi ife tingabwerere ku ufumu pakali pano?” Ufumu wa Chiyuda udzakhazikitsidwa pa dziko lapansi, inu mukudziwa. Yohane anati ufumu unali pamene, mwawona, kuti ukhazikitsidwe.

Tsopano, uwu ndi Ufumu wa Uthenga, inu mukuwona.

²⁹¹ Koma ufumu wa Ayuda udzalalikidwa ndi awa—aneneri awiri awa, kotero zindikirani u—u—ufumu wa pa dziko lapansi apa.

²⁹² “Ufumu wa Kumwamba ukulalikidwa,” . . . ndi Ayuda kapena kwa . . . ine ndikutanthawuza, “kwa Amitundu.”

²⁹³ Ufumu wa pano pa dziko lapansi, uli woti udzakhazikitsidwe mu Zakachikwi, pambuyo, Zakachikwi kwa Ayuda.

²⁹⁴ Tsopano zindikirani. Zindikirani ichi tsopano, apa, pamene iwo—pamene iwo akulalikira, mwawona.

²⁹⁵ Asanati awa—aneneri awa asanatulukire powenekera; Ayuda awa amene anali oti akafe pansu pa Eichmann ndi iwo ali, mmodzi aliyense wa iwo amene anakonzedweratu, akupatsidwa, (mwa chisomo) mwinjira zoyera. Mmodzi aliyense wa iwo akupatsidwa mwinjira zoyera. Zindikirani.

Tsopano chikuchitika nchiyani? Mofulumira pamene icho chikuchitika . . .

²⁹⁶ Ine ndikuyang’ana koloko iyo kumbuyo uko, ndipo ine ndikudziwa tiri—tiri kuchedwa. Koma ine sindikufuna kutero . . . Tawonani, ine—ine . . . Iwo . . . ndikuzindikira anthu osawuka awo ayimirira apo. Mulungu akuthandizeni inu, abale. Ine ndikuyembekeza mmodzi aliyense wa inu adzapatsidwa mwinjira zoyera tsiku limenelo, mwawona. Kuyimirira, kusinthana mmbuyo ndi patsogolo, ndi miyendo ikupweteka. Ndi ena a inu mwagwira ntchito tsiku lonse. Ine ndikudziwa chimene icho chiri. Ndipo taonani apa . . . Ndipo ena mwa akazi osawuka achikulire pang’ono atayimirira. Ine ndikuzindikira ena a amuna awa akuwapatsa akazi mipando yawo; ndipo winawake wamupatsa, mayi wina wamng’ono ali ndi mwana. Ndipo ine—ine—ine—ine ndikuwona izo zonse, mwawona, ndipo ine ndiri wotsimikiza Iye akutero. Zindikirani. Koma ine sindikufuna kukusungani inu motalika kwambiri. Ngati ine ndingakhoze chabe kukutengerani inu powona Uthenga, ndizo zonse ine ndikufuna inu kuti muchite, mwawona.

²⁹⁷ Tsopano zindikirani Ayuda awa. Ine ndiyenera kuchita ichi, polinga kuti ndikuloleni inu kuwona vumbulutso la Chisindikizo ichi; kuwona chimene ilo liri, miyoyo iyi pansu pa guwa, ndi omwe iwo ali. Tsopano zindikirani.

²⁹⁸ Mu nthawi ya Daniele, tsopano, theka lachiwiri la sabata la makumi asanu ndi awiri. Tsopano kumbukirani, “Mesiya anali woti adulidwe mkati mwake.” Ndipo pakati. Chabwino, theka la zisanu ndi ziwiri ndi chiyani? [Osonkhana ati, “Zitatu ndi theka.”—Mkonzi.] Zitatu ndi theka. Khristu analalikira motalika chotani? [“Zitatu ndi theka.”] Uko nkulondola. Tsopano, “Koma pali zoyikidwirabe, kwa anthu,” (chiyani?) “zaka zitatu ndi theka zina.”

²⁹⁹ Chabwino, mu nthawi iyi, chifukwa, onani, chimene chikuchitika, chiri, Mkwatibwi Wamitundu akusankhidwa mu mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo, ndipo akupita mmwamba.

³⁰⁰ Ndipo pamene zikuchitika mwanjira iyo, Ayuda onse amene anaphedwa motsatira kumeneko chifukwa cha khungu, okhala pansu pa guwa, Mulungu akubwera ndipo akuti, “Inu mwawona chimene icho chinali? Tsopano ine ndikupatsani mmodzi aliyense wa inu mwinjiro.”

Iwo anati, “Mpakana liti, Ambuye? Kodi ife tikupita mkati tsopano?”

³⁰¹ Anati, “Ayi, ayi, ayi, ayi. Anthu amzanu, Ayuda, ayenera kuvutikabe pang’ono pokha. Iwo ayenera kuphedwa monga inu munaphedwera. Chirombo chiyenera kuwapeza iwo pamene icho chikuswa pangano lake.”

³⁰² Tsopano zindikirani. Ndipo tsopano zindikirani, kamodzi. . . Tsopano ingokumbukirani, aneneri awa ali oti anenere malingana ndi Chivumbulutso 11. Inu, inu munakweza manja anu, inu munawerenga izo. Mukuwona? Ndipo iwo akupatsidwa mphamvu.

³⁰³ Ndipo ife tipeza amene iwo ali, mu miniti chabe, Ambuye akalola. Tsopano zindikirani amene ali aneneri awa. Ndipo tsopano Baibulo likutiwuzwa izo apa. Ndithudi, Iye akutero. Ndithudi! Mwawona?

³⁰⁴ Tsopano, zindikirani, mkati mwa masabata atatu ndi theka awa tsopano, amene iwo akunenera pansu apa ndipo c—Chivumbulutso apa chinati. . . Ndipo iwo—iwo ananenera masiku chikwi chimodzi mazana atatu ndi makumi awiri awiri. Ngati. . .

³⁰⁵ Tsopano, kalendala wozolowereka wa Chiyuda, nthawi yozolowerekea ya kalendala wa Mulungu, ili chimodzimidzi masiku makumi atatu mu mwezi. Kalendala wa Chiroma, ndimene inasokoneka iyo. Kalendala yozolowereka ili masiku makumi atatu mu mwezi.

³⁰⁶ Tsopano, ngati inu mukufuna kutenga masiku makumi atatu, ndi kuphatikiza zaka zitatu ndi theka kwa iwo, ndipo onani masiku makumi atatu, ndipo, chabwino, inu mwapeza chiyani? Masiku chikwi chimodzi mazana atatu ndi. . . kapena mazana awiri ndi makumi awiri atatu. “Masiku chikwi chimodzi

mazana awiri ndi makumi awiri atatu (masiku makumi asanu ndi amodzi),” chimodzimodzi zaka zitatu ndi theka.

307 Tsopano, inu mukuwona, palibe kulakwitsa kwa izo. Apo izo ziri, kungogwirizana pamodzi monga—chipsyepsye cha nkunda kubwera pamodzi. Zindikirani, aneneri awiri awo analalikira kwa zaka zitatu ndi theka, kwa Ayuda. Mkati umo, muli kuyitanidwa, zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi.

308 Ndiyeno, zindikirani, aneneri awiri awa ali chimodzimodzi Mose ndi Eliya. Mukuwona? Mukuwona? Tsopano penyani, penyani, wawo...Penyani pa utumiki wawo. Tsopano yang’anani zomwe aneneri awa akuchita. “Iwo ali nayo mphamvu yokanthira dziko lapansi ndi mliri, mowirikiza monga iwo angafunire.” Ndani anachita izo? Mose. “Iwo ali nayo mphamvu yotseka miyamba, ndipo siyina vumbe mu tsiku la utumiki wawo.” Ndani anatseka miyamba kwa zaka zitatu ndi theka? [Osonkhana ati, “Eliya.”—Mkonzi.] Apo iwo ali. Ndiwo iwo. Mwawona, ndicho... .

309 Onani, munthu, pamene iye amwalira, iye samasintha udindo wake. Iye samasintha mapangidwe ake, mwawona. Penyani, pamene—pamene, asanati... .

310 Pamene Sauli anali atabwerera mmbuyo, ndipo apo kunalibe aneneri mu dziko, iye sankakhoza kumvetse choti nkuchita—choti nkuchita. Iye anayima motsutsa izo. Iye anali kupita ku nkondo. Iye anapita kwa mfiti yaikazi ya ku Endori.

311 Tsopano, magazi a ng’ombe ndi mbuzi okha, iye ankakhoza kuchita izi. Ndipo iye anawuyitana mzimu wa Samuele.

312 Ndipo pamene Samueli anabwera pamwamba, apo iye anayima, mu mwinjiro wake wa mneneri. Osati icho chokha, koma iye anali akadali mneneri. Anati, “Bwanji iwe wandiyitana ine kuchokera ku kupuma kwanga,” mwawona, iye anati, “powona kuti iwe wakhala mdani kwa Mulungu?” Iye anati, “Pa nthawi iyi, mawa usiku, iwe ukagwa mu nkondo. Ndipo nthawi iyi, mawa usiku, iwe udzakhala ndi ine.” Ndipo ndizo chimodzimodzi zomwe zinachitika. Mukuwona? Osati kokha... . Iye anali akadali mneneri. Mukuwona?

313 Ndipo anthu awa akadali aneneri. Tsopano ife tizama pang’ono mu izo, mu maminiti pang’ono chabe, Ambuye akalola. Mukuwona?

314 O, mai, momwe ine ndimakondera Mawu amenewo! Nzosadabwitsa, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha. Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu!”

315 Aneneri awiri awa ali Mose ndi Eliya, molingana ndi ntchito zawo zomwe zikufanizidwanso kachiwiri. Uwo, uwo wakhala nthawizonse utumiki wawo. Tsopano zindikirani, monga momwe iwo ankachitira. Izo sizinawasintho iwo. Kumbukirani, amuna awa sanafe. Yang’anani miniti chabe.

³¹⁶ Tsopano, musati musokoneze, ife tisanachoke kwa izi. Musati musokoneze utumiki wa Eliya wa nthawi yachisanu ndi utumiki wake wa nthawi yachinai. Ine ndakhala ndikukuwuzani inu, Mpingo wa Amitundu ukuyang'anira Eliya. Kulondola.

³¹⁷ Ndipo apa iye ali cha kuno ndi Myuda. Kumbukirani, iye sangakhoze kubwera kanai; iyo—iyo ndi nambala ya mdani. Iye ayenera kukhala kasanu.

³¹⁸ Nthawi yoyamba imene iye anabwera, iye anali Eliya, mwiniwake. Nthawi yotsatira yomwe iye anabwera, iye anali Elisha. Nthawi yotsatira yomwe iye anabwera, iye anali (chiyani?) Yohane Mbatizi. Nthawi yotsatira yomwe iye akubwera, ili ya mngelo wachisanu ndi chiwiri. Ndipo nthawi yachisanu iye akubwera, iye ali ndi Mose kutsidya uko, akulalikira kwa iwo. Ndithudi. Inde, bwana. Musati mumusokoneze iye. A-nha.

³¹⁹ Kasanu, ngati inu mukudziwa anu—mawerengero anu a Baibulo, kasanu ili nambala ya kuvutikira chisomo. Ndipo ndicho chomwe Iye wachita. Tsopano, yang'anani, inu mukufuna kudziwa pamene izo ziri. Kodi Yesu anali kuvutikira kwa chisomo? J-e-s-u-s, zisanu, l-a-b-o-r. [Mawu awa ali mu chingerezi, kutanthawuza “Yesu, ntchito.”—Womasulira.] Kodi uko nkulondola? Kuvutikira, kwa—kwa chikondi kwa inu. Ndipo ngati inu mufika kwa Iye, inu mumadza chotani, mwa chiyani? F-a-i-t-h mu l-a-b-o-r. [Mawu awa ali mu chingerezi, kutanthawuza “Chikhulupiriro mu ntchito.”—Womasulira.] Kodi uko nkulondola? Labor ili ndi chiwerengero cha grace, chabwino, kwa okhulupirira.

³²⁰ Zindikirani, Eliya woyamba, ameneyo anali iye. Wachiwiri anali Elisha. Wachitatu anali Yohane. Wachinai anali mngelo wachisanu ndi chiwiri, kapena mtumiki wotsiriza kwa Mpingo, malingana ndi Malaki 4 ndi Chivumbulutso 10:7. Tsopano, nthawi yachisanu, iye ali mtumiki kwa Ayuda, kwa zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, kwa Ayuda, utatha Mpingo kupita.

³²¹ Ine—ine—ine ndikungomverera mosayenera pang'ono, onani. Mwawona? Penyani, ngati ena akuganiza kuti... Ine ndikufuna inu mumvetse izi tsopano, mwawona. Ngati ena akuganizabe kuti Malaki 4, “kudzabwezeretsa” anthu, chiri chinthu chomwecho iye akukachita kumusi uko kwa Ayuda, ndi kuganiza izo ziri zonse zofanana, ndiroleni ine ndiwongole icho kwa inu, miniti yokha. Mwawona, izo zikanakhala zosokoneza pang'ono. Chifukwa, kumbukirani, mu Malaki 4, akuti, “Kubwezera Chikhulupiriro cha atate... kapena ana kubwerera kwa atate.” Mwawona, kubwerera kwa atate!

³²² Tsopano ndiroleni ine ndikuwonetseni inu kusiyana kwa utumiki wawo. Ngati iye abwera kudzabwezera Chikhulupiriro cha ana kubwerera kwa atate, iye akanadzamukana Khristu.

Iye akanadzabwerera ku lamulo. Kulondola uko? Atate ankasunga lamulo. Inu mwamvetsa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

³²³ Zindikirani, pamene Elisha, pamene iye anabwera kudzakwaniritsa utumiki wake mu Malaki 4, onani, monga Malaki 4, Eliya anali mwa yekha.

³²⁴ Koma pamene iye akubwera kudzatumikira kwa Ayuda, a Chivumbulutso 11, iye ali naye Mose ndi iye. [M’bale Branham awombetsa manja ake pamodzi kawiri—Mkonzi.] Kotero, apo palibe kusokonezeka, ayi konse. Mukuwona? Mwamvetsa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”]

³²⁵ Pamene Elisha akubwera, wa Malaki 4, iye ali mwa yekha. Eliya adzathamanga; osati Eliya ndi Mose. “Eliya” adzawuka. Koma kudzoza komweko, kumene, anati Eliya adzabwera kwa gawo lotsiriza la m’badwo wa mpingo, “kudzabwezeretsa Chikhulupiriro cha ana kubwerera ku Chikhulupiriro chapachiyambi cha atate,” Chikhulupiriro cha atumwi, chomwe inu mukuyenera kubwererako. Ndipo wotsutsakhristu wawatulutsamo iwo onse. “Kuti abwezeretsenso,” monga Malemba ena onse agwirizana pamodzi. Mwawona, iye akubwera mwa yekha. Mukuwona?

³²⁶ Koma pamene iye akubwera kwa Mpingo, Baibulo... kapena kubwera kwa zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, Baibulo momveka likunena kuti onse iye... Pali awiri a iwo, osati amodzi a iwo. Awiri a iwo! Ndipo utumiki wake woyamba sukanawatenga Ayuda ndi kuwayika iwo mobwerera ku lamulo, akukhala iye... chifukwa iye akubwera, akulalikira Khristu kwa zikwi zana limodzi makumi anayi ndi zinayi, ameni, “Apo Iye ali, Mesiya uyo amene anadulidwa.” Ameni! Ndi zimenezo, kotero musatenge izo mosokoneza. Izo siziri chisokonezo. Lemba si limanama, ayi konse.

³²⁷ Ulemerero! O, pamene ine ndinawoza icho, ine ndinali kulumphamwamba! Ine ndinati, “Zikomo Inu, Ambuye,” pamene ine ndinali kuyang’ana icho chikuchitika kunja uko. Ndinamuwona Eliya uyo akutulukira kumeneko kwa m’badwo woyamba uja, mwa yekha, ndipo iye anali mwa yekha. Ndiye pamene ine ndinamuwona iye akubwera kachiwiri, kutali cha kwinakwakwenso, apo panali awiri a iwo kumeneko pamene izo zimachitika. Anati, “Ndi zimenezo. Izo, izo zikuchita icho, Ambuye. Ameni! Ine ndachiwona icho tsopano! Aleluya!” Ndizo chimodzimodzi.

³²⁸ Ngati ine ndikanapanda kutchula izo, izo zikanakhala zosokoneza pang’ono kwa winawake. Koma Iye—Iye anandiwuza ine kuti ndinene izo, kotero ine ndinatero.

³²⁹ Zindikirani, amuna awa asungidwa amoyo ndi Mulungu, kuchokera ku utumiki wawo wapachiyambi, kwa ntchito ya mtsogolo; iwo anatomikira iyo mwabwino zedi. Mukuwona?

Tangoganizani, mzimu uwo wa Eliya ukutumikira nthawi zisanu; Mose, kawiri. Chiyani? Kusungidwa amoyo kwa kupitiriza, ntchito ya mtsogolo.

³³⁰ Iwo sanali ngakhale mmodzi wa iwo wakufa tsopano; inu musakhulupirire zimenezo. Iwo onse anawoneka, amoyo, akulankhula kwa Yesu pa Phiri la Chiwalitsiro. Koma, kumbukirani, iwo ayenera kufa.

³³¹ Tsopano, tsopano, Mose anafa kumene. Koma iye anawuka, chifukwa iye anali choyimira changwiwo cha Khristu. Mukuwona? Palibe aliyense anadziwa konse kumene iye anayikidwa. Angelo anabwera kudzamutenga iye. Mukuwona? Iye anali naye Mngelo wonyamula mtembo. A-nha. Chifukwa? Palibe munthu wachivundi akanakhoza kumunyamulira iye kumene iye anali kupita. Iye anangopita kupyola mu mchitidwe, ndizo zonse. Iye anali nawo Angelo, onyamula mtembo, mwawona, chifukwa Iwo anamutengera iye kumene iye ankayenera kuti akhale. Palibe mmodzi akudziwa.

³³² Ngakhale kwa Satana, sanathe ngakhale kudziwa. Iye anakangana naye Mngelo wamkulu. Uko nkulondola. Iye sanakhoze kumvetsa chimene chinachitika kwa Mose. “Ine ndinamuwona iye akunjajemera cha kumeneko. Ndi kuyang’ana kunja cha ku dziko, ndi kuyang’ana mobwereza kwa ana, ndi zina zotero, ine ndinamuwona iye akunjajemera. Koma iye anaponda pamwamba pa Thanthwe, ndipo iyo inali nthawi yotsiriza yomwe ine ndinamuwona iye.”

³³³ Ndilo Thanthwe! Ndilo Thanthwe! Ndiroleni ine ndiyime pa Thanthwe limenelo, pa mapeto a ulendo wanga! Inde, bwana! Tsopano, m. . . Abale Anga achikuda ankakonda kubwera pano ndi kuyimba nyimbo yaying’ono, “Ngati ine ndingakhoze, ine ndithudi ndikanayima pa Thanthwe limenelo pamene Mose anayima.” Inde, bwana! O, ndilo Thanthwe lomwe ine ndikufuna kuyimapo, nanenso. Mwa chikhulupiriro ine ndikuyima pamenepo.

³³⁴ Koma kumbukirani, Eliya, iye anangofika potopa, chifukwa iye anali nayo ntchito yambiri patsogolo pake. [M’bale Branham akuyimikira. Osonkhana akuseka—Mkonzi.] Koteru iye anatheratu mwabwino ndithu, ndipo Mulungu anangomutumizira iye pokwera kupita Kwawo, uko nkulondola, anatumiza garetu. Kodi uko nkulondola? [“Ameni.”] Anamutengera iye mmwamba. Iye sanafe konse, chifukwa Iye anamusunga iye wamoyo. Iye anali nayo ntchito yamtsogolo kwa iye. Mumulole iye amudzoze munthu, nayenso, mwawona, kutulukira mwa Mzimu wake.

³³⁵ Koma iwo ayenera kulawa imfa. Tsopano Chivumbulutso, mutu wa 11. Tsopano, tiyeni tipite, ine ndiri apa kumene basibe. Tiyeni tingogunda izo, Chivumbulutso 11. Yang’anani ndi kuwona ngati iwo onse sakuphedwa. Inde, bwana. Iwo

onse ayenera kulawa imfa. Inde, bwana. Utumiki wawo utatsirizika, iwo analawa imfa. Chivumbulutso 11, ndipo tiyeni tiyambire pa 7.

Ndipo pamene iwo...atsiriza umboni wawo, chirobho chimene chinatuluka kuchokera ku maphompho opanda malire...chikupanga nk'hondo motsutsa iwo,...

336 O, mai, iye sangakhoze kupirira izo; awo oyera-odziguduza abwerera kachiwiri, mwawona. Chabwino. Chabwino.

...kuchokera ku phompho lopanda malire... adzapanga nk'hondo motsutsa iwo, ndipo adzawagonjetsa iwo, ndi kuwapha iwo.

337 Koma yang'anani chimene chikuchitika. Iwo afanizidwira mwangwiro tsopano.

Ndipo mitembo yawo idzagona mu msewu—mu msewu wa mzinda wawukulu uwo,...mwauzimu... wotchedwa Sodomu ndi Igupto, kumene nawonso Ambuye wathu anapachikidwa, (Yerusalemu, mwawona).

338 Tsopano iwo ayenera kulawa imfa, (sichoncho iwo?) uko nkulondola, utumiki wawo utatha.

339 Chifukwa? Utumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, utumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, utumiki wa Eliya kwa mngelo wachisanu ndi chiwiri, osati. . . Bwanji osati, bwanji sanakhoze, kani, ine ndikuyesera kunena kuti, utumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri ndiye kudzakhala ndi Mose, ngati iye ali wachisavundi, mommwe zikanakhallira ndi Eliya? Bwanji osati iwo. . . Bwanji Mulungu sanangotumiza, anati, "Eliya, iwe—iwe unagwira molimbira kwambiri, ine. . . ndipo chirichonse, malo onse osiyana awa. Ine—ine ndikukhulupirira ine ndingotumiza Mose pansu?" Chifukwa?

340 Yang'anani pa utumiki wa Mose. Eliya anali mneneri kwa mafuko onse; koma Mose anali wopereka lamulo kwa Ayuda okha. Ameni. Mose ali pamenepo kuti anene. . . Chifukwa chimene iye akubwera ndi Eliya. . . Ayuda awo akuti, "Dikirani, ife tikanasunga lamulo kuno." Koma apa pakuyima Mose mwiniwake; ndipo apa pali Eliya akuyima naye iye. O! Mukuwona? Iye amabwera kwa Ayuda okha. Mukuwona? Mose anangopita kwa Myuda; mneneri Eliya anali kwa mafuko onse. Koma Mose anakhala mneneri kwa Ayuda, ndipo wopereka lamulo. Mukuwona? Umenewo unali uthenga wake, lamulo.

341 Koma uthenga wa Eliya unali chiyani? Kwa akazi odula tsitsi; zipembedzo. Inde, bwana. Ndipo iye anawang'amba iwo kwenikweni mpaka zidutswa. Nkhope zopentapenta; anawawuza iwo, "Inu mudzadyetsedwa kwa agalu." Iye anangowang'amba kwenikweni iwo.

342 Ndiyeno pamene Mzimu wake unabwera pa Yohane, iye anatuluka kuchokera ku chipululu ndipo anachita chinthu chomwecho. Kulondola. Anati, “Inu musaganize kuti ndife a *ichi* kapena *icho*. Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.”

343 Anayenda kukwera ndi msewu, iye anati, “Ndipo inu mukutanthawuza kuti mundiwuze ine kuti inu mwakwatira mulamu wanu yemwe...?” Anati, “Sikoloreka kwa inu kuti muchite izo!” O, m’bale! Psyi! Ha! Iye anamuwuza iye. Ndithudi.

344 Zindikirani, miyoyo iyi ili yoti iyembekezere kanthawi pang’ono, zana limodzi makumi anayi ndi zinayi...kuti aphedwe. O, siziri izo, siziri...Izo zikungoyika Baibulo pamodzi.

345 Tsopano nthawi yanga yatha chimodzimodzi, ngati ine nditi ndikutulutseni mofulumira. Koma ine ndiri nazo chabe pang’ono zochulukirapo zazing’ono kuti ndinene, ngati inu mungapirire icho. [Osonkhana ati, “Pitirizani!”—Mkonzi.] Ine ndikudziwa kuti kwatentha. Ndipo ine ndikuukha thukuta.

346 Koma, tamverani, ine ndiri nacho chabe chinachake choti ndikuwuzeni inu. Icho chiri chabe chabwino kwambiri, icho chikungotentha mu mtima mwanga. Ine ndikuyembekeza inu simunayiwale izo, mukuwona. Ndiroleni ine ndinene izi, mu kukhalapo kwa Iye. Mwa chisomo Chake, Iye anandirolanso ine kuwawona anthu anga, osati kale kwambiri, ali mu miinjiro yoyera. Inu mukukumbukira izo? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Mukukumbukira? Inu mukuyikumbukira nkhaniyo, osati kale kwambiri? [“Ameni.”] Mkwatibwi Wamitundu, iwo ali kumeneko tsopano. Iwo onse anali mu miinjiro yoyera.

347 Ine ndinali nditawuka. Ine ndinali ndiri pa msonkhano. Zakhala ziri pafupi chaka chapitapo, mopitirira pang’ono. Ine ndinawuka mmawa umodzi, ndipo ine ndinanyamuka. Ndipo ine ndinati, “Wokonedwa?” kwa mkazi wanga. Iye sanasunthe. Ana pafupi...Anayenera kuwuka ndi kuwatengera iwo ku sukulu, cha kuno kumene ku malo akale. Chabwino, ine—ine ndinanyamuka mu bedi, inu mukudziwa, ndipo ndinatsamira. Inu mukudziwa momwe; ukadzuka ndipo nkungotsamira mutu wako kumbuyo mogonera thabwa la kumutu. Ife tiri nayo imodzi ya mabedi achikale. Ndipo kotero ine ndingotsamira kumbuyo monga *chonchi*.

348 Ndipo ine ndinaganiza, “Mnyamata, iwe uli kale makumi asanu ndi zitatu. Ngati iwe uti uchite chirichonse kwa Mulungu, kuli bwino iwe uzichitiratu icho, chifukwa iwe ufika pokhala kwambiri—pokalamba kwambiri, pakapita kanthawi.”

349 Ndipo ine ndinaganiza, “Inu mukudziwa, uko nkulondola, tsopano.” Ine ndinaganiza, “Mnyamata, iwe ukudziwa, ine

sindiri kutali kwambiri. Ine ndiyenera kupita posachedwa kwambiri.” Ine ndinati, “Icho—icho ndi chaka chimodzi wamkulu kuposa momwe abambo anga anakhala moyo.” Mukuwona? Ine ndinaganiza, “Ine ndiyenera kuchokapo posachedwa kwambiri. Ine ndinachiwona icho. Ndipo, apa, ine sindinamuchitire kanthu Mulungu, panobe.” Ine ndinaganiza, “Ine nthawizonse ndafuna nditamuchitira chinachake Iye.” Ine ndinaganiza, “Ine ndiyenera kufulumira ndi kukachita icho, ngati ine nditi ndichite icho. Ndipo ine sindikudziwa momwe nditi ndichitire icho, ndizo zonse.”

350 Ine ndinaganiza, “Amuna, ine ndikuyembekeza ndikhala moyo kuti ndidzamuwone Iye akubwera. Ine sindikufuna kudzakhala chipukupuku, kapena mzimu.”

351 Onani, ine ndinali nthawizonse wamantha ndi mzimu. Ndipo tsopano, inu mukudziwa, izo zimakhala ngati. . . Ine nthawizonse ndimaganiza, monga ngati ndikanakumana ndi M’bale Neville iye akanadzakhala kamtambo kakang’ono koyera kakuyendayenda, inu mukudziwa. Ndipo ine ndikanati, “Moni, M’bale Neville.” Ndipo iye akanati, “Moni, M’bale Branham,” mwa mphamvu yinayake; iye sakanakhoza kulankhula. Koma ine ndikanangodziwa kuti uyo anali M’bale Neville. Eya. Ine ndikanafuna kumugwira dzanja lake monga momwe ine nthawizonse ndimachitira. Chifukwa, ndizo zonse zomwe ine ndikudziwa, ali anthu. Mukuwona, ine ndikanafuna kumugwira dzanja lake, koma iye alibe dzanja. Liri pansi uko mu manda, titavunda patali. Mukuwona?

352 Ine ndinaganiza, “Mai, ine ndikuyembekeza ine sindiyenera kupyola mu zimenezo.” Tsopano, ine ndinali. . . Tsopano ine ndikuwuzani inu chowonadi. Ine—ine ndinali wa mantha kuti ndife; osati kuchita mantha kuti ndikanadzatayika, koma ine sindinkafuna kukhala mzimu. Ine ndimafuna kukhalabe munthu. Ine ndimafuna kuyembekezera Mkwatulo, mwawona. Ine ndimangofuna kukhala monga choncho. Ine sindimafuna kukhala mzimu ayi, kumapita uku ndi uku. Ine ndinali nditagona pamenepo, ndikuganiza zimenezo.

353 Ndipo, zonse mwadzidzidzi, panali chinachake chinachitika. [M’bale Branham akhwatchitsa chala chake kamodzi—Mkonzi.]

354 Tsopano, inu mukudziwa, ndipo inu nonse mukudziwa, za masomphenya. Ndipo ngati awa anali masomphenya, ine sindinakhalepo nawo amodzi onga iwo, mwawona. Ndipo ine ndakhala nawo iwo kuyambira ine ndinali mnyamata wamng’ono pang’ono.

355 Ndipo, zonse mwadzidzidzi, chinachake chinachitika. Ndipo ine ndinadzimverera ndekha ndikuchoka. Ine ndinaganiza, “A-o.” Ndipo ine—ine ndinaganiza, “Ine—ine ndamwalira kale, mwawona, ndipo ine—ine ndapitiratu.” Mukuwona?

³⁵⁶ Ndipo ine ndinafika ku malo, ndipo ine ndinaganiza, “Ine ndikukhulupirira ine ndiyang’ana mmbuyo.” Izo zinali chabe monga zenizeni, amzanga, monga ine ndikuyimira pomwe pano. Mukuwona? Ndipo ine ndinachewuka pozungulira, kuti ndiyang’ane mmbuyo. Ndipo apo ine ndinali, nditagona pa bedi. Ndipo ine ndinali nditaziwongola, nditagona pambali pa mkazi wanga.

³⁵⁷ Ine ndinaganiza, “Chabwino, izo mwinamwake anali matenda a mtima.” Mukuwona? Ine ndinaganiza, “Chabwino, mwawona, ine ndangofa mwadzidzidzi,” imene ingakhale njira yabwino yopitira. Kotero, ine ndinaganiza, “Awo ndi matenda a mtima. Ine sindinasowe kuvutikira.” Ine ndinayang’ana, ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, tsopano, ndicho chachirendo. Apo ine ndagona, apo kumene; ndipo apa ine ndayima, pano.”

³⁵⁸ Kotero, ine ndinachewuka. Iwo unkawoneka monga chachikulu chopambana—monga munda wawukulu wopambana, monga, kapena chinachake, kutambalala chabe kwakukulu kwa munda wa wuzu wabuluwu. Ndipo—ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndikudabwa chomwe ichi chiri?”

³⁵⁹ Ndipo, zonse mwadzidzidzi, pamene ine ndinkayang’ana, apa panabwera zikwi kuphatikiza zikwi za akazi aang’ono, onse mu miinjira yoyera, tsitsi likuzendewera pansu mpaka mchiwuno mwawo, opanda nsapato, ndipo iwo anali kuthamanga cholunjika kwa ine. Ine ndinaganiza, “Tsopano ichi ndi chiyani?”

³⁶⁰ Ine ndinachewuka mozungulira, ndinayang’ana mmbuyo *kumeneko*, ndipo apo ine ndinali; ndipo ndinayang’ana mmwamba mbali *iyi*, apo iwo amabwera. Ine ndinaluma chala changa. “Ine—ine—ine—ine sindikugona, chimodzimidzi.” Koma, ine ndimakhoza kumverera. Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ndiye, chinachake pano, chachirendo.”

³⁶¹ Ndipo akazi awa onse akubwera, akuthamanga. Ndipo ine sindinawonepo akazi okongola chotero! Ndipo iwo onse amabwera, akuthamangira kwa ine. Ndipo pamene iwo anathamangira kwa ine . . .

³⁶² Inu mukudziwa momwe ine ndakhalira, kukhala ngati . . . Iwo amanditcha ine wodana nawo akazi, koma ine sindiri, mukuwona. Koma, ine—ine ndikungoganiza, mkazi wabwino ali mmodzi mwa . . . ali ngale. Koma, ine ndikuganiza, mmodzi amene sali wabwino, ali, monga Solomoni amanenera, “madzi mmagazi ako.” Kotero ine ndithudi ndiribe nawo ntchito kwa—kwa akazi a mbiri yoyipa kapena amaphunziro.

³⁶³ Ndipo kotero akazi awa onse amabwera. Iwo anayamba kuponya mikono yawo pozungulira ine. Tsopano, icho si chachizolowezi. Inu mukudziwa ine sindikanayima nacho icho chimenecho. Kotero, ndipo iwo anali . . . Tsopano, ine ndinena ichi mwanjira, yakuti, ine ndiri—ine ndiri mu gulu

losanganikirana. Koma, iwo anali, iwo anali akazi. Iwo anali akazi. Ndipo iwo—iwo ankandikumbatira ine, mmodzi aliyense, ndipo anati, “Wathu—m’bale wathu wofunika!” Ndipo mmodzi amadzandikumbatira ine, ndiyeno mmodzi wina nkudzandikumbatira ine.

364 Ine ndinali nditayimirira pamenepo, kuyang’ana. Ine ndinaganiza, “Chabwino, tsopano, ichi ndi chiyani?” Mukuwona? Ndipo iwo anali kuyimirira pamenepo. Ine ndinaganiza, “Chachitika nchiyani?” Ine ndinayang’ana mmbuyo pansi. Apo ine ndinali, nditagona pansi kumene *pomwepo*; ndipo apa ine ndinali, nditayima *apa*. Ine ndinaganiza, “Tsopano, ndicho chosamvetsika. Ine—ine sindikumvetsa izi.”

365 Ndipo akazi amenewo kufuula, “O, m’bale wathu wofunika,” ndi kumandikumbatira ine. Tsopano, iwo anali chidutswa chirichonse, mwa kumverera, akazi.

366 Tsopano mundikhululukire ine, alongo, pamene ine ndikunena izi, chifukwa... Koma inu mumamvera kwa adokotala anu; ndipo ngati ife tiribe malingaliro oyera, ndiye sindife Akhristu. Ine sindikusamala... .

367 Ine nthawizonse ndakhala moyo woyera. Mulungu akudziwa izo. Pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, Mngelo wa Ambuye anandiwuza ine kuti ndisayipitse thupi langa, kusuta, kapena kumwa. Ndipo icho chakhala chiri chowona. Mwa chisomo cha Mulungu, ine ndasunga izo. Pamene ine ndinali wochimwa, ine sindinali kuthamangathamanga nawo akazi. Ndipo chotero... .

368 Koma mwamuna aliyense yemwe angalole mkazi kumukumbatira mu mikomo mwake, iye pokhala wopangidwa ndi khungu la chimuna, ndipo iye wamkazi, apo pakhala kugirigisha. Ine sindikusamala kaya ndinu yani, tsopano, inu musandiwuze ine kuti inu simuli, ngati inu muli munthu wathanzi.

369 Koma, osati Kumeneko; chifukwa inu mulibe, konse, khungu losiyana. Iwe siwudzachimwa nkomwe Kumeneko. Kumeneko kunali kusintha. Kumeneko kunalibenso choposa chikondi cha pa abale basi kwa akazi amenewo.

370 Ngakhale, mu chisomo chimene iwo amayang’anapo; ine ndikuganiza, m—mkazi, mkazi wabwino amene amadzisunga yekha bwino, ndi kumayenda monga dona, iye ali—iye ali chitsanzo cha ngale pa dziko lapansi. Ine—ine ndimakonda chirichonse chimene chiri chachisomo. Ine ndikuganiza, m—mkazi amene amasunga malo ake, ndikuyesera kukhala dona, ali—ali thunthu la ulemu. Ine ndimakhulupirira izo. Ndipo ine ndikuganiza, mmodzi yemwe sali, ali monga ngati k—Khristu ndi wotsutsakhristu, chinthu chofanana.

371 Ine—ine ndimakonda chirichonse chomwe chiri chachirengedwe. Monga kavalo wokongola, kapena chirichonse, iye amangoyima mu thunthu la kavalo wokongola weniweni. Kapena, chirichonse chonga icho, phiri lokongola, akazi okongola, amuna okongola, chirichonse chimene chimayima mu mapangidwe a Mulungu, ine nthawizonse ndimayamikira zimenezo.

372 Ndipo awa anali angwiro. Koma zinalibe kanthu kaya iwo akanandikumbatira ine kochulukwa bwanji mmikono mwawo, ndipo iwo anali akazi, inu mukumvetsa, koma apo sipakanakhala tchimo ayi. Zogirigisha zachimuna ndi zogirigisha zachikazi, zonse, zinali zitachoka. [M'bale Branham awombetsa manja ake palimodzi kamodzi—Mkonzi.] Ndikuthokoza Mulungu! Iwo anali alongo anga, kwathunthu.

373 Ine ndinayang'ana. Ndipo ine ndinayamba. . . Ine—ine ndinayang'ana pa manja anga; ine ndinawona iwonso onse anali ang'ono kwambiri. Ndipo ine ndinayang'ana; ine ndinali wamng'ono, inenso. Ndipo ine. . .

374 Ndipo kutha tsitsi kwanga, monga bambo wamng'ono; kumayika chidulo chotcheza pa ilo, wometa anatelo, ndipo analichotsapo ilo pamene ine ndinali chabe mnyamata. Ndipo icho chakhala nthawizonse kukhala ngati—chinthu kwa ine, mwakuti ine—ine—ine ndimazizidwa mwamsanga choncho, chifukwa chakuti liwombo langa likadali lofewa, inu mukudziwa. Ndipo mizu ya tsitsi ikadalipo pamenepo, koma iyo inawotchedwa ndi chidulo chotcheza, ndipo tsitsi silingakhoze kumera konse, mwawona.

375 Ndipo ine ndinapita, mkazi wanga, pamene ine. . . zaka patali zapitazo, ndipo anandigulira ine kachidutswa ka tsitsi kuti ndizivala, kachidutswa kakang'ono ka tsitsi, kuti ndizivala, kuphimba mutu wanga. Koma ine ndinali nthawizonse wamanyazi kuvala iko, chifukwa chinkawoneka ngati chinali chinachake chonyengezera. Ndipo ine sindimafuna kanthu konyengezera.

376 Ndipo kotero ine ndinaganiza, “Ine ndizingovala kachisoti.” Ndiye, ine ndinachita, kwa kanthawi. Inu mukudziwa chimene iwo anachita? Iwo ankafuna kumanditcha ine “bishopu” ndiye, ndinati ine ndinkafuna kukhala. . . Mukuwona? Ine ndinangoti, “Chisiyeni icho chipite.”

377 Kotero ine ndinkangovutika nako kuzizira koyipa, ndipo kulola iko. . . Koma, tsopano, inu kungotsegula mazenera amenewo, chirichonse, mpweya pang'ono uwo umene umabwera modutsa monga choncho, mzanga, ine ndimawumva iwo.

378 Ndipo ine ndinapita kwa dokotala ndi kukamufunsa iye, chimene iye anali kuganiza. Iye anati, “Chabwino, ona, ako—mabowo ako ali otseguka. Iwe ukuchita thukutha, kuchokera ku kulalikira. Mpweya umenewo umabwera. Iwo—iwo umayika

nyongolosi yoziziritsa apa mu mamina, ndipo iyo imayenda mpaka kummero wako. Mmawa wotsatira iwe umasasa mawu. Ndi zimenezotu.”

³⁷⁹ Ndipo—ndipo kotero, o, mai, anyamata inu amene muli nalo tsitsi, inu simukudziwa momwe inu muyenera kukhala wothokozerwa, ndi chifukwa chokhala nalo ilo. Uko nkulondola. Mukuwona?

³⁸⁰ Chabwino, tsopano, ine ndinadzazipeza, ndiye, kuti ine—ine ndikupita ku. . . Limodzi la masiku awa, ngati ine sindidzakhala nawo mano anga, ine ndidzayenera kukhala nawo ena a iwo, ndipo, kotero, kapena ngakhale kuchita wopanda iwo.

³⁸¹ Kotero ngati munthu—ngati munthu. . . Chabwino, ine sindikanadzaganiza kuti zingakhalenso kwa mwamuna, ngati iye akufuna kutero, kuvala kachidutswa katsitsi, kuposa momwe zikanakhala kwa mkazi kuvala chimodzi cha mbewa izi kapena makoswe awa, chirichonse chimene iwo amayika mu tsitsi mwawo monga choncho, kuti alikongoletse ilo. Mukuwona? Koma—koma, zedi, ngati iwe uchita izo, zimatengera chimene iwe ukuchitira izo. Mukuwona? Zimatengera pa chimene iwe ukuchitira izo. Ndipo kotero. . .

³⁸² Koma, komabe, nditayimirira pamenepo, ine ndinamverera mmwambamu, ndipo ine ndinali nalo tsitsi langa kachiwiri. Mai! Ine ndinali wamng’ono. Ndipo awa, onse awa, ang’ono! Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, kodi izi siziri zachirendo! Apa iwo ali.” Ndipo iwo anali onse akuthamanga. . .

³⁸³ Ndipo ine ndinawawona, akubwera, ndipo ine—ine ndinamuwona Hope akubwera. Iye anawoneka. . . Inu mukudziwa, iye anamwalira ali makumi awiri ndi ziwiri. Iye anali akadali wokongola monga anali kale. Ambiri a inu mukumukumbukira iye; maso akulu akuda awo. Iye anali wa Chijeremani. Tsitsi lake lakuda likugwera mmusi kumbuyo kwake. Ine ndinaganiza, “Tsopano, pamene iye ati afike apa, iye adzati—iye adzati, ‘Bill.’ Ine ndikudziwa adzatero. Ine ndikudziwa adzati, ‘Bill,’ pamene iye ati afike pano.”

³⁸⁴ Ine ndinali kuyang’ana. Ndipo mmodzi aliyense wa akazi awa akubwera ndi kumandikumbatira ine, kumati, “O, m’bale wofunika, ife tiri okondwa kwambiri kukuwonani inu!” Ine ndinaganiza. . . Mmodzi aliyense atavala chabe mofanana, koma iwo anali nalo tsitsi lawo losiyana, inu mukudziwa, tsitsi lofiira, ndi tsitsi lakuda, ndi tsitsi la bulondi. Ndipo—ndipo iwo anali kubwera, koma iwo onse anali aang’ono.

³⁸⁵ Ndipo pamene iye anafika kwa ine, ine ndinaganiza, “ine ndiwone chabe chimene iye ati anene.”

³⁸⁶ Ndipo iye anayang’ana mmwamba pa ine, ndipo iye anati, “O, m’bale wathu wofunika!” Iye anandikumbatira ine, ndipo iye anangopitirira. Akazi ena anabwera, anandikumbatira ine, chotsatira.

³⁸⁷ Ndipo ine ndinamva phokoso. Ndipo ndinayang'ana cha mbali *iyi*, ndipo apa pamabwera gulu la amuna, anyamata aang'ono, onse mu msinkhu wa pafupi makumi awiri. Iwo anali nalo tsitsi lakuda, ndi tsitsi la bulondi. Ndipo iwo onse anali atavala miinjiro yoyera, ndi osavala nsapato. Ndipo iwo anathamangira kwa ine ndi kuyamba kundikumbatira ine, akufuula, “M'bale wofunika!”

³⁸⁸ Ine ndinaganiza. Ndipo ine ndinachewuka mmbuyo, ndipo apo ine ndinali, ndikugonabe pamenepo. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, tsopano, ichi ndi chachirendo.”

³⁸⁹ Ndipo basi pomwepo Liwu linayamba kulankhula kwa ine. Ine sindinaliwone konse Liwulo. Ilo linati, “Iwe wasonkhanitsidwira, iwe—iwe wasonkhanitsidwira kwa anthu ako.” Ndiyeno munthu wina anandinyamulira ine pamwamba, kundikhazika ine pamwamba, pa chinthu chachitali chachikulu monga *chonchi*.

Ine ndinati, “Chifukwa chiyani iwe unachita izo?”

Anati, “Mu dziko lapansi iwe unali mtsogoleri.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine—ine sindikumvetsa izi.”

³⁹⁰ Ndipo Liwu limenelo likulankhula kwa ine. Ine sindimakhoza konse kuliwona Liwulo. Tsopano, Ilo linali chabe pamwamba panga, likulankhula kwa ine.

³⁹¹ Ine ndinati, “Chabwino, ngati ine—ngati ine ndapitirira, ine ndikufuna kumuwona Yesu.” Ine ndinati, “Ine...Iye anali choncho...Iye anali moyo wanga wonse. Ine ndikufuna kumuwona Iye.”

Ndipo kotero Iye anati, “Iwe siwungakhoze kumuwona Iye tsopano. Iye akadali pamwamba.”

³⁹² Mukuwona, apo panali mmusi mwa guwa, komabe, mukuwona, malo achisanu ndi chimodzi, kumene anthu amapita, mukuwona; osati achisanu ndi chiwiri, kumene kuli Mulungu, malo achisanu ndi chiwiri. Achisanu ndi chimodzi!

³⁹³ Ndipo iwo anali—ndipo iwo anali onse kumeneko, ndipo iwo anali kudutsapo. Ndipo ine ndinati...Zinkawoneka ngati panali makamaka mamilioni a iwo. Ine sindinawawonepo iwo...Ndipo, pamene ine ndinakhala pamenepo, akazi awa ndi amuna akuthamangabe pambali ndi kundikumbatira ine, kumanditcha ine “m'bale.” Ndipo ine ndinakhala pamenepo.

³⁹⁴ Ndiyeno Liwu ilo linati, “Iwe wasonkhanitsidwira kwa anthu ako, monga Yakobo anasonkhanitsidwira kwa anthu ake.”

Ine ndinati, “Onse awa, anthu anga? Kodi onse awa ndi Mabranham?”

Iye anati, “Ayi. Iwo ndi owatembenezira ako kwa Khristu.”

³⁹⁵ Ine ndinayang'ana pozungulira. Ndipo apo panali mkazi wokongola kwenikweni akuthamanga. Iye ankangowoneka

pafupi chomwecho. Iye anatambasulira mkono wake mondikumbatira ine, ndipo iye anati, “O, m’bale wanga wofunika!” Iye anayang’ana pa ine.

³⁹⁶ Ine ndinaganiza, “Mai! Iye ankawoneka ngati Mngelo.” Ndipo iye anadutsa.

Ndipo Liwu lija linati, “Kodi iwe sunamuzindikire iye?”

Ine ndinati, “Ayi, ine sindinamuzindikire.”

³⁹⁷ Anati, “Iwe unamulondolera iye kwa Khristu pamene iye anali atadutsa makumi asanu ndi anai.” Anati, “Iwe ukudziwa chifukwa chimene iye akuganizira mochulukwa za iwe?”

Ine ndinati, “Msungwana wokongola uyo anali atadutsa makumi asanu ndi anai?”

³⁹⁸ “Eya.” Anati, “Iye sangakhoze kusinthanso tsopano.” Anati, “Ndicho chifukwa chake iye akuti, ‘M’bale wofunika.’”

³⁹⁹ Ine ndinaganiza, “O, mai! Ndipo ine ndimachita mantha ndi izi? Bwanji, anthu awa ndi enieni.” Iwo, iwo sanali kupita kulikonse. Iwo sanali kutopa, kukhala Kumeneko.

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, chifukwa chiyani ine sindingathe kumuwona Yesu?”

⁴⁰⁰ Anati, “Chabwino, tsopano, Iye adza—Iye adzabwera tsiku lina. Ndipo Iye adzabwera kwa iwe, poyamba, ndiyeno iwe udzaweruzidwa.” Anati, “Anthu awa ndi owatembenuza ako amene iwe wawatsogolera.”

⁴⁰¹ Ndipo ine ndinati, “Iwe ukutanthawuza, pokhala mtsogoleri, kuti ine . . . kuti Iye adzandiweruza ine?”

Anati, “Inde.”

⁴⁰² Ndipo ine ndinati, “Kodi mtsogoleri aliyense adzasowa kudzaweruzidwa monga choncho?”

Anati, “Inde.”

Ine ndinati, “Nanga bwanji Paulo?”

Iye anati, “Iye adzayenera kudzaweruzidwa ndi ake.”

⁴⁰³ “Chabwino,” ine ndinati, “ngati gulu lake liti likalowe, koteronso langa, chifukwa ine ndalalikira chimodzimidzi Mawu omwewo.” Ndi zimenezotu. Ine ndinati, “Pamene iye anabatiza mu Dzina la Yesu, ine ndinatero, inenso. Ine ndinalalikira . . .”

⁴⁰⁴ Ndipo mamilioni anafuwula, onse pamodzi, anati, “Ife tikupumula pa Chimenecho!”

⁴⁰⁵ Ndipo ine ndinaganiza, “Mai! Ngati ine ndikanadziwa kokha izi ndisanabwere kuno, ine ndikanawapanga anthu kuti abwere kuno. Iwo sangakhoze kukwanitsa kuphonya ichi. Chifukwa, tayang’anani apa!” Ndiyeno . . .

⁴⁰⁶ Ndipo Iye anati, “Tsopano, tsiku lina Iye adzabwera, ndiyeno . . . Tsopano, mkati muno, ife sitimadya konse, kumwa, kapena kugona. Ife tiri chabe tonse amodzi.”

407 Chabwino, icho sichiri changwiwo; icho chiri choposa ungwiro. Icho sichiri upamwamba; icho chiri choposa upamwamba. Palibe dzina lingakhoze. . . Inu simungakhoze kuganiza. . . Mulibe mawu mu chilankhulo kuti anene icho. Inu mwafika basi, ndizo zonse.

408 Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, ichi, ichi chikanakhala changwiwo. Ndiyeno ife tichita chiyani kenako?”

409 Anati, “Ndiye, pamene Yesu abwera, ndipo ife tiri. . . ndipo Iye akuweruza iwe, kapena chifukwa cha utumiki wako, ndiye ife tibwerera pa dziko lapansi ndi kukatenga matupi.” Chabwino, ine—ine sindinaganize nkome za izo ndiye. Ndizo chimodzimodzi Lembu. Anati, “Ndiye ife tibwerera ku dziko lapansi kuti tikatenge matupi, ndiye ife tidya. Iye sitikudya kuno, ngakhalenso kuti ife sitimagona.” Anati, “Ife timadya pansu uko, koma ife tibwerera kudziko lapansi.”

410 Ine ndinaganiza, “Mai, kodi ichi sichiri chodabwitsa! O, mai! Ndipo ine ndinkachita mantha za icho. Chifukwa chiyani ine ndinkachita mantha za kumwalira, kuti ndibwere ku ichi? Chabwino, ichi chiri ungwiro, kuwonjezera ungwiro, kuwonjezera ungwiro. O, ichi ndi chodabwitsa!”

411 Mukuwona, ife tinali kumene pansu pa guwa. Mwawona? Icho chinali chimenecho, mukuwona, pansu kumene pa guwa, kuyembekezera Kudza, mwawona, kuti Iye apite kukatenga iwo amene anali kugona mu. . . m—matupi omwe akugona mu fumbi, kuti akatidzutsa ife kachiwiri; kubwera, kutidzutsa ife.

412 Monga Yesu anabwera kupyola mu paradiso, ndipo anamudzutsa Abrahamu, Isaki ndi onse awo, inu mukudziwa, amene anali kuyembekezera chiwukitsiro choyamba. Iwo analowa mu mzinda ndipo anawonekera kwa ambiri.

413 Izo ziri Mwamalemba mwangwiwo. Masomphenya anali chimenecho, kapena chirichonse chimene iwo anali, iwo anali Mwamalemba mwangwiwo.

414 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, kodi siziri izi zodabwitsa!” Ndiyeno ine ndinaganiza, “Siziri izo zodabwi- . . . ?”

415 Ine ndinamva chinachake chikulira, monga kavalo. Ndipo ine ndinayang’ana. Ndipo kavalo wanga wokwerapo wamng’ono amene ndinkakonda kumukwera, Prince wamng’ono, ine ndinkaganiza zochuluka kwambiri za iye. Apa iye anali, atayima pamenepo pambali pa ine, ndi kuyika mutu wake cha paphewa langa, kuti andikumbatire ine. Monga ine ndinkakondera kumupatsa iye shuga, inu mukudziwa, ndipo iye anayika lake. . . Ine ndinayika mkono wanga pa iye. Ine ndinati, “Prince, ine ndinkadziwa kuti iwe udzakhala kuno.”

Ine ndinamverera chinachake chikunyambita dzanja langa. Apo panali galu wanga wakale wosaka mbira.

416 Pamene—pamene Bambo Short, kumusi uko, anamupatsa iye chiphe, ine ndinalumbira kuti ndidzawapha Bambo Short chifukwa cha icho. Ine ndinali pafupi zaka khumi ndi zisanu ndi chimodzi zakubadwa. Iwo anamuthirira iye chiphe, ndi kumupatsa iye chakudya cha galu. Ndipo abambo anga anandigwira ine ndiri ndi mfuti, ndikupita kumusi kukawawombera iwo, komweko ku polisi sitieshoni. Ndipo ine ndinati, “Ine ndiwapha iwo.” Ine ndinati, “Chabwino. . .” Ine ndinapita kumanda a galuyo. Ndipo ine ndinamuwuzwa iye, ine ndinati, “Fritz, iwe wakhala monga bwanawe kwa ine. Iwe wandiveka ine ndi kunditumiza ine ku sukulu. Pamene iwe unakalamba, ine ndinali woti ndikusamalire iwe. Tsopano iwo akupha iwe.” Ine ndinati, “Ine ndikukulonjeza iwe, Fritz, kuti iye sakhala moyo.” Ine ndinati, “ine ndikukulonjeza iwe, kuti iye sakhala moyo. Ine ndidzamupeza iye pa msewu nthawiya, akuyenda, ndiye ine ndidzamugunda iye, mukuwona.” Ndipo ine ndinati, “ine ndidzamupeza iye chifukwa cha iwe.”

417 Koma inu mukudziwa chiyani? Ine ndinamulondolera bamboyo kwa Khristu, kumubatiza iye mu Dzina la Yesu, ndi kumuyika iye pa imfa yake. Inde, bwana. Ine ndinatembenuka pafupi zaka ziwiri zitachitika izo. Ine ndinawona zinthu mosiyana ndiye, mwawona. Ine ndinamukonda iye mmalo mwakumuda iye.

418 Kotero ndiye, koma, komabe, apo panali Fritz akuyimirira pamenepo, akundinyambita ine pa dzanja. Ndipo ine ndinali. . . Ine ndinapenya.

419 Ine sindikanakhoza kulira. Palibe amene akanakhoza kulira. Chinali chonse chisangalalo. Iwe sukanakhoza kukhala wachisoni, chifukwa chinali chonse chisangalalo. Iwe sukanakhoza kufa, chifukwa unali wonse Moyo. Mukuwona? Mukuwona? Sukanakhoza kukalamba, chifukwa unali wonse umwana. Ndipo ndicho chimene. . . Iwo uli chabe ungwiro. Ine ndinaganiza, “O, kodi siziri izi zodabwitsa!” Ndipo mamilioni. . . O, mai! Ine ndinali kumene kwathu, mwawona.

420 Ndipo—ndipo nthawi yomweyo ine ndinamva Liwu. Ndipo Ilo linafuwula mokweza, linati, “Zonse zomwe iwe unazikondapo. . .” mphotho ya ntchito yanga. Ine sindikusowa mphotho. Iye anati, “Zonse zomwe iwe unazikondapo, ndi zonse zomwe zinakondapo iwe, Mulungu wazipereka kwa iwe.”

Ine ndinati, “Ambuye alemekezeke!”

421 Ine ndinamverera mwachirendo. Ine ndinaganiza, “Chavuta nchiyani? Ine ndikumverera mwachirendo.” Ine ndinatembenukanso ndi kupenya. Ndipo pa bedi, thupi langa linali kusuntha. Ine ndinati, “O, ine sindikusowa kuti ndibwerere, ndithudi. Musati, musati mudirole ine ndipite.”

422 Koma Uthenga unayenera kulalikidwa. Mu mphindi chabe, ine ndinali pa bedi kachiwiri, mwawona, monga choncho.

423 Mosaposa pafupi miyezi iwiri yapitayo, pamene... Inu munamva icho chikuwerengedwa icho mu—mu *Voice* ya Anthu Amalonda. Icho chinapita paliponse mdziko, mwawona. Ndipo M'bale Norman, muno apa, ine ndikuyembekeza iye ali muno penapake usiku uno. Iye anamasulira kuchokera apo, ndi kutumiza icho mu timabukhu. Icho chapita kulikonse. Ndipo atumiki analemba kuno, ambiri a iwo, ndipo anati . . .

424 Mmodzi apa, ine ndingokuwuzani chimodzi chimene ichi. Pali mazana a izo, zedi. Mmodzi uyu anathamanga, nati, "M'bale Branham, masomphenya anu mu *Voice* ya Anthu Amalonda . . ."

425 Ndipo ine ndikumuyamikira Tommy Nickels, ngakhale iye sali nawonso Anthu Amalonda, konse. Ine sindikudziwa chifukwa, koma iye sali. Koma iye analemba izo mmenemo molondola kumene, pamene ine ndinanena. Momwemo mu magazini yautatu iyo, iye anati, "Pamene ine . . . Pamene Paulo anabatiza mu Dzina la Yesu, ndi kuwalamulira anthu achite momwemo, ine ndachita momwemo." Mukuwona, iye anayika izo basi momwe izo zinaliri. Mukuwona? Ndipo kotero ndiye ine—ine—ine ndinaganiza, "Mai!"

426 Mtumiki uyu analemba kuno, anati, "M'bale Branham, masomphenya anu . . ."

427 Amene, akanakhoza kukhala masomphenya. Anati... Tsopano, ine sindikufuna kunena, "kusinthidwa." Ngati Paulo . . . Ngati ine ndinawatulidwira kulowa mmwamba moyamba umu ndi kuwona chimenecho, nanga bwanji Paulo amene anakwatulidwa kupyola mpaka mmwamba mwachitatu? Chinali chiyani icho? Iye anati sankakhoza ngakhale kulankhula za icho, mwawona, ngati iye anakwatulidwa. Ngati uko kunali kukwatulidwa, ine sindikudziwa. Ine sindinganene. Ine sindingakhoze kukuwuzani inu.

428 Koma mtumiki uyu anati, "M'bale Branham, masomphenya anu akumveka Mwamalemba kwambiri ndipo ali olondola mpaka inu munalankhula za kavalo kukhala ali kumeneko." Anati, "Kavalo Kumwamba?" Anati . . . Tsopano onani munthu wachipembedzo iyo, nzeru, lingaliro? Mukuwona? Iye anati, "Kumwamba kunapangidwira anthu, osati akavalo."

429 Chabwino, ine ndinakhala pansu. Billy, mwana wanga apa, anayiyika kalatayo kuno mu ofesi yakale ya mpingo, pafupi miyezi itatu kapena inai yapitayo.

430 Ine ndinati, "M'bale wanga wokoma, ine ndiri wodabwitsidwa pa nzeru zanu, koma, ndi kudziwa kwanu kwa Lemba. Ine sindinanene kuti ine ndinali Kumwamba. Ine ndinati anali mu malo wonga paradiso, chifukwa Khristu anali akadali pamwamba, mukuwona. Koma," ine ndinati, "ngati izo zingakukhutseni inu, inu mutsegule ku Chivumbulutso 19. Ndipo pamene Yesu akubwera kuchokera mmiyamba ya Kumwamba, Iye akubwera pa kavalo woyera, ndipo oyera onse

ndi Iye akukwera pa akavalo.” Kulondola. Mwamtheradi. Inde, indedi.

431 Ndipo pamwamba mu Malo womwewo, apo panali chimodzi chinkawoneka monga mphungu, ndipo chimodzi chinkawoneka monga ng’ombe, ndipo chimodzi . . . Chabwino, mai, ali kuti akavalo awo amene anabwera kudzamutenga Eliya? Chikungokupita kuti chikuwonetseni, inu mukuwona, malingaliro amunthu akungofuna chinachake choti atsutsepo. Uko nkulondola.

432 Tsopano zindikirani. Koma ine ndimangoganizira, pamene m’bale wokoma uyu, waumulungu, Yohane . . . Ine ndinangoganiza awo angakhale malo abwino kubayiramo icho, chabe ndisanatseke, mukuwona. Ngati Yohane anayang’ana cha Kumeneko, ndipo awo anali a abale ake, mukuwona, abale ake amene anali woti akazunzike pang’ono; ndiye, onani, Ambuye Mulungu anandirola ine kuti ndiwawone abale anga ndi oyera amene anali kuyembekezera Kudza kwa Ambuye. Zindikirani, iwo sanali pansi pa guwa la nsembe; anga sanali. Koma, awa anali, iwo anali ofera. Mukuwona? Anga sanali pansi pa guwa la ofera.

433 Tsopano ine ndikufuna inu mumvetse mwatcheru kwenikweni. Ndipo ine nditseka, mowona mtima, basi pafupi mu maminiti khumi, pa teni koloko, ngati ndingangodula ndi kutsiriza izo mawa.

434 Penyani. Iwo, iwo sanali anga . . . awo omwe Ambuye anandiwonetsa ine, Mkwatibwi, Iye sanali pansi pa chipika cha ofera, ayi, guwa la nsembe la ofera; koma anali atalandira miinjiro yoyera, pakuvomereza chisomo chokhululukira cha Mawu amoyo. Khristu anali atawapatsa iwo mwinjiro woyera. Ine sindikuganiza, mwa kutsegula . . .

435 Kapena, ine ndikuganiza, kani, mwa kutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu, monga ine ndikukhulupirira, kuti Icho chatsegulidwa kwa ife. Ine ndinachita izo ndi chikumbumtima chabwino, ndi vumbulutso lomveka pamaso pa Mulungu. Osati kuyesera kungochipangitsa icho, kuganiza, chifukwa chakuti ine nthawizonse ndinali wotsutsa bungwe, sindidzakhala wa iwo. Koma Icho chatsegulidwa kwa ine tsopano.

436 Ndipo ine ndikuganiza chinthu china. Mwa kutsegulidwa kwa Chisindikizo Chachisanu ichi, mu tsiku ili, chikuwongola chiphunzitso pomwe apa, chimene ine ndikhoza kuchilankhula, cha kugona kwa moyo. Tsopano, ine ndikuzindikira kuti muli anthu muno amene amakhulupirira zimenezo, mukuwona, mu kugona kwa moyo. Ine ndikuganiza kuti Ichi chikutsutsa izo. Iwo sakugona. Iwo ali amoyo. Matupi awo, akugona. Koma, moyo, osati mmanda, iwo ali mu Kukhalapo kwa Mulungu, mwawona, pansi pa guwa.

437 Apa pali pamene ine ndimasiyana naye m'bale wanga wokoma, mphunzitsi. Ndipo, ine ndikuzindikira, ine ndikudziwa ine ndikuwona ena a anthu ake akhala apa. Yemwe, ine ndikuzindikira kuti uyu ali mphunzitsi wamphamvu. Iye ndi dokotala, ndipo Dokotala Wauzimu, ndi Ph., LL.D.. Ndipo iye ali—iye ali munthu wabwino kwenikweni, nayenso. Ine ndikuganiza iye anatsogola, pa nthawi yino. Koma iye anali munthu wabwino, ndi wolemba wabwino. Ndipo ali M'bale Uriah Smith, mlembi wa *Danieli ndi Mavumbulutso*. Tsopano, kwa inu anthu amene muli otsatira a zophunzitsa zake, onani, tsopano ine sindikuti. . . ine sindiri chabe. . . sindikufuna kunena izi mwamwano, koma ine basi. . . Mukuwona?

438 Koma, M'bale Smith, ndipo poyesa kuthandizira, onani, ndi kuyesera kuthandizira kugona kwa moyo, pamenepo iye akutchula kuti, “Moyo umagona. Ndipo kulibe guwa la nsembe Kumwamba. Kutu, guwa lokhalo limene likulankhulidwa,” lomwe iye—iye amalikhulupirira kuti liri Kumwamba, “liri guwa la lubano.” Koma kwa inu anthu okonedwa. . . Ndipo osati kutsutsana naye m'bale wanga. Ine mwina ndidza. . . ndikuyembekeza kudzakumana naye iye mbali yinayo, mukuwona. Osati kutsutsana naye mphunzitsi wopambana uyo.

439 Koma kungofuna kukuwonetsani inu momwe Ichi chikutsutsira izo, mwawona. Ichi chikutsutsa izo. Kutsegula kwa Chisindikizo ichi, mu tsiku lotsiriza lino, chikungotenga kugona kwa moyo kukuchotsa mnjira. Mukuwona? Iwo ali amoyo. Iwo sali akufa. Mwawona? Zindikirani.

440 Zindikirani ichi tsopano. Tsopano, ngati uko kulibe guwa la nsembe Kumwamba, ndiye nsembe ya tchimo ikugona pati, Mwanawankhosa? Payenera kukhala malo amene Mwanawankhosa wophedwayo, wamagazi, ali kugona kumeneko, kumene Magazi. . . iwo.

441 Tsopano, lubano anali mafungo, chinthu chonunkhira chimene iwo ankawotcha, chimene Baibulo linati anali “mapemphero a oyera.” Ngati palibe nsembe pa guwa, ndiye mapemphero sangalandiridwe. Ndi kokha mwa Magazi, pa guwa lansembe, amene amalola mapemphero kufika kwa Mulungu.

442 M'bale Smith anali kulakwitsa, mwawona. Osati kutsutsana naye iye; ine ndikuganiza ndadzipanga ndekha kumveka, ndi chikondi cha pa abale ndi malemekezo chifukwa cha ntchito yake yayikulu, mwawona. Koma iye anali kulakwitsa.

443 Chisindikizo Chachisanu chatsegula izo, mukuwona, mukuwona; zinthu zina zambiri, ngati inu mwamvetsa izo. Mukuwona? Ine ndikuyembekezera mafunso anga, mwawona, ngati ine. . . Chabwino.

444 Tsopano, linali kuti likasa; Mwanawankhosa, wophedwa, wovulazidwa, wowukha magazi, wamagazi wa chitetezero, kwa mapemphero afungo lokoma awa?

445 Zindikirani, Baibulo likuti, “Ngati kachisi wa dziko lapansi uyu wa mokhala mwathu akhala atawonongedwa, ife tiri naye mmodzi akuyembekezera kale.” Ndiko kumene ine ndinawawona oyera awo. Mukuwona?

446 Yang’anani pamene mwana...Mundikhululukire ine kachiwiri, alongo, chifukwa cha kulankhula komveka uku pamaso pa akazi ang’ono. Koma, penyani. Pamene mayi ali ndi pakati, ndipo gulu laling’ono la akatumba ilo liri kuzipota ndi kulumpha, inu mukumvetsa, ilo ndi thupi lachibadwa. Ndipo monga momwe chirengedwe chikuchita thupi lachibadwa . . .

447 Kodi inu munayambapo mwawazindikira akazi anu ana asanabadwe? Iwo nthawizonse, popitirira kumene, pamapeto, amakhala wachifundo kwenikweni, wokoma. Ngati iye sanakhalepo, moyo wake wonse, iye adzakhala pamenepo. Kodi inu munayamba mwazindikirapo chiyero chake, kapena kukhala ngati kumverera, komwe inu mumawazindikira amayi?

448 Ndipo inu mumawona wochimwa wina kunjako, akumuchita chipongwe mayi yemwe m—mayi woyembekezera. Ine ndikuganiza ndicho chipongwe. Ndiwo moyo ukubwera ku dziko.

449 Koma kodi inu munazindikira, pozungulira mayi ameneyo pamawoneka kukhala kumverera kokoma? Nchiyani icho? Ilo ndi thupi lalingono lauzimu, moyo wauzimu, ukuyembekezera kuti ulowe mu thupi laling’ono ilo mofulumira pamene ilo liti libadwe. Tsopano ilo chabe ali ndi pakati pake; koma, pamene ilo labadwa, ilo labadwa. Thupi lauzimu likulumikizana nalo thupi la chibadwa.

450 Ndipo, ndiye, Baibulo limaphunzitsa kuti ife tiri tsopano mu pakati pa Mulungu. Ife tiri mu pakati pa Mzimu Woyera, kuti, mwa ife muli Khristu, mwana wa Mulungu akuwumbidwa mwa ife. Ndipo pamene thupi la dziko lapansi ili likhala litawonongedwa, thupi lauzimu ili likubwera kuchokera mmimba za dziko lapansi, pamenepo pali thupi lina likuyembekezera kulilandira ilo. “Ngati kachisi wa dziko lapansi uyu wagwetsedwa, pali thupi lina kuti tililandire ilo.” Thupi lachivundi ili likuvala chisavundi. Thupi la lapansi ili likuvala lakumwamba. Izi, mukuwona chomwe ine ndikutanthawuza? Pali thupi lachibadwa lomwe liri lamachimo; koma, mu mapangidwe ake, monga ngati ilo, liri thupi lina limene ife timapitako.

451 Ndipo ine ndiri woyamika kwa Mulungu kuti ine ndikhoza kunena, monga m’busa wanu ndi m’bale, ine ndawawona anthu amenewo, kotero ndithandizeni ine, mu thupi limenelo, ndipo ndinawagwira iwo ndi manja anga. Uko nkulondola. Zindikirani.

452 Penyani. Yang’anani pa Mose, Elisha. Mose anali atamwalira, ndipo Elisha anali atatengedwera kumka

Kumwamba, iye anayimirira apa pa Phiri la Chiwalitsiro ndi mphamvu zake za kulankhula, kumva, kumvetisa, ndipo analankhula kwa Yesu asanapachikidwe. Tsopano, ndi thupi lamtundu wanji limene iye anali nalo?

⁴⁵³ Yang'anani pa Samueli, atamwalira kwa pafupi zaka ziwiri. Anayitanidwanso mu—mphanga usiku umenewo, ndi mfiti yaikazi ya ku Endori, ndipo analankhula kwa Saulo ndi chilankhulo; anamumva Saulo, analankhula moyankha, ndipo anadziwiratu zinthu zomwe zinali zoti zidzachitike. Apabe, mzimu wake unali usanasinthe. Iye anali mneneri.

⁴⁵⁴ Pamene mzimu wa Eliya ubwerera pa munthu, iwo udzamalondolera iye basi ngati Eliya. Iye adzapita ku chipululu. Iye adzakonda chipululu. Iye adzakhala wodana nawo akazi amakhaliidwe oyipa. Iye adzakhala wotsutsa bungwe. Iye sadzanyengerera aliyense. Ndipo umenewo uli basi. . . Ndiwo, umenewo udzakhala mzimu wake. Iwo unali, nthawi iliyonse iwo unabwera, mukuwona.

Mose adzakhala munthu yemweyo.

Tsopano, ndipo ife tikupeza, mu Chivumbulutso 22:8, chinthu chomwecho.

⁴⁵⁵ Tsopano, kapena kuti tikhazikitse izo, chifukwa cha iwo amene. . . Miyoyo iyo (tsopano yang'anani ichi) pansu pa guwa, pa kumatula kwa Chisindikizo ichi, amene anali ataphedwa mu nthawi ya pakati pa imfa ya Khristu ndi kukwera kumwamba kwa Mpingo; gulu la Eichmann, ndi onse awo, Ayuda owona awo ali ndi maina awo pa Bukhu. Ngati inu muti muyang'ane, m'bale wanga, malingana ndi Lemba, iwo amakhoza kulankhula, kufuula, kulankhula, kumva, ndipo anali nazo mphamvu zonse zisanu. Osati kugona mmanda, atakomoka. Iwo anali maso kwambiri kumene, ndipo amakhoza kulankhula, kulankhula, kumva, china chirichonse. Nkulondola uko? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] O, tithandizeni ife!

⁴⁵⁶ Maminiti awiri. Ameni. Ine ndinali wo pepesa ine ndakusungani inu theka la ora. Ayi, ine sindingakhoze, ine sindikuyenera kunena izo, mwawona. Mukuwona? Uko nkulondola, mwawona.

⁴⁵⁷ Koma, yang'anani, apa pali mwa kupambana kwa kumvetisa kwanga, mwa kupambana. Ndipo malingana ndi vumbulutso limene linaperekedwa kwa ine mmawa uno chabe kusanawale, ndi Ambuye Yesu Khristu, apo pali Chisindikizo Chachisanu chotsegulidwa, kuti chipite ndi zina zinai. Mwa chisomo Chake, Iye anandipatsa ine icho, chisomo Chake kwa inu ndi ine. Ife tikumuthokoza Iye chifukwa cha Icho. Ndipo, ndi thandizo Lake, ine ndikulinga kukhala moyo moyandikirirapo. . . monga ine ndingakhalire moyo, kuwaphunzitsa ena kuchita chinthu chomwecho, mpaka ine nditakumana naye Iye, ndi inu, mu Ulemerero, pamene zinthu zonse zitatha. Ine ndikumukonda Iye

chifukwa cha izi, ndipo ndicho mwakupambana kwa kudziwa kwanga kwa Icho.

⁴⁵⁸ Ndipo ine mowona ndikukhulupirira, ndi mtima wanga wonse, kuti mavumbulutso owona a kuwulula kwa Chisindikizo, Choyamba, Chachiwiri, Chachitatu, Chachinai, ndi Chachisanu, ali tsopano otseguka kwa ife.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda

[M'bale Branham mwakachechete akulankhula ndi winawake—Mkonzi.]

Pa mtengo wa Kalvare.

[M'bale Branham akuyamba kung'ung'uza *Ndimkonda Iye*—Mkonzi.]

⁴⁵⁹ Tsopano, mwakachetechete, mwaulemu, pamaso pa Mulungu! Pamene ife tawona Chisindikizo ichi chikutsegulidwa kwa ife, Mulungu poti atenge ana Ake Omwe okonedwa ndi kuwachititsa khungu maso awo, ndi kuwatumiza iwo, chifukwa chilungamo Chake Chomwe—chilungamo chimafuna chiweruzo cha tchimo. Ganizani za icho. Chilungamo Chake, ndi chiyero Chake zimafuna chilungamo. Lamulo lopanda chilango siliri lamulo. Ndipo malamulo Ake Omwe, Iyemwini, Iye sangakhoze kulinyoza ndi kukhalabe Mulungu.

⁴⁶⁰ Ndicho chifukwa chake Mulungu anachita kukhala munthu. Iye sakanakhoza kutenga choloweza mmalo, mwana wamwamuna yemwe sanali...mwana wamwamuna wamba chabe kwa Iye, kapena chinachake. Mulungu anadzakhala zonse, Yesu anadzakhala zonse Mwana ndi Mulungu, njira yokhayo Iye akadachitira icho mwachilungamo. Mulungu anayenera kudzitengera chirango, Iyemwini. Icho sichikanadzakhala chilungamo, kuchiyika icho pa winawake, munthu wina. Koteru, Munthu wa Yesu anali Mulungu, kuwonetsedwa mu thupi, lotchedwa Emanuele.

⁴⁶¹ Ndipo kuti achite izo, ndi kuti atenge Mkwatibwi, ndi kuti apulumutse gulu losapembedza la Amitundu, Iye anayenera kuwachititsa khungu ana Ake Omwe. Ndiyona nkuwalanga iwo chifukwa cha icho, mu thupi, chifukwa chokana. Koma chisomo Chake chinapereka miinjiro. Koma, Moyo, onani chimene chinachitika.

⁴⁶² Ndipo ngati Iye anachita kuchita izo, polinga kuti ife tipeze mwayi, ife tingawukane bwanji mwayi umenewo mu chikondi? Ngati alipo mu nyumba yino, usiku uno, munthu ameneyo, wamng'ono kapena wamkulu, amene kufikira nthawi yino wakana mwayi umenewo umene unamutengera Mulungu mtengo woterowo, ndipo inu mukufuna kuti mulandire kupereka kwa Mulungu uko, usiku uno; mwakuti inu simukusowa kuchita, monga mmene ife tikudziwira konse, kuti ukhale

wofera, ngakhale inu mungakhale. Koma mwinjiro woyera waperekedwa kwa inu. Ndipo ngati Mulungu akugogonda pa mtima wanu tsopano, bwanji osachilandira icho! [M'bale Branham anagogoda pa guwa katatu—Mkonzi.]

Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu kachiwiri.

463 Ngati munthu ameneyo, kapena anthu, ali mkati muno, amene akukhumba icho, kapena akufuna kulandira icho pa maziko a chikhulupiro chanu mu Mwazi wokhetsedwa umene Mulungu anachita kukukhetserani inu, anazunzika kupitirira chirichonse chimene wachivundi wina anatero. Apo sipakadakhala munthu wachivundi kuvutika monga choncho. Mpaka, chisoni Chake Chomwe chinalekanitsa madzi Ake kuchoka ku Magazi Ake, mu mitsempha Yake. Iye asanapite ku Kalvare, madontho a Magazi anali kubwera kuchokera mthupi Lake, ndi chisoni choterocho ndi mtima wosweka kwa chimene Iye ankayenera kuchichita. Koma, akanakhoza kuchikana icho, nayenso. Koma, mololera anachita icho chifukwa cha inu ndi ine. Kodi inu mungakane chikondi chosati nkuchifanizitsacho?

464 Ndipo inu mukuchiwona icho tsopano, pa kutseguka kwa Zisindikizo izi; kuti chimene inu mwachita, ndi chimene Mulungu wakuchitirani inu. Ndipo inu muli okonzeka kupereka moyo wanu kwa Mulungu, ndipo ngati Iye adzakukwatuleni inu kuchokera mmanja a wotsutsakhristu mmene inu muli tsopano? Kodi inu mungalandire kupereka Kwake, pa kungokweza dzanja lanu kwa Iye, kunena, “Mulungu, pa kutere, ine ndikuzindikiritsa. Ine ndikuvomereza kupereka uko kwa chisomo.”

465 “Ndipo, M'bale Branham, ine ndikukhumba mapemphero anu, kuti ine ndikhalebe wokhulupirika.”

466 Kwezani dzanja lanu, ndipo ine ndipemphera. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mutanthawuze icho tsopano. Musati—musati muchite icho pokha inu mukutanthawuza icho. Ndipo pomwepo pamene inu mwakhala, muvomereze icho pomwepo. Chifukwa, kumbukirani, inu simukanakhoza kukweza dzanja lanu pokha Chinachake chitakuwuzani inu kuti muchite icho. Ndipo palibe kanthu kalihone kakanakhoza kuchita icho koma Mulungu.

467 Kotero, tsopano, pamene inu mukuwona Malemba akufutukulidwa mwangwiro chotero! Inu mukuwona chimene chakhala chikuchitika, mmusi kupyola mu mibadwo, zaka pang'ono zotsiriza, zaka makumi awiri kapena makumi atatu. Inu mwaliwona izo zikutsimikiziridwa mwangwiro. Inu mwaliwona Lemba likunena chimodzimodzi chimene chachitika, ndi chimene chikukonzekera kuchitika. Ndiye, pa maziko a chikhulupiro mu ntchito ya Khristu, pamene inu mukukhala pakali pano, ndipo mwakweza manja anu, nenani, “Kuchokera pa miniti yino, icho chakhazikika. Ine

ndikutenga Khristu tsopano kukhala Mpulumutsi wanga. Ndipo ine ndidzakhallira moyo Iye, moyo wanga wonse. Ndipo ine ndikukhumba Mulungu andidzaze ine ndi Mzimu Woyera.” Ndipo ngati inu simunabatizidwepo mu Dzina la Yesu Khristu, dziwe lidzakhala likuyembekezera inu.

Tiyeni ife tipemphere.

⁴⁶⁸ Ambuye Mulungu, panali chiwerengero chachikulu cha manja pakati pa anthu, omwe anakwezedwa. Ine ndiri wotsimikiza kuti Inu muli Ambuye Yesu yemweyo amene anapanga chitetezero kwa ife, zaka zambiri zapitazo. Ndipo powona Zisindikizo izo zikuwululidwa, ndi zinthu zazikulu zimene zachitika pomwe apa mu zaka pang’ono zotsiriza, ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti khomo la chifundo likuyamba kutsekeka, ndipo Inu muli wokonzeka kutenga ulendo Wanu tsopano kudzawombola anthu Anu. Pamene pakadali malo, ndi khomo lotseguka, monga zinaliri mu masiku a Nowa, mulole miyoyo yokoma iyi yomwe ikukhala mu thupi la kachisi uyu limene liti lidzasungunuke tsiku lina, yomwe inakweza dzanja lachivundi lija, mkati mwa iwo; chifukwa cha kwawo—kukhudzidwa kwawo ndi chodzinenera chawo, kuti iwo akukhulupirira ndipo akufuna kuvomereza kufunsira Kwanu kwa iwo, kwa chipulumutso, pa Bukhu losindikizidwa-lotseguka ili limene latsegulidwa kwa ife. Perekani kwa iwo, usiku uno, Ambuye, mwinjiro wa chilungamo cha Yesu Khristu, ndi kuveka moyo wawo mmenemo, kuti akakhoze kuyima pamaso pa Inu mu Tsiku limenelo limene layandikira, angwiwo, mwa Magazi a Khristu.

⁴⁶⁹ Ambuye Mulungu, ngati iwo sanabatizidwepo mu Dzina la Yesu Khristu! Ndi pa vumbulutso limene Inu mwandipatsa ine lokhudza icho; ndipo powona kuti Paulo anawalamulira anthu amene ngakhale anali atabatizidwa ndi Yohane Mbatizi, kuti abatizidwenso kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu, kuti alandire Mzimu Woyera, mu Machitidwe 19. Ine ndikupempha kuti Inu mudzawatsimikizire iwo, Ambuye, za Chowonadi, ndipo iwo atakumverani Inu.

⁴⁷⁰ Ndiyeno mu mukumvera kwa kulandira kwawo, ndi kumvera ku kuvomereza kwawo, ndi ku madzi; mulole Inu, pobwezera, muwadzaze iwo ndi Mzimu Woyera, ku mphamvu ya utumiki, moyo wawo wonse. Ine ndikuwapereka iwo tsopano kwa Inu, mu Dzina la Mwanawankhosa wa Mulungu woperekedwa nsembe, Yesu Khristu. Ameni. Ameni.

Ndimkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

⁴⁷¹ Tsopano, kwa inu amene munakweza manja anu. Mverani kulamulira kwa Mzimu, kumene kuti kutsatire—kuperekedwa

kwa Mawu, kwa wochimwa wolapa. Kutsateni iko, mu kuchita kulikonse. Ndipo Mulungu wa Kumwamba akupatseni inu mphotho chifukwa cha kuyima kwanu kwa Iye. Ambuye akudalitseni inu.

⁴⁷² Mawa usiku, bweretsani mapensulo anu ndi mapepala, tsopano, monga momwe inu mwakhala muli. Ife tikuyembekeza kudzakhala pano nthawi yomweyo, pa hafu pasiti seveni, ndendende, Ambuye akalola. Ndipo mwa . . . mundipempherere ine, kuti Mulungu adzatsegule Chisindikizo Chachisanu ndi chimodzi kwa ine, mawa, kuti ine ndidzakhoze kuchibweretsa Icho kwa inu pamene Iye apereka Icho kwa ine. Mpaka apo, ife tiyimbe kachiwiri. Osati kokha kupyolera mu nyimbo, koma kupyolera mu mayamiko kwa Iye amene anafa mmalo mwathu ndipo anatiwombola ife. *Ndimkonda Iye*. “Ndi . . .”

Apa pali m’busa wanu tsopano.

. . . mkonda Iye, ndimkonda Iye
Poti Iye anayamba kundikonda.



CHIVUMBULUTSO CHA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©1994 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org